

NDONDOMEKO

ZA

KHOLOLA LA UZIMU

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a Harvest International Institute ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Nthcito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	3
Mau Oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	5

GAWO LOYAMBA: KUCHENUTSA MASOMPENYA

1. Kupeza Masomphenya Anu.....	6
2. Masomphenya.....	17
3. Maso Ake Ali Pa Mayiko Onse.....	26

GAWO LACHIWIRI

4. Kumvetsetsa Cholinga Cha Kuseli Kwa Masomphenya.....	31
---	----

GAWO LACHITATU: KUPEZA ZOLINGA

5. Minda Yopanda Kanthu Ndi Zikwakwa Zosathwa.....	38
6. Ndomoko Za Kholora Lauzimu – Mbali Yoyamba.....	53
7. Ndomoko Za Kholora Lauzimu – Mbali Yachiwiri.....	64
8. Kututa Mwa Bvumbulutso.....	73

GAWO LACHINAYI

9. Kumphwanya Goli.....	89
10. Kudalitsa Mafuko.....	98
11. Kukwaniritsidwa Kwa Masomphenya.....	109
Mayanko Amafunso odziyesa nokha.....	116

KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogololera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Nchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphonzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphonzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphonzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

MUTU: Kuchenutsa Masomphenya

PHUNZIRO: Ndongomeko za Kholora la Uzimu

MAU OYAMBA

Baibulo ku Miyambo 29:18 limafotokoza kuti “Popamba masomphenya anthu amawonongeka”

Padziko lonse lapansi pali okhulupilira ambiri amene akuwonongeka koma sikuti akuwonongeka chifukwa cha tchimo. Izi zili chomwechi ngakhale kuti anthuwa amapita ku tchalitchi, amawerenga Baibulo angakhale enanso ndi adindo mu mpingo.

Akhristu amenewa akufa muzimu, chikhristu chawo ndi cha chizolowezi, alibe cholinga chenicheni kapena masomphenya. Masomphenya amene tikukamba apa simasomphenya a kuthupi koma ndi masomphenya a uzimu.

- Kodi mukumva kupelewera m'moyo wanu wauzimu?
- Kodi mukufuna Mulungu atakugwiritsani ntchito, koma choti muchite simukuchidziwa pokwaniritsa dongosolo lake?
- Kodi mukuzindikira kuti chikhristu chiposa zizolowezi zimene moyo wanu wakhazikika

Mayankho a mafunso onsewa ndiwo masomphenya.

Mulungu akudzutsa amayi ndi abambo akufa mu uzimu ndi kuwapanganso kukhala amoyo muzimu. Masomphenya ndiwo kukhala ndi cholinga china chokhalira ndi moyo. Chotero, masomphenya ndiyo nkhani yayikulu mu phunziro limeneli la ndondomeko za kholola la uzimu ndipo phunziroli likuthandizani kuti mukakwaniritse masomphenya anu kudzera mundondo mekeko zimene zifotokozeredwe.

ZOLINGA ZA MAPHUNZIROWA

Pa mapeto a phunziroli muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

1. Kofotokozerana masomphenya kholola la uzimu.
2. Kugwiritsa ntchito njira zopindulitsa pofuna kukolola za uzimu pamoyo wanu ndi utumiki.
3. Kupeza zinthu zimene zimalepheretsa kukolola zinthu za uzimu m'moyo wanu.
4. Kuona dziko m'mene Mulungu amaliwonera.
5. Kukolola mabvumbulutso a zokolola.

GAWO LOYAMBA: KUCHENUTSA MASOMPENYA

KUPEZA MASOMPHENYA ANU

CHAPUTALA 1

ZOLINGA

Pamene mwamaliza chaputalachi muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kufotokoza tanthauzo la masomphenya.
- Kufotokoza m'me masomphenya amabadwira.
- Kusiyanitsa kubadwa kwa uzimu ndi kwa thupi kwa masomphenya.

VESI YOTSOGOLERA

Miyambo 29:18 “Popanda maso mphenya (bvumbulutso) anthu amawonongeka”

MAU OTSOGOLERA

Baibulo limafotokoza mu buku la Miyambo kuti popanda masomphenya anthu amawonongeka. Masomphenya akukambidwa apawa ndi masomphenya a uzimu.

Masomphenya a uzimu amapereka chitsogozo, amapereka m'mene moyo umakhalira ndipo popanda masomphenya a uzimu anthu amakhalanso akufa ku uzimu. Kukhala ndi masomphenya ndi ndongosolo lozindikira cholinga chimene Mulungu anatiyikira mu Ufumu wake. Muchaputala chimenechi, tiwona “za kubadwa kwa masomphenya”.

NCHIFUKWA CHIYANI TIYENERA KUKHALA NDI MASOMPHENYA

Nchifukwa chiani masomphenya ndiofunika kwambiri; nanga nchifukwa ninji anthu opanda masomphenya amawonongeka?

Yankho la funsoli tikulipeza mu chitsanzo chimodzi cha masomphenya a uzimu chimene chikupezeka m'buku la 2 Mafumu 6:15-17. Nkhani ya Elisa ndi kapolo wake Gehazi.

Anthu a Mulungu, ana a Israyeli, anazingindwa ndi Asuri amene anali adani awo ndipo Asuri anali ndi zida zambiri za nkhondo komanso asilikali. Pamene Gehazi, kapolo wa Elisa anawona zimenezi, anagwida ndi mantha akulu ndipo analilira kwa mbuye wache “tidzapanga bwanji”.

Koma Elisa anamuza iye kuti: “Usaope, pakuti okhala pamodzi ndife achuruka kuposa okhala ndi iwo”

Ndipo Elisa anapephera kuti Mulungu atsekure maso auzimu a Gehazi ndikuona zinthu zauzimu, ndipo Gehazi anaona a nkhondo a Mulungu atazungulira Israyeli.

Muchitsanzo chimenechi, Mulungu anamulora Gegazi kuti akawone masomphenya awuzimu ndimaso ake akuthup, kotere kuti kuipanda kukhara ndi msomphenya awuzimu, anthu aMulungu sangawone zoposera zimene maso awo akuthupi amawona.

Malingana ndimene amaziwonera zinthu Gehazi, iwo anali wogonjetsedwa ndi adani awo, maso awanthu amawon azinthu mwanthupi. Ndipo masomphenya awo anakhazikika pazimene amawoma ndi maso awo akuthupi. chifukwa chopanda masomphenya awuzimu, iwo samatha kuwona chikonzero chaMulungu.

KUKHAZIKITSA MASO A UZIMU

Musanabadwe mwatsopano munali akhungu chifukwa cha tchimo, koma chipulumutso chodzera mumwazi wa Yesu Khristu chinachotsa kusapenya kumeneku ndipo Mulungu akufuna akuze maonedwe anu auzimu. Chitsanzo chabwino tikuchipeza mu utumiki wa Yesu Khristu pa ndime iyi:

Ndipo anadza ku Betsaida. Ndipo anadza naye kwa Iye munthu wakhungu, nampempha Iye kuti amkhudze. Ndipo anamgwira dzanja munthu wakhunguyo, naturukira naye kunja kwa mudzi; ndipo atamthira malobvu m'maso mwace, naika manja pa iye, anamfunsa, Uona kanthu kodi? Ndipo anakweza maso, nanena, Ndiona anthu; pakuti ndiwapenya ayendayenda ngati mitengo. Pamenepo anaikanso manja m'maso mwace; ndipo anapenyetsa, naciritsidwa, naona zonse mbee. Ndipo anamtumiza amuke kwao, nanena, Usalowe konse m'mudzi. (Marko 8:22-26)

Chodabwitsa chimenechi, chinali machiritso akuthupi amene Yesu anachita mu utumiki wake. Koma funso mkumati, ‘Nchifukwa chiani Yesu atamukukhudza munthuyu sanachire pompopompo? Kapena kuti Yesu Khristu analibe mphamvu zonse? Yesu akupereka chitsanzo cha kuthupi pofuna kuwonetsa chowonadi cha kuwuzimu. Choyamba, Yesu akufuna kuchiritsa khungu lauchimo kenako, Iye akufuna kuti maso athu awuzimu akhazikike kapena awumbidwe.

MASOMPHENYA AUZIMU NDI CHIANI?

Masomphenya awuzimu ndi kuwona zoposera dziko lowoneka ndi maso, ndipo ndikukhala ndi kumvetsetsa dongosolo la Mulungu ndi kuzindikira udindo wathu mudongosolo la Mulungu.

Okhulupilira amene akuwonongeka kuzimu ali mumagawo awa:

1. Alibe masomphenya auzimu
2. Analandira bvumbulutso la uzimu koma akhala osamvera bvumbulutsolo
3. Analandira masomphenya, koma samadziwa kuti angakwaniritse bwanji. Akhala akuyesa koma zakhala zikukanika kapena sanayese mkuyesa komwe.

Masomphenya awuzimu amapereka chithunzithunzi cha zimene Mulungu akufuna kuti ife tichite, ndipo masomphenyawa amapereka ndondomeko ya kakwaniritsidwe ka cholinga chanthu.

MASOMPHENYA A PAULO

Mtumwi Paulo anali ndi masomphenya auzimu. ndipo pa Machitidwe Atumwi 26:19 anati:

Potero, Mfumu Agripa, sindinakhala ine wosamvera masomphenya a Kumwamba; (Macitidwe 26:19)

Masomphenya a kumwamba kapena auzimu ndi amene amapereka mphamvu kwa Paulo. Iye anazindikira kuti kukhala ndi masomphenya sikokwanira; kuchitapo kanthu ndiye kofunika kwambiri.

Masomphenya akhoza osakwaniritsidwa ngati simuchitapo kanthu. Ndipo Mulungu akapereka masomphenya, amaperekanso ndondomeko zowoneka zakakwaniritsidwe ka masomphenyawo.

Pamene Mulungu anapereka masomphenya kwa Paulo, Iye anaperekeratu zinthu zoti zichitike kuti masomphenyawo akwaniritsidwe.

Komatu uka, imilira pa mapazi ako; pakuti cifukwa ca ici ndinaonekera kwa iwe, kukuika iwe ukhale mtumiki ndi mboni ya izi wandionamo Ine, ndiponso ya izi ndidzakuonekeramo we; ndi kukulanditsa kwa anthu, ndi kwa amitundu, amene Ine ndikutuma kwa iwo, kukawatsegulira maso ao, kuti atembenuke kucokera kumdima, kulinga kukuunika, ndi kucokera ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu, kuti alandire iwo cikhululukiro ca macimo, ndi colowa mwa iwo akuyeretsewa ndi cikhulupiriro ca mwa Ine. (Macitidwe 26:16-18)

Mulungu anapereka masomphenya auzimu kwa Paulo ndi cholinga chompanga iye kuti akakhale mtumiki ndi mboni yake.

Mulungu anapereka utumiki wapadera kwa Paulo kuti akatumikire kwa Amitundu, mau akuti “Amitundu” amatanthauza wina aliyense amemene si M’yuda. Choncho Paulo anapatsidwa utumiki wadziko lonse lapasi.

Mulungu anapeleka kwa Paulo zinthu izi kuti akakwaniritse:

- Kuti akatsekule maso auzimu kuchoka kum’dima kupita kukuwala.
- Kuti akawalanditse kumphamvu ya satana ndikupita nawo kwa Mulungu.
- Kuti akawatsogolere kuchikhululukiro cha machimo awo.
- Kuti akabvumbulutse cholowa chawo chاوزimu chobwera ndi chikhulupiliro

KUBADWA KWA MASOMPHENYA

Cholinga cha Mulungu ndicho kuti atipatse masomphenya auzimu ngati m’mene anachitira ndi Paulo. Ndipo Mulungu akufunanso kuti abvumbulutse cholinga chake ndi ndondomeko zokwaniritsira masomphenyawa.

Pamene muchitira umboni za kubadwa kwa masomphenyawa, mutengepo nawo mbali osati kungowonelera.

Pachilengedwe, m’mene mwana amabadwira kudziko, sizikusiyana ndimene masomphenya amabadwira m’dziko lawuzimu. Mudzadutsa magawo awa kuti mukabadwitse masomphenya anu.

KUYIMA:

“Kuyima” kumatanthauza kupanga. Masomphenya auzimu amapangidwa kapena kulengedwa ndi mzimu wanu.

Pamene Mulungu anapereka masomphenya auzimu kwa Paulo, Iye anaperekanso kumene masomphenyawa akuchokera kapena gwero lake (Mach 26:15)

KUKUZA:

Pamene mwangolandira bvumbulutso lauzimu, zimakhala ngati mwana amene wangoyambapo kumene m’ mimba mwa amayi ake amene ayenera kukula.

Chimodzimidzi, Mulungu amakunza masomphenya anu auzimu pamene mukukula ndi Iye.

Mulungu ndi amene amabadwitsa masomphenya auzimu mkati mwanu. Ndipo masomphenya amanewa amakhwima, ndipo ngati mungayese kuwasintha masomphenyawa, zinthu zimasemphanana ndi dongosolo la Mulungu kapena kuti chobadwacho chimakhala cholumala.

Ndipo masomphenya akabadwitsidwa ndi Mulungu mkati mwanu, masomphenyawo sayenera kusintha angakhale kuti mukhoza kuwakwaniritsa pogwiritsa njira zosiyanasiyana.

Masomphenya ayenera kukula pamene nanunso mukula muuzimu. Zipatso zake sikuti zimakahala chimodzimidzi nthawi zonse. Koma musayiwale masomphenya enieni amene Mulungu wakuyitanirani.

Kukula kwa masomphenya kumatenga nthawi ndithu monga chimodzimidzi ndi m'mene mwana amakulira m'mimba mwa mayi ake. Dziwani kuti masomphenyawo amafa ngati sakula mkati mwanu.

Chimodzimidzi m'mene mzimayi akhalira ndi mwana wake nthawi zonse, nanunso mukalandila masomphenya, amakhala gawo lalikuru la moyo wanu.

Pamene mwana akukula m'mimba mwa mayi, mayiyu adzimana zinthu zambiri. Chomwecho nanunso muyenera kudzimana zinthu zina angakhale kusiya zinthu zina zimene munakonza kuti mukwaniritse. Mwachitsanzo, mukhoza kufunika nthawi yambiri kuti mupephere komanso mwina kusiya chuma chadziko lapansi.

MIKWINGWILIMA:

Mlaliki 5:3 amakamba kuti:

Pakuti loto lafika mwakucuruka nchito; ndipo mau a citsiru mwakucuruka maneno. (Mlaliki 5:3)

Mau akuti 'khwimbi' amatanthuuza kuti zakikuru ndipo mau akuti 'geni' (business) matanthauza mikwingwirima m'Chiheberi. Choncho maloto kapena masomphenya ambwera mu mikwigwirima.

Kubadwa kwa mwana kumakhala ndi maululu ake kapena zobvuta zake; chimodzimidzinso, kuti masomphenya abadwe pamakhala mikwigwirima kapena kuti

maululu. Ndipo kubadwitsa masomphenya kumafunanso kudzipereka kuthupi ndi kuuzimu. Pamene mukumphunzira mphunziroli, chidwi chanu chikhale pa chimene mukufuna kuti Mulungu abadwitse mkatiu mwanu.

M'dziko la kuthupi, pamene mayi akubereka, amalolera chilengedwe chokha kuti chibadwitse mwanayo, samakakamiza kuti mwana atuluke chifukwa amatha kufa mwanayo. Mfundoyi, imagwiranso mchito pobadwitsa masomphenya anthu auzimu, ngati mungayese kubadwitsa masomphenya auzimu ndi mphamvu zanu, sizimapita patali. Chotero, muloleni Mulungu kuti alowelerepo.

Mukhonza kuchita chilichonse kuti masomphenya atumphuke, koma kuyesayesa kwanu sikungaphule kanthu, kumangowononga masomphenyawo. Petro anakuwa kwa Ambuye “Ndichokereni, Ambuye, pakuti ndine wochimwa” (Luka 5:8) Iye anazindikira kuti masomphenyawo anali akulu ndithu kuti akwanitse mwa iye yekha. Nthawi zambiri muyenera kukhala nokha m' masautso akubadwitsa masomphenya ngati m'mene mayi achitira.

KUBADWITSA:

M'dziko la kuthupi, imafika nthawi yakubadwitsa mwana ndipo iyi imakhala nthawi yowawitsa kwambiri. Izi sizikusiyana ndikubadwitsa masomphenya auzimu kotere kuti mukumana nazo nyengo zimenezi.

Kubadwitsa kumabweretsa kusintha kwakukulu chomwechonso pamene Mulungu wakupatsanani masomphenya auzimu, moyo wanu uyenera kusintha mumagawo ambiri. Izi zimafuna kudzipeleka kwambiri.

Mukhoza kukumana ndizokulepheletsani pamoyo wanu wa tsiku ndi tsiku; ndipo mutha kumabuwula ndi ululu wobadwitsa masomphenya amene Mulungu wakupatsani.

Ndipo iyi ikhoza kukhala nthawi imene mukhoza kulephera kulandira masomphenya anu. Mulungu nthawi zambiri wakhala akupereka masomphenya kwa anthu, koma chifukwa cha ululu wakubadwitsa masomphenya ambiri amalephera.

Kubadwitsa kumalira kusintha maganizidwe ngakhalenso m'mene timachitra zinthu zathu. Chifukwa cha ichi anthu ena amakanika kusiya kuyesa mwawokha pofuna kukwaniritsa masomphenya. Izi ndi zimene ana a Israyeli amachita.

Monga ngati mkazi wokhala ndi pakati, amene nthawi yace yakubala yayandikira, amva zopweteka, ndi kupfuula m'zowawa zace; momwemo takhala ife pamaso

panu, Yehova. Ife tinali ndi pakati, ife tinamva zopweteka, tafanana ngati tabala mphepo; sitinacite cipulumutso ciri conse pa dziko lapansi; ngakhale okhala m'dziko lapansi sanagwe. (Yesaya 26:17-18)

Mikwingirima imabweretsa chisoni koma imadzetsa kubwadwitsa mwana kumene kumabweretsa chimwemwe:

Mkazi pamene akuti abale ali naco cisoni, cifukwa yafika nthawi yace; koma pamene wabala mwana, sakumbukilanso kusaukako, cifukwa ca cimwemwe kuti wabadwa munthu ku dziko lapansi. (Yohane 16:21)

Baibulo limafotokoza kubuku la Yesaya kuti Mulungu anachitira umboni mikwingwilima ya Yesu Khristu. Ndipo masomphenya amenewa anakwaritsidwa pamtanda. Awa ndi masomphenya amene analonjezedwa pamene munthu anagwa (Genesis 3:15) kudzera m' mikwingwirima, chipulumutso cha munthu chinakwaniritsidwa.

Nyengo ya mikwigwirima ndi nyengo yowawitsa, koma ndi mikwigwirima imene imabadwitsa masomphenya.

Atero Yehova, Monga vinyo watsopano apezedwa m'tsango, ndipo wina ati, Usaliononge, pakuti muli mdalitso m'menemo, momwemo ndidzacita cifukwa ca atumiki anga, kuti ndisawaononge onse. Ndipo ndidzaturutsa mbeu mwa Yakobo, ndi mwa Yuda wolowa nyumba wa mapiri anga; ndipo osankhidwa anga adzalandira colowa cao, ndi atumiki anga adzakhala kumeneko. (Yesaya 65:8-9)

KUBABWA

Kukula kwa masomphenya kumayenera kufika kumapeto pamene masomphenyawo ayenera kubadwa. Ngati masomphenya abadwa nthawi isanakwane kapena kuchedwa kubadwa, izi zimatha kubweretsa imfa.

Pamene mwana wabadwa kuthupi, amapitilirabe kukula. Chimodzimodzi pamene masomphenya abadwa, amapitilira kukulabe ndipo zinthu zina zatsopano zimawonekera.

MASOMPHENYA A ABRAHAMU

Abrahamu anayesayesa kubadwitsa masomphenya a Mulungu kudzera m'mphamvu zake mukubadwa kwa Ishimayeli. Iye imazidikira kuti Mulungu amafuna kum'panga iye kukhala mtundu waukulu koma sanakhulupilire kuti izi zidzachitika kudzera mwamkazi wake, Sara.

Abrahamu anachitapo kanthu mwa iye yekha ndipo Ishimayeli anabadwa. Koma kodki izi zinachitika ndi mphamvu ya Mulungu kapena Abrahamu? Kodi kukwalitsidwa kwa masomphenya kudzera mwa Ishimayeli kunali kopangidwa ndi Mulungu kapena ndi munthu?

Ishimayeli akuyimila kufuna kukwanilits dongosolo laMulungu ndi nzeru zathu kapena njira zathu zakuthupi. Koma Isaki akuyimira masopenya obadwitsidwa ndi mwini wake mulungu.

KODI GWERO LA MASOMPHENYA AUZIMU NDI CHIANI?

Atafunsidwa, “tipange bwanji kuti tikachite zazikuru za Mulungu” ndipo Yesu anayanka nati “iyi ndiye ntchito ya Mulungu”. Izi zikungowenetsera kuti Yesu ndi gwero la masomphenya (Yohane 6:28-29).

Mulungu sanafuna kuti Abrahamu akhale gwero la masomphenya ake ndipo samafuna kuti ife tikhale gwero la masomphenya auzimu. Mulungu sakufuna kuti ife tipange masomphenya athu patokha ndikuthekera kwathu. Mulungu ndiye mwini masomphenya ndipo iye akufuna kuti ife tilandire masomphenya ake.

Malemba amawonetsa kuti Mulungu sanalankhulenso ndi Abrahamu kwa zaka khumi ndi zisanu atangobadwa Ishimayeli. Mpaka Abrahamu atazindikira kuti mwayekha sanakwanitsa kubweretsa mwana wa malonjezano; masomphenya a Mulungu anabadwanso mkati mwake.

Kuti masomphenya a Mulungu abadwe, nkoneyera kusiya kuyesayesa mwatokha ngati m'mene Abrahamu anachitira ndi Ishimayeli. Inde zimakhala zovuta kusiya kuyesa kwathu, koma ngati mmene Mulungu anamulankhulira Abrahamu asalire Ishimayeli, chomwechonso Mulungu mwini ndiye mwini masomphenya osati kuyesayesa kwathu.

KODI MWAKONZEKA?

Kubadwa kumafuna kusintha, ku dziko la kuthupi, mwana ayenera kusiya chitetezo cha amayi ake. Pamene munabadwa mwatsopano, munasiya moyo wanu wauchimo ndikumulola Yesu kuti alamulire moyo wanu. Chimodzimodzinso, kubadwitsa masomphenya auzimu kuchoka malo amene timamva bwino ndikupita ku magawo ena amene sitikuwadziwa.

Kodi mwakonzeka kulandira masomphenya auzimu? Kodi mwakonzeka kukumana ndi zokhoma? Kodi mwakonzeka kukumana ndi mazunzo auzimu kuti mukabadwitse chatsopano mmoyo wanu wa Chikhristu? Ngati simunakonzeka, nkwabwino kungosiya maphunziro amenewa chifukwa ngati mumvetsetsa masomphenya aphunzitori, moyo wanu sudzakhara chimodzimodzi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yapamtima yoloweza?

2. Kodi masomphenya awuzimu amatanthauza chani?

Welengani mndandanda wa mayina oyamba, kenako werengani mdandanda wachiwiri. Mukatero sankhani nambala ya chiganizo imene ikugwirizana ndi dzina la munthu limene likupezeka mu mndandanda woyamba. Onani chitsanzo chaperekedwacho.

Mdandanda Woyamba Mdanda Wachiwiri

- | | |
|----------------|---|
| <u>2</u> Paulo | 1 ndiyayesa kubadwitsa masomphenya kudzera mwa Ishimayeli |
| ___ Gehazi | 2 sindinamver masomphenya akumwamba” |
| ___ Abrahamu | 3 “Ndipange bwanji” |
| ___ Mulungu | 4 "kodi ndidzangoyima koma osabala? |
| ___ Yesu | 5 "chokani kwa ine Ambuye, ndine munthu wochimwa” |
| ___ Petro | 6 Mulungu anachitira umboni mwikhiwirima yesu ndipo anakhutira. |

3. Werengani chiganizo mu mndandanda woyamba, ndipo ikani nambala kumbuyo kwa mau amene ali mzere imene ikuyimira chiganizo chimene chikugwirizana ndi nambalayo.

Mdandanda Woyamba Mdanda Wachiwiri

- | | |
|-------------------|--|
| ___ KUYIMA | 1 Nthawi imene masomphenya amakula mkati mwa mzimu wanu. |
| ___ KUKUZA | 2. Angakhale musanabadwitse, nthawi imene simukuyenera kuyesayesa mwa inu nokha koma kumulola Mulungu abadwitse yekha masomphenya. |

___**MIKWINGWIRIMA:** 3 Chiyambi cha masomphenyo mkati mwa mzimu wanu
zimayamba ndi Mulungu.

___**KUBADWITSA:** 4 Nthawi yazowawa yakubadwitsa kwauzimu, zowawitsa
zakuthupi angakhalenso mumaganizo.

MAFUNSO OWONJEZERA

1. Fotokozani zimene mumadziwa zokhudzana ndi mikwingirima malingana ndi ndime izi:

Yohane 16:21: amabweretsa chisoni, koma izi zimadzetsa chimwemwe.

1 Atesalonika 2:9: kugwira ntchito, kuthupi ndi kuuzimu komwe.

1 Atesalonika 2:9: ndikubereka ku dziko la kuthupi ndi la kuuzimu komwe.

Agalatiya 4:19: Yesu anabadwa mkati mwanu ngati zotsatira zake.

Agalatiya 4:19: izi zimabadwitsa Yesu mkati mwanu.

Aroma 8:22-25: **zimabweretsa** chiyembekezo

Aroma 8:22- 25: **zimaberetsa** chiyembekezo

Yesaya 66:7-9: **ndicholinga cha Mulungu** kuti **mikwigwirima** kapena masautso auzimu kuti abale **zauzimo**.

Taganizirani za mau awa

“masomphenya opanda chochita ndi osatheka kapena ndikudzinyenga chabe.

chochita chopanda masomphenya chimakhala cholemetsa.

Ntchito yokhala ndi masomphenya ndi mene imamanga utumiki”

3. “Anthu oyipa kapena amphulupulu amabala maganizo aupandu”

Taonani, ali m'cikuta ca zopanda pace; Anaima ndi cobvuta, nabala bodza.
(Masalmo 7:14)

4. Pali amayi angapo mu Baibulo atakhala zaka zambiri osabereka, Mulungu anawakhudza nabereka ana amphamvu.

- Sara anabala Isaka
- Lakelo anabala Yosefe
- Manowa anabala Samisoni
- Hana anabereka Samueli
- Rute anabala Obedi
- Elizabeti anabala Yohane

CHAPUTALA 2

MASOMPHENYA

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi muyenera kudziwa zinthu izi:

- Kusiyana kwa chilungamo chathupi ndi chاوزimu.
- Pezani zitsanzo za zokolola zathupi ndi zokolola za kuuzimu.
- Fototokozani ndondomeko zolandilira masomphenya.

VESI YOTSOGOLERA

Kodi simunena inu, kuti, yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta (Yohane 4:35.)

MAU OYAMBA

Chaputala changopitachi, tinafotokoza za ndondomeko za kukuza masomphenya auzimu; ndipo chaputala ichi chitambasula masomphenya amene Yesu Khristu akufuna kuti abadwitse mu mzimu wanu ndipo. Chaputalachi chikufotokonzaso mmene mungalandilire masomphenyawa.

Masomphenya ake ndi omwe aja amene Yesu anapereka kwa aphunzira ake dzaka 2000 zapitazo. Ndipo kuti tidzetse masomphenya amenewa tiyenera kuti timvetse mfundo imodzi ya Mau a Mulungu ndipo mfundo imeneyi imakhudza kufanana kwa choonadi chاوزimu ndi chathupi.

Chaputalachi chikufotokozera mfundoyi ndikuwonetsera mmene Mulungu angagwiritsire ntchito moyo wanu.

CHOONADI CHAKUTHUPI NDI CHAUZIMU

Baibulo limatsindika nkhani za anthu, malonjezano, ma uneneri ndi mfundo zakachitidwe kazinthu.

Gawo lalikulu la Baibulo limafotokoza nkhani za anthu, makamaka mmene Mulungu anchitira nawo kapena mmene iwo anachitira **ndikunkhura** kwa Mulungu. Magawo enanso akuluakulu a Baibulo amafotokoza za uneneri wa m'tsogolo ndiponso pali malonjezano ambiri amene anaperekedwa kwa anthu a Mulungu.

Baibulonso limafotokoza mfundo zoti tigwiritse ntchito kuti timvestse mau ake a Mulungu. Ndipo imodzi mwa mfundoyi ndikufanana kwa choonadi cha kuthupi ndi chauzimu. Mulungu amagwiritsa ntchito zinthu zakuthupi pofuna kufotokozerana zoonadi chauzimu

Mafanizo a Yesu Khristu ndi chitsanzo choonadi chathupi ndi chauzimu. Mwa chitsanzo, Yesu Khristu anapereka chitsanzo cha m'zimayi amene anagwiritsa ntchito chotupitsa pang'ono ku mkate. Ndipo kufalikira kwa chotupitsacho kukuyimira kufalikira kwa ufumu wa Mulungu padziko lapansi.

Ili ndifanizo limodzi la Yesu limene akugwiritsa ntchito ngat chitsanzo chakuthupi pofotokoza chilungamo chauzimu.

Mfundo ya kufanana kwa choonadi chathupi ndi chauzimu ikufotokozedwa ku buku la 1 Korinto.

Koteronso kwalembedwa, 11 Munthu woyamba, Adamu, anakhala mzimu wamoyo. Adamu wotsirizayo anakhala mzimu wakulenga moyo. Koma cauzimu siciri coyamba, koma cacibadwidwe; pamenepo cauzimu. (1Akorinto 15:45-46)

Ichi ndichitsanzo chabwino chakufanana kwa choonadi chakuthupi ndi chauzimu. Munthu woyamaba kulengedwa anali wakuthupi kapena wakunthaka amene dzina lake linali Adamu. Koma Yesu Khristu amene ali ngati Adamu wotsiriza, ndipo Iye ndiye munthu wakumwamba kapena wauzimu.

Adamu ndi chitsanzo chabwino chakuthupi chauzimu chimene anachibvumbulutsa kudzera mwa Yesu. Kudzera ma munthu wachibadwidwe kapena wakuthupi, tchimo ndi infa zinalowa dziko lapansi ndipo chipulumutso chinadza ndi munthu wakumwa kapena wauzimu.

Chinthu chimene chili chakuthupi kapena chachibadwidwe ukhoza kuchigwira, kuchiona angakhale kuchimva kumene. Koma chimene chili chauzimu mukhoza kuchizindikira ndi makuti auzimu okha.

Zinthu zakuthupi zimadziwika kuthupi komweko koma zithu zauzimu zikhoza kuzindikiridwa ndi makutu auzimu kudzera m'mabvumbulutso a Mzimu Woyera. Kumvetsetsa izi mkothandiza kuti tikuze kumvetsa kwathu kwa Mau a Mulungu.

KHOLOLA

Masomphenya amene Yesu Khritsu anaikiza mwa ophunzira ake ndi amene amafuna kuti abadwitse mkati mwa mzimu wathu ndipo anabvumbulutsidwa ndi chitsanzo choonadi chathupi chazimu.

Yesu anati kwa ophunzira ake:

Kodi simunena inu, kuti yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta. (Yohane 4:35)

Yesu samalankhula za kholola lakuthupi ngati m'mene anthu achitira kumunda, iye makamba za kholola wauzimu. Iye anapereka chitsanzo cha kholola la kuthupi pofuna kuti omutsatira ake amvetse tanthauzo lake ndi kumvetsetsa m'mene zimagwilira ntchilo m'moyo wauzimu.

KODI AMATANTHAUZA CHIANI?

Kodi chitsanzo cha kholol la la kumunda chikutanthauza chiani ku moyo wauzimu?

Werengani Yohane 4:3-35 paulendo wake wopita ku Yudeya, Yesu anadutsa ku Samariya, ndipo pamene ophunzira ake anapita kukasaka chakudya, Yesu Khristu analalikira Uthenga Wabwino kwa mzimayi wa ku Samaria.

Ndipo ophunzira ake atabwera nacho chakudya, Yesu anati kwa iwo

Chakudya changa ndiye chakuti ndichite chifuniro cha Iye amene anandituma, ndikutsirinza ntchito Yake (Yohane 4:32-34).

Yesu anazindikira kuti kuposa zinthu zina zopatsa moyo, chinthu chofunika kwambiri ndiye kuchita chifuniro cha Mulungu pomaliza kugwira ntchito Yake. Koterokuti Yesu anatsindika kuti chinthu chofunika kwambiri ndicho kuchita ntchito yake ndi chifuniro chake.

CHIFUNIRO NDI NTCHITO YA MULUNGU

Kodi chifuniro cha Mulungu ndi chiani? Nanga ntchito yake ndi chiani. Izi zabvumbulutsidwa m'masomphenya a kholola.

Yesu anawuza ophunzira ake kuti aponye maso awo m'munda ndikupenya zokolola zimene zacha kale. Iye anagwiritsa ntchito **chitsanzo** cha munda pofuna kuwonetsera minda yauzimu ya miyandamiyanda ya anthu amene apsysa kungodikira kuti akololedwe mu ufumu wa Mulungu.

Mzimayi waku Samariya ndi chitsanzo chabwino cha kuchuluka kwa zokolola zauzimu. Mzimayi anali wokonzeka kulandira mokondwera Uthenga Wabwino ndipo chifukwa chakukolola, mzinda wonse inagwedezeka ndikumudziwa Yesu.

Ndipo m'mudzi mula anthu Asamariya ambiri anamkhulupirira iye cifukwa ca mau a mkazi, wocita umboniyo, kuti, Anandiuza ine zinthu ziri zonse ndinazicita. ndipo ananena kwa mkazi, kuti, Tsopano sitikhulupira cifukwa ca kulankhula kwako: pakuti tamva tokha, ndipo tidziwa kuti Mpulumutsi wa dziko lapansi ndi Iyeyu ndithu. (Yohane 4:39,42)

MASOMPHENYA LERO LINO

Pamene anali pakati pa munda weniweni wakuthupi, masomphenya auzimu anabadwitsidwa mkati mwa ophunzira a Yesu Khristu. Ndipo ndi masomphenya omwewa amene Yesu Khristu akufuna kubadwitsa mkati mwa mzimu wanu. Ndipo mukazindikira zenizeni za masomphenyawa komanso udindo wanu, moyo wanu sudzakhala chimodzimodzi.

Yesu anati:

Ndipo munda ndiwo dziko lapansi (**Mateyu 13:38**)

Dziko lonse lapansi kuyambira ku Africa kufikira kumalekezere a dziko, zokolola zacha, koma okolola ndiwochepa. Miyandamiyanda ya anthu ikudikira kuti ikamve Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu.

Komanso masomphenya sanasinthe, akadali chikhalire momwe Yesu adawapelekera m'moyo wa ophunzira ake. Chifuniro cha Mulungu chikadali chomwe chija chifukwa ntchito ya Mulungu siinathe. Masomphenya ndiye munda wa kholola la dziko lapansi.

ZOKOLOLA ZATANI?

Chifukwa chiani Yesu anagwiritsa ntchito chitsanzo cha kholola pofuna kuwonetsera masomphenya auzimu kwa ophunzira ake? Pali zitsanzo zambiri za kuthupi zimene Yesu anakatha kugwiritsa ntchito. Koma ndi chifukwa chiani Iye ansankha kugwiritsa ntchito chitsanzo cha zokolola?

Chitsanzo cha kholola chinali chomvetsetseka kwa ophunzira ake. Mbiri ya ana a Israyeli imayamba ndi Adamu amene ntchito yake inali ulimi ndipo chuma cha nthawi imeneyi chinali ulimi angakhale nthawi ya Mose imene.

Mu nthawi ya Yesu, chuma chinakhazikika pa zokolola ndipo izi zimakhudza angakhale chipembedzo cha nthawi imeneyo. Panali zikwondwewero zitatu zimene Mulungu anakhazikitsa zokhudza zokolola. Kholola limakhudzanso chipembedzo chifukwa panali zikwondwewero zingapo zongwirizana ndi kholola zimene Mulungu anakhazikitsa. Mwachitsanzo, panali zikondwewero za Pasaka (Ekisodo 23:16) chikondwewero, madyelero a zipatso zoyamba (Ekisodo 34:22) ndi madyelero a mkate opanda chotupitsa. Koma nkhani yayikulu ndiyakuti madyelero onsewa amachitika munyengo ya kholola.

Chifukwa chakuti moyo wa a Yuda unakhazikika pa zokolola, kunali kosabvuta kuti ophunzira amvetsetse chitsanzi ichi.

Chofunikanso kwambiri ndichakuti pali mfundo za kufesa zimene zimalumikazana ndi zokolola. Ndipo mfundo za makololede a kumunda zimagwirizana ndi kakoloredwe ka zokolola zauzimu ndipo ophunzira a Yesu izi amazimvetsa kwambiri chifukwa moyo wa tsiku ndi tsiku unali wodallira ulimi kapena zokolola. Koterokuti kugwiritsa tchito mfundo za okulola za kumunda kukhoza kuthandiza kuti tikolole zochulukira zauzimu. Mfundo zimenezi tizisanthulabe chaputala china.

Ophunzira a Yesu azindikira machawi amene akufinika chifukwa zokolola zikacha ziyenera kukololede mwachangu, ndi nkhani yokolola kapena kuzisiya kuti ziwonongeke m'munda momwemo. Ndi chifukwa chake Yesu analakhula kuti:

Zokolola zachulukira koma antchito achepa (Mateyu 9:37).

KULANDIRA MASOMPHENYA

Pamene Yesu Khristu analankhula ophunzira ake masomphenya a zokolola. Iye anafotokoza ndondomeko zisanu zowayenerera kulandira masomphenya.

Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta. (Yohane 4:35)

(1) KODI SIMUNENA INU, (2) KUTI, YATSALA MIYEZI INAI, NDIPO KUDZA KUMWETA? (3) ONANI NDINENA KWA INU (4), KWEZANI MASO ANU, (5) NIMUYANG'ANE M'MINDA, KUTI MWAYERA KALE KUFIKIRA KUMWETA. (YOHANE 4:35)

Ndondomeko Yoyamaba “Kodi simunena inu kuti”

Okhulupilira ambiri amawononga nthawi yawo yambiri kukambirana zakholola. Iwo nthawi zonse amakhala akupita ku nkhoekwe (tchalitchi) sabata ndi sabata namakambirana njira zabwino zokololera. Amanola zikwakwa zawo zomwetera kenako ndikubwelerera kunyumba.

Nthawi zambiri amakumana namakambirana njira zabwino zokololera, kotero kuti mpaka zaka zimakhala zikuppita akungokambirana, koma chonsecho palibe ndi m’modzi yemwe amene amapita kumunda kukakolera.

Yesu akutiuzza kuti kungokamba za zokolola zauzimu nkosakwanira, muyenera kutengapo gawo pokolola zinthu zauzimu. Koma izi sizikutanthauza kuti wina aliyense asiye ntchito nayamba kupempha ndalama ndicholinga choti akalalike Uthenga Wabwino. Koma nkhani yayikulu ndi yakuti munthu wina aliyense ayenera kutengapo gawo pokolola zauzimu osati kungolankhula chabe.

Ndondomeko Yachiwiri “Yatsala Miyezi Inai”

Kuti mukhale gawo limodzi la kholola lauzimu, simukuyenera kuchita chidodo ndipo simungadikire kudzagwira nchitoyi mtsogolo.

Longani zenga, pakuti dzinthu dzaca; idzani, pondani, pakuti cadzala coponderamo mphesa; zosungiramo zisefuka; pakuti zoipa zao nzazikuru. Aunyunji, aunyunji m'cigwa cotsirizira mlandu! pakuti layandikira tsiku la Yehova m'cigwacotsiriziramlandu. Yoweli 3:13-14

Ndondomeko Yachitatu “Ndinena Ndinu”

Njira za Mulungu ndizosiyana ndi za munthu:

Pakuti monga kumwamba kuli kutali ndi dziko lapansi, momwemo njira zanga ziri zazitari kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambana maganizo anu. (Yesaya 55:9)

Anthu amakamba za zokolola zauzimu ndikuchita chidodo, koma zimene Mulungu amakamba m’zosiyana ndi zokamba za munthu.

Ndondomeko Yachinayi “Kwezani Maso Anu”

Maso a ophunzira a Yesu anatchingika, sanalunjike masomphenya awo pa masomphenya a munda wa zokolola zauzimu.

Kuti mulandire masomphenya auzimu muyenera kutengapo gawo lanu. Muyenera kukweza maso anu ndikuposa zotchinga kuti muone. Zolempheretsa za moyo uno zisakulepheretseni kuchita kholola lauzimu.

Ndondomeko Yachisanu “Wonani Kholola”

Kungochotsa maso anu kuzolepheretsa kuona munda wa zokolola sizokwanira ayi, muyenera kuona zinthu m'mene Mulungu amaziwonera. Samazindikira za udindo wawo m'munda wazokolola.

Ambiri alibe masomphenya auzimu chifukwa chakuti satsekula maso awo ndikupenya ndipo iwo samakhala ndi chidwi ndikuona mmene zithu ziliri m'munda.

KUTI MULANDIRE MASOMPHENYA AUZIMU...

- Simukuyenera kungokamba za izi ayi.
- Simungakwanitse kuchita chidodo
- Ndipo muyenera kumvera zimene Mulungu akufuna ndikumvera zimene akukamba, "kodi tidzatuma ndani ndipo adzapita ndi ndani" (Yesaya 6:8).
- Ndipo maso anu alunjike kumunda wazokolola posakodwa ndi ziyangoyango zoti musapenye munda wazokolola.
- Maonedwe anu azinthu akhale ngati a Mulungu

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yapamtima yotsogolera

2. kodi mau oti choonadi chathupi ndi choonadi chauzimu amatanthauza chani?

3. Chitsanzo chakuthupi chimene Yesu anapereka kwa ophunzira ngati masomphenya auzimu ndichitsanzo cha _____
4. Chitsanzo cha munda wa kholola ndi _____
5. Tchulani zifukwa zitatu zimene Yesu amagwiritsira ntchito zitsanzo zakuthupi zazokolola pofuna kupereka masomphenya auzimu kwa ophunzira ake.

6. Tchulani ndondomeko zisanu zimene zaperekedwa pa Yohane 4:35 zimene zingathandize kuti mulandire masomphenya auzimu.

ZOPHUNZIRA ZAPADERA

Chaputala ichi chimatsindika zotengapo mbali mu masomphenya a kholola.

Werengani nkhani ya Msamaria Wachifundo (Luka 10:25-35). Chaputala ichi chimawonetsera chidwi chotengapo mbali. Komanso ndimeyi ikuwonetsera m'mene okhulupilira amayionera nkhani ya kholola lauzimu m'munda wa dziko lapansi.

Taonani mawonedwe a zinthu a anthu awa, wansembe, wakuba, Mlevi, wachifwamba Msamaria, wachilamulo ndi mwini nyumba. Ndipo tawonani zolinga za Wachilamulo amene anafunsa funso limene linapangitsa Yesu kuti ofotokoze fanizoli.

KHALIDWE

ZOLINGA

Wachilamulo: Anawona funso lofuna kukambirana

Wachifwamba: Amaona munthu akhoza kumubera

Wansembe ndi mlembi: Anawona bvuto lofunika thandizo koma iwo anasankha kusachitapo kanthu

Mwini nyumba:

Iye amangowona kasitomala oti akhoza kupanga naye ndalama kapena phindu.

Msamaria

Iye amawona munthu akumwalira, zokolola zikuonongeka ndipo anachitapo kanthu mwa iye yekha ku chosowa cha munthuyu.

CHAPTAULA 3

MASO AKE ALI PA MAYIKO ONSE

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kudziwa zinthu izi:

- Kufotokoza tanthauzo lakuona dziko m'mene Mulungu amaliwonera.
- Kumvetsetsa m'mene zinthu ziliri m'munda wa kholora lauzimu m'dziko lapansi.
- Kuchitapo kanthu potenga mbali yokhala m'modzi wa anthu otuta nawo kholola lauzimu padziko lapansi.

VESI YOTSOGOLERA

Maso ake ayang'anira amitundu (Masalimo 66:7)

MAU OTSOGOLERA

Chaputala chapitachi chimatsindika mfundo yokweza maso anu ndikupenya m'munda wa kholola lauzimu la dziko lapansi.

Ophunzira a Yesu sanali ndi masomphenya omwe Yesu anali nawo. Ndichifukwa chake Yesu amamema kuti atsekule maso ndikupenya chosowa chenicheni cha dziko lapansi ngati m'mene iye mwini amaonera.

Muyenera kuona dziko lapansi ngati m'mene Mulungu amalionera. Izi ndizofunika ngati mukufuna kukuza masomphenya anu auzimu.

Chaputala ichi chikutsindika kholola la dziko lapansi. Bairbulo limafototokoza kuti maso ake ali pa dziko lapansi. Koma funso mkumati, "Kodi Mulungu amati bwanji akaona munda wa dziko lapansi?"

MINDA YOPANDA KANTHU, ZIKWAKWA ZOSATHWA

Mulungu amaona dziko lapansi ngati munda wa kholola.

Mundawo ndiye dziko lapansi (Mateyu 13:38).

Mfuwu wochokera ku dziko lapansi umveka m'makuti a Mulungu.

Yeremiya 8:20 Masika apita, mphakasa yatha, ndipo ife sitinapulumsidwe.

Ndipo kholola lauzimu la munda wadziko lapansi likufanana ndi minda imene m'neneri Yoweli analilira:

Gomani, akulima m'minda inu; lirani, akulima mpesa; cifukwa ca tirigu ndi barele; pakuti zinthu za m'minda zatayika. (Yoweli 1:11)

Maso a Mulungu akapenya mayiko a dziko lapansi, Iye amawona kholola lauzimu likuonongeka chifukwa cha kuchepa kwa otuta kapena okolola. Yesu sanafotokoze kuti ofesa ndi ochepa, koma kuti antchito achepa kuti akolole kholola lauzimu. Ndipo ndizoonadi kuti munda wakula koma atchito achepa (Mateyu 9:37).

Pakadali pano kumpoto kwa Amerika kumapezeka atumiki 94 mwa atumiki 100 onse adziko lapansi. Izi zikutathauza kuti atumiki 6 pa atumiki 100 akutumikira anthu 94 a dziko lonse lapansi.

Pali anthu miyandamiyanda, mitundu yokwana 16,000 amatindu yosiyanasiyana amene Uthenga Wabwino sunawafikire. Ndipo pali zilankhulo zokwana 2000 zimene Baibulo silinatanthauziridwebe.

Mwa midzi yokwana 100,0000 yaku India, midzi yokwana 9,950 ilibe atumiki ofalitsa Uthenga Wabwino. kukakhala ku Japani, mwa anthu 100 alionse, ndi munthu m'modzi yekha amene amakhala kuti ndi m'Khristu.

Izi zikungochitira umboni kuti chosowa cha Uthenga Wabwino ndi chachikuru mu madera onse a dziko lapansi, kuyambira mayiko aku Africa ndi mayiko onse adziko lapansi. Umu ndi m'mene Mulungu amawonera maiko a dziko lapansi.

Izi ndi zimene Mulungu amaona akayang'ana pa dziko lapansi.

CHOLEPHERETSA

Baibulo limafotokoza kuti:

Pakuti pali Mulungu mmodzi, ndi Mtetezi mmodzi pakati pa Mulungu ndi anthu, ndiye munthu, Kristu Yesu (1 Timoteo 2:5).

M'khalapakati kapena mtetezi amafunika pamene magulu awiri a anthu sakumvana.

Ndipo Mulungu akaliona dziko lapansi amaona anthu ambiri ali olekanitsidwa ndi Iye. Ndipo chimene chalekanitsidwa munthu ndi Mulungu ndi tchimo.

Yesu Khristu ndiye m'khalapakati wa munthu ndi Mulungu. Ndipo awiriwa sangayanjane popanda Yesu chifukwa Yesu anapanga zotheka kuti apulumutsidwe ku tchimo ndi kulandiridwa ndi Mulungu.

Anthu ambiri akuyembekezera kumva Uthenga Wabwino wa chipulumutso ndipo Uthenga Wabwino umene Yesu Khristu analamulira ophunzira kuti alalike cholinga chake ndicho kubwenzeretsa ubale wa muthu ndi Mulungu. Anawalamulira kuti akafalitse uthenga kuchokera ku Yerusalemu, Yudea, Samariya, ndi dziko lonse lapansi.

Ophunzira amayenera kuyamba kulalika Uthenga Wabwino kuyambira Yerusalemu. Amayenera

kutero chifukwa kunali kosabvuta kufikira anthu amene amadziwa kale chikhalidwe chawo. Pamene anthu aku Samariya ndi Yudea ndi osiyaniranapo ndi anthu aku Yerusalemu m'chikhalidwe. Kotera kuti amafunika dongosolo lapaderadera kuti Uthenga Wabwino ukawafikire.

Pachiyambi ophunzira a Yesu amachita chidodo kuti akalilike Uthenga Wabwino kwa anthu ena Amitundu chifukwa chakusiyana chikhalidwe. Chifukwa cha mazunzo, anayamba kufalitsa Uthenga Wabwino kudutsa malire a Yerusalemu angakhale kuti uthenga sunafalikire kwambiri (Machitidwe 8:4)

Ngati mukukwaniritsa lamulo lalikuru lofalitsa Uthenga Wabwino ndikukulola kholola la uzimu, tiyenera kusiyana ndi athu amtundu wathu ndikupita kukalikira kwa anthu amitundu ina. Izi zikutanthauza ngakhale kuchoka dera limene timakhala. Mukuyenera kuchitapo kanthu polalikira Uthenga Wabwino wonjanitsa munthu ndi Mulungu.

CHOLEPHELETSA CHINA

Kupatula tchimo ngati chinthu chimodzi chomulekanitsa munthu ndi Mulungu, pali cholepheretsa china cha kholola lauzimu pakati pa Yesu Khristu – Kulephera kwa anthu ake kukalalikira Uthenga Wabwino.

Ndipokhapokha mwalandira masomphenya akholola lauzimu, simungamvetse za udindo wanu mu Ufumu wa Mulungu. Masomphenya akholola ayenera kukhala gawo limodzi la moyo wanu angakhale kuti anthu ambiri sizimawakhudza.

Nthawi zambiri timakonda kulankhula za zinthu zimene timakonda monga kuonera kanema kapena m'mene timawakondera akazi athu. Koma nthawi zambira sitimakamba za anthu otayika. Kodi ndi kangati kamene timaganizira za anthu ambiri amene akutayika kapena mmene zokolola zikuonongekera mmunda?

Paulo akuyankula za zinthu za chizolowezi zimene timachita tsiku ndi tsiku monga kudya ndi kumwa ngati zimene zikhoza kupereka ulemelero kwa Mulungu (1 Akorinto 10:31). Tikhoza kugwiritsa ntchito chili chonse pokwaniritsa masomphenya auzimu ndipo tsiku lililonse limakhala mwayi okwaniritsa masomphenyawa.

Mukazindikira udindo kwa anthu amene akutayika, masomphenya a kholola la zauzimu limawira mkati mwanu, ndipo mumakhala m'modzi mwa anthu ochokera maiko osiyanasiyana amene amaona zinthu ngati m'mene Mulungu amazionera pofalitsa Uthenga Wabwino.

Ndipo anthu amenewa amatchedwa “Okhulupilira a dziko lapansi” ndipo awa ndi okhulupilirawa akhoza kunena mwa mphamvu kuti:

“ndikudziwa kuti tsiku langa lero lapindulitsa potumikira lingaliro la Khristu pa dziko lonse lapansi”

Ichi ndiye chenicheni cha kholola lauzimu izi ndi zimene mau oti kuona dziko m'mene Mulungu amaonera kumathanthauza.

MAKOMO OTSEKUKA

Maiko ena amaoneka ngati osafikirika ndi Uthenga Wabwino kapena kuti otsekeka. Ndipo maiko amene atchedwa kuti osafikirika ndi uthenga, nthawi zambiri boma silimalola kuti atumiki a Mulungu alalike Uthenga Wabwino ndipo amayesetsa kuti uthenga usafale m'dzikomo.

Koma Mulungu samaona malire. Ndipo iye samaona dziko losafikirika ndi Uthenga Wabwino angakhale kuti pali maiko ena amene amaletsa atumiki ochokera maiko ena kulalikira Uthenga Wabwino.

Koma khomo lakutsogolo la dziko likatsekeka, pamakhala khoma lakumbuyo limene limakhala kuti latseguka. Mwachitsanzo, maiko amene amaletsa atumiki kulowa m'dzikomo, nthawi zambiri anthu ena okagwira ntchito zina monga zomangamanga kapena zaulimi, amakhala akulalikabe Uthenga Wabwino uku akugwira ntchito imene anabwelera.

Maiko amene tikuti ndiotsekeka ku Uthenga Wabwino, pali okhulupilira amene azidikira udindo wao pofalitsa uthengawu. Kotere kuti tiyenera kukhudzika ndi mphamvu komanso maulamuliro amene akulimbana ndi cholinga cha Mulungu:

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

Muyenera kukhala okhudzika ndi dziko lapansi angakhale kulilira kumene ngati m'mene Yesu analilira mzinda wa Yerusalemu. Kotere kuti tiyenera kuona dziko ngati m'mene Mulungu amalionera.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera ya pamtima.

2. Kodi kuliona dziko ngati m'mene Mulungu amalionera zimatanthauza chiani?

3. Kodi ndi anthu angati pa dziko lonse lapansi amene Uthenga Wabwino sunawafikirebe?

4. Kodi ndi magulu angati a anthu amene Baibulo silinamasuliridwe mu chiyankhulo

chawo?

5. Chifukwa chiani pali kulekana kofunika m'khalapakati (Yesus Khristu) kuti munthu ndi Mulungu ayanjane.

Lembani chilembo cha “T” kutsogolo kwa chiganizo chimene ndichoona, ndipo lembani F ku chiganizo chilichonse chimene sicholondola.

- a. _____ Mayiko otsekeka sangafikiridwe ndi Uthenga Wabwino.
- b. _____ M'dani weneniweni wotsutsana ndi kufalitsa Uthenga Wabwino ndi ma Boma
- c. _____ Yesu anakamba kuti kudzakhala okolola ochepa m'munda wa kholola lauzimu ladziko lapansi.
- d. _____ Kodi kukhala wokhulupilira wa dziko lonse lapansi kumatanthauza chiani?

Zophunzira zowonjezera

Werengani za masomphenya a Yesaya (6:1-9)

Masomphenyawa anali:

- Masomphenya okwera kumwamba (msinkhu): Anawona Mulungu
- Masomphenya olunjika mkati (kuya) anadziunguza yekha m'moyo wake wauzimu.
- Masomphenya olunjuka kunja (mulitari) amaona dziko lonse lapansi.

Anali masomphenya:

- A chiyero cha Mulungu.
- Okuswa mtima: “ndine munthu wochimwa”
- Opangitsa kuthedwa “ndili munthu wa miloma yonyansa”
- Kugwira njakata “ndidzatuma yani”

Lingalirani za mau ofunikira awa.

- Tsoka: mau akulapa (vesi 5)
- Mphulupulu zako zachotsedwa: mau osonyeza kukonzedwanso mwatsopano
- Kauze anthu awa: Kuyitanidwa (vesi 9)

GAWO LACHIWIRI

KUMVETSETSA CHOLINGA CHA KUSELI KWA MASOMPHENYA

CHAPUTALA 4

DZIKO LAPANSI MU MAU A MULUNGU

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro, muyenera kutha kuchita zinthu izi:

- Kufotokoza dongosolo la Mulungu pa maiko a dziko lapansi kuchokera pachiyambi.
- Kuona m'mene masomphenyawa avumbulutsidwira kuchokera ku Genesis mpaka ku Chibvumbulutso.

VESI YOGOTSOGOLERA

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti tikakonzedwe pa makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10).

MAU OYAMBA

Gawo loyamba la maphunzirowa tinaona m'mene masomphenya amayambira ndi ndondomeko za kubadwitsa masomphenya a Mulungu ndi kuona dziko lapansi mmene Mulungu amalionera.

Chaputala ichi chimakhudzana ndi “Kuganiza Mozama,” – ndondomeko yachiwiri mu Ndongomeko za Kholola Wauzimu. Chaputalachi, chikufotokoza cholinga chakuseli kwa masomphenya auzimu. Kuonjezera apo “Kuganiza Mozama” ndi mutu umene umalumikizitsa dziko lapansi m'Mau a Mulungu omwense amabvumbulutsa cholinga cha dziko lonse lapansi.

CHOLINGA CHA MULUNGU

Kuchokera pachiyambi Mulungu wakhala ali ndi cholinga chimene amachitsata pa ubale wake ndi munthu angakhale pokwaniritsa malonjezano ndi ma uneneri okhudza munthu.

Mulungu waulula zolinga zake kwa okhulupliira:

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti tikakonzedwe pa makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)

Cholinga cha Mulungu kuchokera pachiyambi chakhala chofuna kuyanjanitsa kumwamba ndi dziko lapansi kudzera mwa Khristu Yesu. Awa ndiwo masomphenya ake okhudza dziko lonse lapansi...

Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (Petro 3:9)

Cholinga cha Mulungu ndiko kupulumutsa dziko lonse lapansi. Chifukwa chakuti ichi ndi cholinga cha Mulungu, chiyeneranso kukhala cholinga chathu. Kotere kuti tiyenera kuika patsogolo cholinga cha Mulungu pa dziko lonse lapansi.

Pali zosowa zambiri zimene dziko lapansi likukumana nazo monga, umphawi, matenda, njala ndi zina zambiri. Chifukwa cha zinthu izi, anthu ofalitsa Uthenga Wabwino ochokera maiko ena akhala akutengapo mbali. Iwo amachita izi pakuzindikira zomwe Baibulo limaphunzitsa pa zinthu zimenezi.

Koma sitiyenera kuiwala kuti masomphenya akholola lauzimu ndi wofunika kwambiri ndipo ayenera kukhala pamtima pathu. Kuthandiza zinthu zakuthupi kubwere titatha kupanga gulu la anthu ophunzira.

Ntchito ya mishoni imakhudza magawo onse amoyo koma tisayiwale kuti kholola lauzimu lobweretsa anthu kwa Mulungu ndiye chinthu choyamba komanso chofunika kwambiri.

CHIPANGANO CHATSOPANO

Cholinga cha Mulungu chikuoneka kuyambira ku Genesis mpaka buku la Chibvumbulutso ndipo mau ake ndi mbiri ya m'mene wakhala akuchitira ndi anthu komaso maiko pofuna kukwaniritsa malingaliro ake.

Kuitanidwa kwakukulu kunaperekedwa koyamba pamene Mulungu anena kwa Adamu ndi Hava kuti:

Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, Mubalane, mucuruke, mudzaze dziko lapansi, muligonjetse: mulamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakukwawa pa dziko lapansi. (Genesis 1:28)

Adamu ndi Hava amayenera kudzada dziko lapansi poberekana. Iwo analengedwa mu chifanizo cha Mulungu, ndipo anali pa ubale ndi Mulungu. Kuthupi, iwo amayenera kubereka ana ndipo kuuzimu amayenera kubereka okhulupilira. Patapita nthawi, Mulungu anakhazikitsa pangano lamuyaya ndi Abrahamu. Pangano limeneli linali lokhudza anthu onse a dziko lonse lapansi ndipo anati:

m'mbeu zako mitundu yonse ya dziko lapansi idzadalitsidwa: cifukwa wamvera mau anga. Ndipo mwa mbeu yako mabanja onse a dziko lapansi adzadalitsika (Genesesi 22:18).

Kudzera mwa Abrahamu Mulungu anadzutsa mtundu wa Israyeli. Mulungu anagwiritsa nchito Israyeli ngati mboni yake kwa anthu amitundu ndi maiko ena ozungulira. Maiko onse a dziko lapansi anadalitsika kudzera mwa Israyeli.

Mu nthawi imene Mulungu anatumiza miliri kwa Aiguputo, Mulungu anauza Farao kuti Iye anaponya miliri pa Aigupto kuti iwo akadziwe Mulungu ali pamwamba pa milungu yonse.

Pakuti nthawi yino ndidzatuma miliri yanga yonse pamtima pako, ndi pa anyamata ako, ndi pa anthu ako; kuti udziwe kuti palibe wina wonga Ine pa dziko lonse lapansi (Eksodo 9:14).

Pamene Israyeli adachita kakasi kuti awoloka bwanji mtsinje wa Yorodani, Mulungu anaumitsa madzi kuti anthu a dziko lonse lapansi akazindikire mphamvu yake.

Yoswa 4:24 kuti mitundu yonse ya pa dziko lapansi lidziwe dzanja la Yehova, kuti ndilo lamphamvu; kuti liope Yehova Mulungu wanu masiku onse.

Pamene Davide adakumana ndi Goliati kuti achite nkondo, Mulungu analonjeza kuti adzapereka chipambano kwa Davide kuti dziko lapansi lidziwe kuti kuli Mulungu.

Lero lino Yehova adzakupereka iwe m'dzanja langa, ndipo ndidzakukantha, ndi kukucotsera mutu wako. Ndipo lero ndidzapatsa mitembo ya makamu a Afilisti kwa mbalame za mlengalenga, ndi kwa zirombo za dziko lapansi; kuti dziko lonse likazindikire kuti kwa Israyeli kuli Mulungu (1 Samueli 17:46).

Ufumu wa Israyeli utakhazikitsidwa, anamvetsetsa malingaliro a Mulungu a dziko lonse lapansi. Ndipo anati:

ndipo akabwerera kwa Inu ndi mtima wao wonse ndi moyo wao wonse, m'dziko la adani ao adawatenga ndendewo, ndipo akapemphera kwa Inu molunjika ku dziko lao munapatsa makolo awo, ku mudzi munausankha Inu, ndi kunyumba ndamangira dzina lanu; (Mafumu 8:48)

Mfumu Davide inayitanira anthu kuminda ya dziko lapansi pamene anafuula nati:

Fotokozerani ulemerero wace mwa amitundu; Zodabwiza zace mwa mitundu yonse ya anthu. (Masalmo 96:3)

Fotokozerani ulemerero wace mwa amitundu; Zodabwiza zace mwa mitundu yonse ya anthu. Nenani mwa amitundu, Yehova acita ufumu; Dziko lokhalamo anthu lomwe likhazikika kuti silingagwedezeke; Adzaweruzwa mitundu ya anthu molunjika. (Masalmo 96:3,10)

Aneneri awiri a Chipangano Chakale, Danieli ndi Yona anatumikira anthu amene sanali a mtundu wawo. Daniel anatumikira Mulungu pamene amagwira ntchito ku Babulo pamene Yona anatumikira ngati mtumwi ku dziko la Nenevi.

Mneneri Yesaya analengeza kuti Israyeli ndiye kuunika kapena mboni ya Mulungu kwa anthu amitundu.

Amitundu onse asonkhane pamodzi, ndi anthu aunjikane; ndani mwa iwo anganene

ici ndi kuonetsa ife zinthu zakale? atenge mboni zao, kuti abvomerezeke ndi olungama; pena amve, nanene zoonadi. Inu ndinu mboni zanga, ati Yehova, ndi mtumiki wanga, amene ndakusankha; kuti mundidziwe, ndi kundikhulupilira Ine, ndi kuzindikira, kuti Ine Ndine; ndisanakhale Ine, panalibe mulungu wolengedwa, ngakhale pambuyo panga sipadzakhala wina. Ine, Inetu ndine Yehova; ndipo palibe Mpulumutsi, koma Ine ndekha. (Yesaya 43:9-11)

Chipangano Chakale chonse ndi mbiri ya Mulungu m'mene anagwiritsira ntchito Israel kukhala kuunika kwa anthu amitundu yonse ya dziko lapansi. Ndipo Chipangano Chakale chimawonetsera malingaliro a Mulungu pofuna kuti akamudziwe Iye mu choonadi.

CHIPANGANO CHATSOPANO

Chipangano Chakale chinakonzekeretsa kukwaniritsidwa kwa malingaliro a Mulungu kudzera mu malonjezano akubwera kwa Yesu Khristu. Ndipo Chipangano Chatsopano chimafotokoza zakukwanirisiwa kwa dongosolo la Mulungu kudzera mu utumiki wa Yesu Khristu. Yesu anauza ophunzira ake za masomphenya auzimu powauza kuti:

Yesu ananena nao, Cakudya canga ndico kuti ndicite cifuniro ca iye amene anandituma Ine, ndi kutsiriza nchito yace. (Yohane 4:34)

Moyo wa Yesu khristu unakhazikika pakuchita kholola la amayi ndi abambo ndikuwakokera ku ufumu wa Mulungu.

Koma anati kwa iwo, Kundiyenera Ine ndilalikire Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ku midzi inanso: cifukwa ndinatamidwa kudzatero. (Luka 4:43)

Pamene Yesu anakwera kumwamba, anatisiyira ntchito kapena Kutumidwa Kwakukulu kumene kukutilamula kuti tikachite kholola lauzimu. Ndipo izi zalembedwa mabuku osiyanasiyana mu Chipangano Chatsopano.

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse.....ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya panso pano. (Mateyu 28:18-20)

Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa. Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:15-18)

Ndipo anawatsegulira mitima yao, kuti adziwitse malembo; ndipo anati kwa iwo, Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacityatu; ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. 11 Inu ndinu mboni za izi. Ndipo onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera Kumwamba (Luka 24:45-49).

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko (Macitidwe 1:8).

Ndiudindo wathu ngati okhulupilira kukwaniritsa zolinga za Mulungu pakuti ndife mboni zake ku maiko onse a dziko lapansi.

Buku la Machitidwe a Atumwi limafotokoza za chiyambi cha mpingo woyamba. Ndipo mutu waukulu mu bukuli ndi “mudzakhala mboni zanga” (**Mach 1:8**) ndipo izi zimaoneka mu Buku lonse la Machitidwe:

Kulalikira kwa Ayuda 1:1-8:3

Kulalikira kwa Ayuda ndi Amitundu Acts 8:4-12:25

Kulalikira kwa Amitundu Acts 13:1-28:31

Mpingo woyamba unabadwa pakuonetsa mphamvu ya Mulungu ndipo izi tikuziona pa Machitidwe 2 pamene Mulungu akupanganso gulu lina la anthu omutsata kudzera mu mpingo umene umayenera kupita kudziko lonse lapansi.

Ndi kuwalitsira onse adziwe makonzedwe a cinsinsico, cimene cinabisika ku yambira kale kale mwa Mulungu wolenga zonse; kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu (Aefeso 3:9-10).

Dongosolo la Mulungu ndi lakuti Iye apulumutse anthu ake onse mwa Yesu Khristu kudzera ku mpingo ndipo izi zidziwike kwa anthu onse a dziko lapansi.

Makalata a m'Chipangano Chakale amafotokoza za maudindo, dongosolo komanso mwayi umene anthu amene ali mumpingo ali nao. Mpingo umene unali ndi dongosolo labwino komanso umene umawonetsera mphamvu ya Mulungu ndi umene umayenera kugwira ntchito ya kholola lauzimu pa dziko lapansi.

M' buku la Chibvumbulutso mutu 1 mpaka 3, Yohane akufotokoza makhalidwe a mipingo ya nthawi imeneyo. Ndipo ndimezi zikupereka chithunzithunzi cha m'mene zinthu zinalili nthawi imeneyo.

Ina mwa mwipingo imene ikukambidwa inaiwala cholonga chao, moyo wauzimu wa mipingo unali ozizira komanso opanda mphamvu. Angakhale zinthu zinali choncho, malingaliro a Mulungu sikuti anasintha konse ayi.

Taona, ndaima pakhomu, ndigogoda; wina akamva mau anga nakatsegula pakhomu, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine. (Cibvumbulutso 3:20)

Kwa anthu onse amitundu yonse, maiko onse ndi zinenero zonse. Cholinga cha Mulungu chofuna kudzibvumbulutsa kuchokera pachiyambi sichinasinthe; cholinga chake ndi chomwe chija.

Harvestime International Institute imaphunzitsa mphunziro lina limene limatchedwa “**Kukuza Kaonedwe ka Znthu mwa Umulungu**”. Phunziroli limafotokoza mwa tsatane-tsatane zolinga za Mulungu pa maiko a dziko lonse lapansi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi ya pamtima

Lembani “T” ku mayambiliro kwa chiganizo chimene chili cholondola ndipo lembani F ku mayambiliro kwa chiganizo chimene sicholondola.

1. _____Mulungu sanabvumbulutse zolinga zake kwa munthu
2. ____Cholinga cha Mulungu ndi kuyanjanitsa zinthu zonse kudzera mwa Khristu Yesu.
3. ____Mu Chipangano Chakale, Mulungu anagwiritsa nchito Israyeli kuti akhale kuunika kwa anthu amitundu ina.
4. ____Mu Chipangano Chatsopano, mpingo ndi gulu la anthu amene Mulungu akufuna kuwagwiritsa ntchito kuti akafalitse Uthenga Wabwino

Kodi cholinga cha Mulungu ndi chani ndipo pelekani zitsanzo kuchokera mu Baiburo kuchitira umboni yankho lanu.

ZOPHUNZIRA ZOONJEZERA

1. Werengani buku la Chibvumbulutso mutu 1-3 pamene akufotokoza za uthenga wa Mulungu ku mipingo isanu ndi iwiri.
2. Tchulani m’ndandanda wa makhalidwe a mipingo imene Mulungu inaiyamikira ndipo fokotokozani m’mene khalidwe la mipingo mwatchulayo linathandizira kufalitsa Uthenga Wabwino.

3. Tchulani m'ndandanda wa mavuto amene Mulungu anawapeza mu mipingo imene mwawerengayi, ndipo kodi mavuto amenewa angalepheretse bwanji mpingo kukwaniritsa cholinga chake chokhala mboni ya Mulungu ku maiko onse a dziko lapansi?
4. Pitolizani kuona dziko lapansi mu mau a Mulungu ndipo pamene muwerenga Baibulo, muone cholinga cha Mulungu pa anthu onse adziko lapansi.
5. Pezani ma vesi a mu Baiburo amene akufotokoza machitachita a Mulungu onse ndi anthu onse adziko lapansi.

Gwiritsani nthchito cholemba kapena pensulo kuti mudure nzere kungsi kwa mau awa mu Baibulo lanu.

- Dziko
- Dziko lapansi
- Maiko
- Amitundu
- Achikunja

GAWO LACHITATU: KUPEZA ZOLINGA
ZOLINGA ZOKWANIRITSIRA MASOMPHENYA ANU

CHAPUTALA 5

MINDA YOPANDA KANTHU NDI ZIKWAKWA ZOSATHWA

(Zoleperetsa Kholola la Uzimu)

ZOLINGA

Pamapeto a phunziro ili, muyenera kukwanitsa kuchita izi:

1. Kupeza zinthu zimene zimalpheretsa kholola ku dziko lakuthupi.
2. Gwiritsani ntchito mfundo za kholola lakuthupi kukholola la kuuzimu.

VESI YOTSOGOLERA

Musanyengedwe; Mulungu sanyozeka; pakuti cimene munthu acifesa, cimenenso adzaciduta. Pakuti wakufesera kwa thupi la iye yekha, cocokera m'thupi adzatuta cibvundi; koma wakufesera kwa Mzimu, cocokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha (Agalatiya 6:7-8).

MAU OYAMBA

Gawo loyamba la maphunzirowa limakamba za kholola lauzimu ndipo gawo lachiwiri limafotokoza za zolinga za masomphenya auzimu. Koma mu gawo ili, tiona dongosolo limene lingathandize kuti tikwaniritse masomphenya auzimu.

Muchaputala chimenechi tiona zinthu zimene zimapangitsa kholola lauzimu kuchepa. Kudziwa zofunika kupewa pochita kanthu kena kake nkofunika kwambiri molingana ndi kudziwa kachitidwe ka chinthucho.

Mkulu wina otchedwa Edison Thomas amene anaymbitsa nyali za magesi, iye anayesa ka 1500 kufikira pamene anakwaniritsa kupanga nyali zamagetsi. Ndipo iye atafunsidwa za izi anayankha nanena kuti “ndapeza njira 1500 zolakwika pa pakangidwe ka nyali za magetsi. Kotero kuti izi zidamuthandizira kuti asadzaonongeso nthawi yake pogwiritsa ntchito njira zolakwika zimenezi.

Inuyo simukuyenera kuyeselera kholola lauzimu chifukwa Mulungu wapeza kale njira zolakwika zimene zimachepetsa kholola lauzimu. Ndipo nkoyenera kumvetsa mfundo zimenezi kuti musataye nthawi yanu ndi njira zolakwikazi.

M'machaputala awiri akubwerawa tiona ndondomeko za kholola, mfundo kapena ndondomeko zothandiza pa zokolola zochulukana.

MFUNDO YA “NGATI-KOMA”

Mfundo ya “ngati-koma” ndiyofunika kwambiri m’Mau a Mulungu. Mulungu anapereka malonjezano ake ambiri kwa anthu ake ndipo ambiri mwa malonjezano amenewa inakhazikika pa mfundo ya “ngati-koma” Deuteronomo 28 ndi chitsanzo chimodzi cha mfundo imeneyi.

Ndipo kudzali, mukadzamvera mau a Yehova Mulungu wanu mwacangu, ndi kusamalira kucita malamulo ace onse amene ndikuuzani lero, kuti Yehova Mulungu wanu adzakukulitsani koposa amitundu onse a pa dziko lapansi (Deuteronomo 28:1).

M’ndime ya pamwambayi, Mulungu akufotokoza madalitso amene anthu ake adzalitsidwa nao ngati adzamtumikira Iye. Limodzi la malonjezano amenewa ndilo kukolola za kumunda zochuluka kwambiri.

Zidzakhala zodala zipatso za thupi lanu, ndi zipatso za nthaka yanu, ndi zipatso za zoweta zanu (Deuteronomo 28:3-4).

Koma vesi 15 ikupeleka chenjezo:

Koma kudzali, mukapanda kumvera mau a Yehova Mulungu wanu, kusamalira kucita malamulo ace onse ndi malemba ace amene ndikuuzani lero, kuti matemberero awa onse adzakugwerani ndi kukupezani (Deuteronomo 28:15).

Limodzi mwa matembelero a kusamvera Mulungu ndi zokolola za kumunda zochepe.

Mudzakhala otembereredwa m'mudzi, ndi otembereredwa pabwalo. Zidzakhala zotembereredwa zipatso za thupi lanu, ndi zipatso za nthaka yanu, zoswana za ng'ombe zanu, ndi zoswana za nkhosa zanu.

Mudzaturuka nazo mbeu zambiri kumunda, koma mudzakolola pang'ono; popeza dzombe lidzazitha. Mitengo yanu yonse ndi zipatso za nthaka yanu zidzakhala zao zao za dzombe (Deuteronomo 28:16, 18, 38-42).

Chaputala 28 cha Deuteronomo chikuonetsera mfundo ya “ngati-koma”. Malonjezano a Mulungu amatengera mmene ife tachitira ndi malamulowo.

ZITSANZO ZOFANANA ZA KUTHUPI NDI ZAUZIMU

Baibulo limafokotoza mfundo zimene zingabweretse zokolola zochuluka za kumunda, komanso limachenjeza kuti zokolola zikhoza kukhala zochepe ngati mfundo zimenezi sizitsatidwa. Komanso mfundozi zimagwiranso ntchito ku kholola lauzimu.

Kumvetsetsa mfundo kukhoza kuthandiza kuti tikwaniritse kufalitsa Uthenga Wabwino ku dziko lonse lapansi komanso mfundozi zikhoza kuthandiza ku gawo lililonse la moyo wathu monga nkhani zachuma ndi zina zambiri.

CHOLINGA CHA SATANA PA KHOLOLA

Satana nayenso ali ndi cholinga pa kholola. Yesu analakhula kwa Petro:

Satana amafuna akupete iwe ngati tirigu (Luka 22:31).

Cholinga cha satana ndikutenga zonse zabwino zimene zili mwa inu ndi cholinga choti mungotsala ndi zinyalala zokhazokha.

Kuti timvetse njira zimene satana magwilitsa ntchito pofuna kutibera zokolola zamoyo wathu, Mulungu anachenjeza za zinthu zimene zimalepheretsa kholola lauzimu. Ndipo kuti tikwaniritse kholola lauzimu nkoyenera kuti tichotse zinthu zimene zimatilepheretsa kholola lauzimu pa moyo wanu.

Kuthana ndi zinthu zolepheretsazi kuli ngati kugalauza m'munda pokonzekera kuti mudzale mbeu. Nthaka iyenera kukonzedwa pochotsa zinthu ngati tchire komanso kuphwanya zibuma ndi cholinga choti nthakayo ilandire mbeu.

ZIFUKWA ZOBWERETSA KHOLOLA LOCHEPA

Zina mwa zifukwa zopangitsa kholola lochepa ndi izi:

KUSAMVERA MAU A MULUNGU

Ndime tinanawerenga kuchokera ku Deuteronome ikuonetsera chimodzi mwa zifukwa zopangitsa kholola lochepa. Mulungu analonjeza zokolola zochuluka kwa anthu ake ngati amvera Iye, ndipo ngati samvera, zokolola zao zidzakhala zochepa.

Mneneri Yesaya anafotokoza za munda wa mphesa wa Mulungu. Chifukwa cha kusamvera Mau a Mulungu, Israyeli samabala zipatso. Ndipo ngati simumvera Mulungu, izi zimabweretsa chilala chazimu.

Taonani, akudza masiku, ati Ambuye Yehova, akuti ndidzatumiza njala m'dzikomo, si njala ya mkate kapena ludzu la madzi, koma njala ya kumva mau a Yehova. Ndipo adzayendayenda peyupeyu kuyambira kunyanja kufikira kunyanja ndi kuyambira kumpoto kufikira kum'mawa; adzathamangathamanga kufunafuna mau a Yehova, koma osawapeza (Amosi 8:11-12).

KUIWALA MULUNGU

Kuyiwala Mulungu ndi kusampatsa Mulungu malo oyenera m'moyo wathu kapena kum'chotsa Mulungu m'moyo wathu.

Cifukwa iwe waiwala Mulungu wa cipulumutso cako, sunakumbukira Thanthwe la mphamvu zako; cifukwa cace iwe waoka mitengo yokondweretsa, waokapo zipinjiri zacilendo; tsiku lako looka uzingapo mpanda, nuphukitsa mbeu zako m'mawa mwace; mulu wa masika udzaoneka tsiku lakulira ndi la cisoni cothetsa nzeru. (Yesaya 17:10-11)

Sizokwanira kungodziwa zinthu za Mulungu, koma nkofunika kumudziwa Mulungu. Tikuyenera kudziwa malingaliro ake pamoyo wathu komanso ndi kumulora kuti alamulire moyo wathu.

Ngati simumpatsa Mulungu mpata m'moyo wanu, mukhoza kugwira ntchito usiku ndi usana opanda chopindula, kapena opanda kholola lililonse lauzimu ndipo Israel ndichitsanzo chabwino cha anthu amene anamuiwala Mulungu.

Koma anaiwala nchito zace msanga; Sanalindira uphungu wace: Anaiwala Mulungu mpulumutsi wao, Amene anacita zazikulu m'Aigupto (Masalmo 106:13, 21).

Chifukwa cha kusamvera, Israyeli akhudzidwa kuthupi ndi kuuzimu komwe. Koma pamene ambiri amaiwala Mulungu, iwo samazindikira kuti izi zimachepetsa zokolola zao, zakumunda ndi zakuthupi zomwe.

Adzadya zokolola zako, ndi mkate wako, adzadya nkhusa zako ndi zoweta zako; adzadya mphesa zako ndi nkhuu zako; adzapasula ndi lupanga midzi ya malinga yako, imene ukhulupiliramo. Koma masiku onsewo, ati Yehova, sindidzatsirizitsa konse ndi iwe. Ndipo padzakhala: pamene mudzati, Cifukwa canji Yehova Mulungu wathu aticitira ife zonse izi? ndipo udzayankha kwa iwo, Monga ngati mwandisiya Ine, ndi kutumikira milungu yacilendo m'dziko lanu, momwemo mudzatumikira alendo m'dziko siliri lanu (Yeremiya 5:17-19).

Amosi akufotoza momveka bwino zifukwa za zokolola zochepa mu chaputal 4 ndi 5 mu buku la Amosi.

Ndipo Ine ndakumanani mvula, itatsala miyezi itatu isanafika nyengo ya kukolola; ndipo ndinabvumbitsira mudzi umodzi mvula, osabvumbitsira mudzi wina; munda wina unabvumbidwa mvula, ndi m'munda mosabvumbidwa mvula munafota. (Amosi 4:7)

Ndinakukanthani ndi cinsikwi ndi cinoni; minda yanu yocuruka yamipesa, ndi yamikuyu, ndi yaazitona, yaonongeka ndi cirimamine; koma simunabwerera kudza kwa Ine, ati Yehova. (Amosi 4:9)

Koma Amosi atatha kupeza bvuto, akuperekanso yankho lake.

mundifunefune ine ndipo mudzakhala ndi moyo (Amos 5:4)

KUFESA KOSAYENERA

Mulungu anawachenjeza anthu ake:

Musamabzala mbeu zosiyana m'munda wanu wamphesa, kuti zingaipeidwe mbeu zonse udazibzala, ndi zipatso za munda wamphesa zomwe. (Deuteronomo 22:9)

Cifukwa iwe waiwala Mulungu wa cipulumutso cako, sunakumbukira thanthwe la

mphamvu zako; cifukwa cace iwe waoka mitengo yokondweretsa, waokapo zipinjiri zacilendo; tsiku lako looka uzingapo mpanda, nuphukitsa mbeu zako m'mawa mwace; mulu wa masika udzaoneka tsiku lakulira ndi la cisoni cothetsa nzeru (Yesaya 17:10-11).

M'ndimeyi Mulungu akukamba za mbeu zosakanikirana, zikhoza kuoneka ngati zikukula koma zokolola zake zimakhala zotembeleredwa. M'Chipangano Chatsopano, mbeu imatchedwa Mau a Mulungu. Ndipo zimene mumafesa zimakhudza moyo wanu. Ngati mwafesa Mau a Mulungu, mumatuta kapena kukolola zambiri.

Ngati mumaona ngati zikhalidwe za anthu, mipingo kapena kachitidwe ka zinthu kukhala kofunika kwambiri kuposa Mau a Mulungu, ndekuti mukusakaniza mbeu. Mipingo yambiri imaoneka ngati ndi ya mphamvu chifukwa chakuti ili ndi anthu ambiri kapena mwinanso chikukwa chakuti ali ndi nyumba zopempheleramo zokongola. Koma chifukwa chakuti aphantikiza zikhalidwe za mpingo wao ndi Mau a Mulungu, mbeu zao zimakhala zotembeleredwa. Izi ndi zimene zimabweretsa mipingo yophunzitsa ziphunzitsa zonyenga, ndipo izi zimabweretsa kholola lokhumudwitsa.

Mau a Mulungu ndi mbeu yamphumphu imene imabweretsa kholola lakubadwanso mwatsopano mkati mwa amy ndi abambo.

Inu amene mudabadwanso, osati ndi mbeu yofeka, komatu yosaola, mwa Mau a Mulungu amoyo ndi okhalitsa (1 Petro 1:23).

KUSALABADIRA

Buku la Miyambo limakamba za mwana amene amagona nthawi yokolola

.... Koma wogona pakututa ndi mwana wocititsa manyazi. (Miyambi 10:5)

Nthawi ya kholola ndi nthawi yotanganidwa; ndi nthawi yofunika kwambiri chifukwa ngati zokololazo sizichotsedwa msanga m'munda zikhoza kuonongekera m'munda momwemo. Munthawi ya Baibulo, ikafika nthawi yakholola, wina aliyense amatengapo gawo kotere kuti mwana wogona nthawi yakholola anali wochititsa manyazi ku banja lake.

Tikukhala munthawi yofunika kwambiri ya kholola lauzimu chifukwa Yesu watsala pang'ono kubwera koma ana a Mulungu akugonabe; sanagwirane manja ndi okhulupilira amene ali m'munda. Zikwakwa zao zinachita dzimbiri komanso m'munda mwao mulibe kanthu.

Buku la Miyambo limakamba zotsatira zowonetsera kukhudzika:

Ndinapita pa munda wa mlesi, Polima mphesa munthu wosowa nzeru. Taonani,ponsepo panamera minga, Ndi kuwirapo khwisa; Chinga lace lamiyala ndi kupasuka. Pamenepo ndinayang'ana ndi kuganizira, Ndinaona ndi kulandira mwambo. Tulo tapang'ono, kungoodzera pang'ono, Kungomanga manja pang'ono m'kugona, Ndipo umphawi wako udzafika ngati mbala; Ndi kusauka kwako ngati munthu wacikopa. (Miyambi 24:30-34)

Kusakhuzika kumabweretsa kusabala zitpatso ndipo Yeremiya analakhulapo za atsogoleri amene amaononga kholola chifukwa chakusasamala:

Abusa ambiri aononga munda wanga wamphesa, apondereza gawo langa, pondikondweretsa apayesa cipululu copanda kanthu. Apayesa bwinja; pandilirira ine, pokhala bwinja; dziko lonse lasanduka bwinja; cifukwa palibe munthu wosamalira (Yeremiya 12:10-11).

Utsogoleri wosasamala kapena kukhudzika umapangitsa otsatira kuti akhalenso osakhakulupirika. Izi ziri chomwechi chifukwa atsogoleri ali ndi udindo wofotokozera anthu awo zakholola la uzimu.

KUYESA MWA IFE TOKHA

Sitingabweretse kholola lauzimu ndi mphamvu kapena nzeru zathu. Kuyesa patokha kumabweretsa zinthu izi:

Tsiku lako looka uzingapo mpanda, nuphukitsa mbeu zako m'mawa mwace; mulu wa masika udzaoneka tsiku lakulira ndi la cisoni cothetsa nzeru (Yesaya 17:11).

Mu chaputala choyamba, tinaona kuti masomphenya auzimu samatheka ndikuthekera kwathu kapena kuyesa kwathu. Njira yokhayo yokwaniritsira masomphenya auzimu ndikugwiritsa ntchito ndondomeko zimene Mulungu mwini wapereka zakholola lauzimu.

Hoseya anafotokoza bvuto la kholola lochepa limene limabwera chifukwa chakuyesayesa tokha. Mwachitsanzo, Israyeli amadzidalira yekha osati Mulungu. Ngati mungadalire nzeru zanokha komanso anthu anu owoneka amphamvu, kudzakhala kovuta kukwaniritsa masomphenya auzimu. Nchito ya Mulungu iyenera kwugwiridwa m'mene Mulungu akufunira (Hosea 10:13).

KUTEMBELEREDWA KWA ZINTHU ZONSE ZOBALA

Chotsatira chimodzi chimene chinadza chifukwa cha tchimo kunali kutembeleredwa kwa zinthu zonse zimene zimabeleka. Mzimayi, chifukwa cha tchimo, anatembeleredwa kotere kuti amayenera kumva kuwawa pobereka. Angakhale nthaka imene imamera ziyangoyango ndi minga kotero kuti zimatenga mphamvu zambiri kuti nthaka ibale zipatso. Ndipo kutembeleredwa kwa zinthu zonse za chilengedwe ndi chifukwa cha tchimo (Genesis 3:16-19).

Pa moyo wathu wauzimu, ngati mukukhala mu tchimo pamakhala tembelero limene limakhudza moyo wathu wauzimu. Ndipo izi zimatengera mwazi wa Yesu Khristu yekha basi kuti thembelero limeneli lichoke basi. Mkosatheka kukhala ndi m'dalitso wa kholola lauzimu ngati tikuyendabe muuchimo chifukwa mukhala mukuyendabe mu thembelero latchimo.

KUYANG'ANIRA NYENGO ZAMOYO

Nyengo zathu zamoyo zikhoza kulepheretsa kholola lauzimu.

Wolesi salima cifukwa ca cisanu; Adzapemphapempha m'masika osalandira

kanthu (Miyambi 20:4)

**Woyang'ana mphepo sadzafesa; ndi wopenya mitambo sadzakolola.
(Mlaliki 11:4)**

Kudziko lakuthupi, ngati mlimi angadikire nthawi yabwino, sangafese kapena kukolola kumene. Tsono posatengera nyengo, kaya kutetha kaya mitambo, mlimi amakhala akugwira ntchito kumunda.

Angakhale m'moyo wauzimu, tikadikira nthawi yabwino kuti tikachite kholola lauzimu, palibe chimene chingachitike chifukwa mavuto athu a tsiku ndi tsiku monga kusowa kwa ndalama chikhoza kukhala chinthu zolepheretsa kuti tikachite kholola lauzimu. Pa chifukwa ichi, sitikuynera kulabadira kwambiri mavuto athu ngati tikufuna kholola lauzimu.

KUSALUNJIKI PAKUCHITA ZINTHU

Mukhoza kutaya nthawi yanu yonse kugwira ntchito zina osati ntchito ya Mulungu.

Pakuti abzala mphepo, nadzakolola kabvumvulu; alibe tirigu wasasenga; ngala siidzaturutsa ufa; cinkana iuturutsa, alendo adzaumeza. (Hoseya 8:7)

Pali zinthu zambiri zabwino kuzichita ndipo inu mukhoza kuononga nthawi yanu kuchita zithu monga zimenezi. Koma kuti mukakwaniritse kholola lauzimu, ntchito zabwino zokha sizokwana. Yesu Khristu anati:

Yesu ananena nao, Cakudya canga ndico kuti ndicite cifuniro ca iye amene anandituma Ine, ndi kutsiriza nchito yace. (Yohane 4:34)

Chinsisi cha kholola lauzimu ndikusatanganidwa kuchita ntchito zachifundo zokha ayi koma kugwiranso ntchito ya Mulungu malingana ndi zolinga zake za Mulunguyo. Kupanda kutero ndiye kuti mbeu yathu ikhala ngati yofesedwa mu mphepo ndikuulitsidwa, mbeu imeneyi simabala.

MATENDA NDI TIZILOMBO

Kudziko lakuthupi, kuli matenda ndi tizilombo zimene zimagwira zomera ndi kuziononga. Tizilombo ndi zinthu zimene zimaononga kunja kwa chomera, monga dziwala dzimatha kuononga mbeu. Koma matenda amalowa mkati mwa mbeu ndi kuiononga.

Okhulupiliranso amakumana ndi tizilombo ndi matenda. Satana amalimbana nafe kudzera munyemga zathu za kuthupi ndipo izi zimakhudza maganizidwe athu mkati mwathu.

Alimi amazindikira kufunika kwa kudilira mitengo yazipatso podula nthambi zosefukira. izi zimathandiza kuti zipatsozo zibale kwambiri. Izi ndizofunikiranso m'moyo wa anthu okhulupilira. Pali zinthu zambiri zimene zimachokera mkati mwathu zimene zimalepheretsa kuti tikabale zipatso zambiri (Mariko 7:15) ndipo Mulungu amadulira zinthu zimenezi ndikuti tikabale zipatso zambiri. Yohane akufotokoza mmene ndondomeko imeneyi imayendera.

Vuto lenileni la tizilombo ndi matenda auzimu ndi zinthu zimene timakumana nazo kapena m'mene timaganizira. Vuto lenilenei lagona pa mphamvu zimene zili kuseri kwa nyengo zathu.

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba (Aefeso 6:12).

Kudziko la kuthupi, zomera zikagwida ndi matenda ndi tizirombo, mankhwala amagwiritsidwa ntchito pofuna kupha tiziromboti. Ku dziko lauzimu, zida za Mulungu ndi zimene zimateteza kholola lauzimu pa moyo wathu.

Mwa ici mudzitengere zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoza kuima citsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutacita zonse, mudzacirimika.

Cifukwa cace cirimikani, mutadzimangira m'cuuno mwanu ndi coonadi, mutabvalanso capacifuwa ca cilungamo; ndipo mutadzibveka mapazi anu ndi makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere; koposa zonse mutadzitengeranso cikopa ca cikhulupiriro, cimene mudzakhoza kuzima naco mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo. Mutengenso cisoti ca cipulumutso, ndi lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu (Aefeso 6:13-17).

KUFESA MOLAKWIKWA

Kufesa molakwikwa kumaononga mbeu.

Kodi mlimi amalimabe kuti abzale? kodi amacocolabe, ndi kuswa zibuma za nthaka? Atakonzatya pamwamba pace, kodi safesa ponse mawere, ndi kumwazamwaza citowe, nafesa tirigu m'mizere ndi barele m'malo ace osankhika, ndi mcewere m'maliremo?

Pakuti Mulungu wace amlangiza bwino namphunzitsa. Pakuti sapuntha mawere ndi copunthira cakuthwa, ngakhale kuzunguniza njinga ya gareta pacitowe; koma amakulunga mawere ndi munsu, naomba citowe ndi cibonga.

Tirigu wa mkate aperedwa; pakuti samampuntha osaleka; ngakhale kuyendetsapo njinga ya gareta wace, ngakhale kumphwanya ndi ziboda za akavalo ace sapersa. (Yesaya 28:24-28)

Pali njira zambiri zoyenera zokonzekera kudzala mbeu kumunda komanso njira zozdalira. Komanso pali njira zosiyana-siyana zokololera mbeu malingana ndi mbeu imene ikukololedwa.

Chimodzimodzi pamene tikukolera amai ndi abambo kuti abwere mu ufumu wa Mulungu, ena zimakhala zophweka kubwera kwa Mulungu pamena ena zimatenga nthawi kuti abvomereze kuti Yesu ndi Ambuye.

Njira zokololera mbeu zimaononga mbeuzo kotere kuti pamafunika nzeru zakakoledwe kabwino. Chimodzimodzi ndi kholola lauzimu, pamafunika nzeru zochokera kwa Mulungu.

NTHAKA YOSALIMIDWA

Ngati nthaka sikonzekeretsedwa bwino, zokolola zikhala zochepa. Werenga fanizo la ofesa mbeu ku buku la Mariko 4:12-20, Mateyu 13:1-23 ndi Luka 8:4-15. Mumafanizo amene, mau a Mulungu akufanizidwa ndi mbeu imene timadzala kumunda. Ndipo mbeuyi imadzalidwa m'mitima ya anthu.

Mwa mafanizo amenewa, pali chinthu chimodzi chimene chikukhudza mbeu, chinthu chimenechi ndiye dothi. Nthaka yina sinasamalidwe moyenera kotere kuti zokolola zake sizinachite bwino. Koma mbeu yogwera pa nthaka yabwino ikuyimira mitima yokonzeka kulandira mau a Mulungu ndipo zokolola zake zinali zochuluka.

Ndipo iwo ofesedwa pa nthaka yabwino ndiwo oterewa akumva mau, nawalandira, nabala zipatso zakupindula makumi atatu, ndi makumi asanu ndi limodzi, ndi makumi khumi. (Marko 4:20)

Anthu ena amakhala okonzeka kulandira Mau a Mulungu, pamene ena safuna kulandira. Chifukwa cha ichi, ngati simukukolola kholola lauzimu vuto likhoza kukhala kuti mwafesa pa dothi lopanda chonde kotere kuti yankho lake ndikungokonzaso dothilo mwadongosolo. Mneneri Hoseya anati:

Mudzibzalire m'cilungamo mukolole monga mwa cifundo; limani masala anu, pakuti yafika nthawi ya kufuna Yehova, mpaka afika Iye, nabvumbitsira inu cilungamo. Mwalima coipa, mwakolola cosalungama, mwadya zipatso za mabodza; pakati watama njira yako ndi kucuruka kwa anthu ako amphamvu (Hoseya 10:12-13).

Nthaka yosalungama ikufanana ndi maziko osalungama ku moyo wauzimu. Hoseya anafotokozerana ana a Israyeli kuti anakolola chosalungama pakuti anadzala chosalungama. Zotsatira zakufesa mbeu yachosalunga ndi izi:

Kusagwirizana

Mwamuna wamphulupulu amabweretsa kusagwirizana (Miyambo 6:12,14)

Kusalungama

Wofesa zosalungama adzakolola tsoka (Miyambo22:8)

Monga umo ndaonera, olimira mphulupulu nabzala bvuto, akololapo zomwezo. (Yobu 4:8)

Kulimbana

Munthu okhota amautsa makani (Miyambo 16:28)

Thupi:

Musanyengedwe; Mulungu sanyozeka; pakuti cimene munthu acifesa, cimenenso adzaciduta. Pakuti wakufesera kwa thupi la iye yekha, cocokera m'thupi adzatuta cibvundi; koma wakufesera kwa Mzimu, cocokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha. (Agalatiya 6:7-8)

Ndipo nchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, otetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenjezani nazo (Agalatiya 5:19-21).

Muyenera kukonza nthaka yanu yauzimu ndikuchotsa zonse zolepheretsa ngati tikufuna kukolola kholola lambiri lauzimu, tiyeneranso kufunafuna Mulungu mpaka iye atadza ndikuvumbitsa kulungama kwake mwa ife ngati mvula.

MAZIKO OSALUNGAMA

Pamene zokolola sizinachite bwino, mneneri Hagai adauza anthu kuti aunguzenso njira zao

Mwabzala zambiri, koma mututa pang'ono ... Mtima wanu usamalire njira zanu. (Hagai 1:6)

Anthu ake a Mulungu angakhale adafesa mbeu mokwanira, koma zokolora zawo zinali zomvetsa chisoni kotero kuti Hagai anawafotokozerana kuti ayenera kukonzaso njira zawo zakuthupi ndikuuzimu kuti akakolole zochulukana.

NDI CHIFUKWA CHIANI AMAYENERA KUMANGANSO?

Kuthupi, ana a Israyeli amazengereza kumanganso kachisi wa Yehova ndipo iwo anatanganidwa ndikumanga nyumba zao. Zofuna zao zinali patsogolo pamene zofuna za Mulungu anaziyika pambuyo.

Maziko a ana A Israyeli auzimu anali olakwikwa. Iwo amafesa ndikukolola kuuzimu ndi manja awo odetsedwa pamaso pa Mulungu.

.... Momwemo anthu awa, ndi momwemo mtundu uwu pamaso panga, ati Yehova; ndi momwemo nchito iri yonse ya manja awo; ndi ici acipereka, ciri codetsedwa. (Hagai 2:14)

Mulungu anauza Israyeli kuti, Nsembe yoyenera yoperekedwa ndi manja odetsedwa imakhala yodetsedwa pamaso pa Mulungu.

Ndipo Ine ndinakuoka mpesa wangwiro, mbeu yoona; kodi bwanji wandisandukira Ine mbeu yopanda pace, ya mpesa wacilendo? (Yeremiya 2:21)

Zokolola zimatembeleredwa ngati maziko anthu auzimu sali oyenera pamaso pa Mulungu.

Ndinakukanthani ndi cinsikwi ndi cinoni ndi matalala m'nchito zonse za manja anu, koma simunabwerera kudza kwa Ine, ati Yehova. (Hagai 2:17)

Chilichonse chimalakwikwa chifukwa cha za kusalungama. Mneneri Hagai anawatsimikizira ana a Israyeli kuti amayenera kumanga kuthupi ndi kuuzimu komwe kuti adalitsidwenso.

Musamalire, kuyambira lero ndi m'tsogolo, kuyambira tsiku la makumi awiri ndi cinai la mwezi wacisanu ndi cinai, kuyambira tsiku lija anamanga maziko a Kacisi wa Yehova, samalirani. Kodi mbeu ikali m'nkhokwe? Ngakhale mpesa, ndi mkuyu, ndi khangaza ndi mzitona sizinabala; kuyambira lero lino ndidzakudalitsani. (Hagai 2:18-19)

Kachisi atangoyambaso kumangidwa, Mulungu anagwetsanso mdalitso wake pa anthu ake koma maziko ake anali ungwiro wao wa moyo wauzimu. Pamene mungama maziko amoyo wanu mu choonadi ndi ungwiro, Mulungu amayambaso kudalitsa ndipo mudzakolola kholola lambiri m'moyo wanu.

Harvestime International Institute imapereka phunziro lina lotchedwa “Maziko a Chikhulupiliro.” Phuziroli limaona kufunika kwa maziko oyenera ku moyo wa chiKhristu. koma phunziroli ndi lalikulu kwambiri kotero kuti sitingafotokozere chilichonse mokwanira. Komabe ndikofunika kuti tione maziko oyenera obweretsa kholola lochuluka. Ena mwa maziko amenewa ndi awa:

Kumanga pa Thanthwe Lolimba

Iye afanana ndi munthu wakumanga nyumba, amene anakumba pansi ndithu, namanga maziko anyumbayo pathanthwe; ndipo pamene panadza chigumula, mtsinje unagunda pa nyumbayo, ndipo sunakhoza kuigwedeza, chifukwa idamangidwa bwino (Luka 6:48).

Tanthwe limenero ndi Yesu Khristu:

Palibeso tanthwe lina; ai sindidziwa liri lonse (Yesaya 44:8)

Maziko enieni amamangika pa choonadi.

Choonadi chenicheni chimakhala ndi maziko osatha (Miyambo 10:25).

Ndimaziko okoma:

Nadzikundikire okha maziko okoma..... (1 Timoteo 6:19)

Ndi maziko amuyaya:

Nadzikundikire okha maziko okoma ku nyengo ikudzayi, kuti akagwire moyo weni weniwo (1Timoteo 6:19),

Amamangigwa pa Mau a Mulungu:

Mau aMulungu amaima pokhazikika, ndipo palibe angawasuthe. (2 Timeteo 2:19)

Maziko a maima pa fundo ziwiri:

Koma maziko amane amaikidwa ndi Mulungu amaima nji ndipo samagwedezeke, ndipo amakhala ndi chisindikizo ndi zolembedwa

Mfundo ziwiri zomwe maziko amaimapo/kumangidwapo:

1. Anthu owomboledwa: + Mulungu amadziwa amene ali ake
2. Anthu owomboledwa amoyo + Aliyese amene akuzitcha yekha ndi dzina la Mulungu asiye zoipa ndikutalikirana nazo.

Zimenezi ndi maziko enieni a kholola lauzimu.

ANTCHITO NGOCHEPA

Ngati antchito ngochepa m'munda wa kholola, zokolola zidzakhala zosasangalatsa kapena zochepa. Zokolola zikhoza kuwola zisanakololedwe. Yesu anati:

Zinthu zichuluka, koma antchito achepa; potero pemphani mwini zinthu kuti akankhe antchito kukututa kwache (Luka 10:2).

ZOTSATIRA

Zinthu zomwe zimantchinga kholola ziri ndi zotsatira zoopsya mudziko la uzimu:

Munda umaonongeka, nthaka imalira; tirigu amaonongeka: Vinyo watsopano amauma, nawo mafuta amatha pang'onopang'ono.

M'munda mwaonongeka, vinyo watsopano wamwelera, mafuta akutha pang'onopang'ono. Gomani, akulima m'minda inu; lirani, akulima mpesa; chifukwa cha tirigu ndi barele; pakuti dzinthu za m'minda zatayika. Mpesa wauma, mkuyu wafota, mtengo wa mkangaza ndi kanjedza ndi maula, inde mitengo yonse ya kuthengo yafota; pakuti chimwemwe chathera ana a anthu. (Yoweli 1:10-12).

Ku dziko la kuthupi, zokolola zochepa zimabweretsa chisoni...

Ndipo chikondwero ndi msangala zachotsedwa m'munda wopatsa zipatso; ndi m'minda ya mipesa simudzakhala kuyimba, ngakhale phokoso losangalala; palibe woconda adaponda vinyo m'moponderamo; ndaleketsa mfuu wa masika amphesa (Yesaya 16:10).

Kudziko lauzimu kholola wochepa amapangitsaso kuti chimwemwe ndi kukondwa zitaiké:

Chakudya sichichotsedwa kodi pamaso panthu? Chimwemwe ndi chikondwerero pa nyumba ya Mulungu wathu? (Yoweli 1:16)

Ngati tikudabwa kuti chifukwa chiani tiribe chimwemwe m'moyo mwanthu, mwinaso nkumadabwa kuti chifukwa chiani timaimba koma chigonjetso chinachoka m'kachisi wathu... zimenezo ndi zotsatira za zokolola zauzimu zochepa.

NDIYE TINGAPANGE BWANJI?

Taona zifukwa zimene zimapangitsa kuti pakhale kholola wochepa wauzimu. Tazindikiraso chifuka chimene tikusowera chimwemwe ndi chisangalalo.

Nde mungatani kuti titembenuze kholola wauzimu wochepa ndikuyambaso kukolola zochuluka miyoyo yanthu?

Pamene kholola wakuthupi anali wochepa ku Israele, Yoweli anauza anthu a Mulungu kuti:

Koma ngakhale tsopano, ati Yehova, munditembenukire Ine ndi mtima wanu wonse, ndi kusala, ndi kulira, ndi kuchita maliro. Ndipo ng'ambani mitima yanu, si zobvala zanu ai; ndi kutembenukira kwa Yehova Mulungu wanu; pakuti Iye ndiye wachisoni ndi wodzala ndi chifundo, wosapsya mtima msanga, ndi wochuruka kukoma mtima ndi woleka choipacho (Yoweli 2:12-13).

Mukuyenera kubwerera kwa Mulungu ndi kulapa posamvera mau ake komaso posakhudzika pa zokolola zauzimu. Mukuyenera kumupempha Iye kuti akuchotsereni tizirombo ndi matenda akuuzimu omwe amakuletsani kukhala okhulupirika. Mukuyenera kulapa chifukwa chakuti mumayesa kuchita panokha; m'madzidalira nokha ndikumpempha chitsogozo chake kuti mukwaniritse cholinga chake ku maiko onse. Mukuyenera kutipula nthaka yomwe sinalimidwepo ndikumanganso maziko amoyo wanu wachiyero.

Yoweli analangiza atsogoleri auzimu kuti alape ndi kusala:

Mudzimangire ciguduli m'cuuno mwanu, nimulire ansembe inu; bwnani, otumikira ku guwa la nsembe inu; lowani, gonani usiku wonse m'ciguduli, inu otumikira

Mulungu wanga; pakuti nsembe yaufa ndi nsembe yothira zaletsedwera nyumba ya Mulungu wanu. Patulani tsiku losala, lalikirani masonkhano oletsa, sonkhanitsani akulu akulu, ndi onse okhala m'dziko, ku nyumba ya Yehova Mulungu wanu; nimupfuulire kwa Yehova. (Yoweli 1:13-14)

Ngati ndinu mtsogoleri wa chiKhristu ndipo mpingo wanu sunatutepo kholola la uzimu mukuyenera muchite zotsatirazi:

- Muitanitse msokhano wa akulu ampingo ndi okutsatirani.
- Mulape ndi kusala kudya pamodzi.
- Mupempheni Mulungu kuti akupatseni masomphenya akholola lauzimu lochuluka.
- Ndipo mugwirizane m'mene mungakwaniritsire masomphenya amenewo.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera mu ndime imeneyi

2. Lembani "T" kutsogolo kwa ziganizo zomwe ziri ZOONA. Lembani F kutsogolo kwa ziganizo zomwe ziri ZONAMA.

- a) _____ Deutoronomo 28 ndi chitsanzo chamalonjezano a Mulungu.
- b) _____ Sanata alibe chidwi mukholola la uzimu.
- c) _____ Kuyesa powekha ndikofunika potuta kholola wauzimu.
- d) _____ Muziyang'ana kaye bwino zochitika musanakolole zauzimu.
- e) _____ Kungochita ntchito zabwino sikokwanira kuti kutha kubweretsa kholola wauzimu.
- f) _____ Mabvuto anu sakukhudzana ndi zochitika zanu koma ndi mphamvu zauzimu.
- g) _____ Ntchito zabwino zochitidwa ndi manja odetsedwa ndizosalandilidwa.

3. Lembani zina mwa zinthu zoipa zomwe timafetsa zomwe zimapangitsa kuti mukolole zoipa zauzimu.

4. Kodi ndi ndi mfundo ziwiri ziti zomwe zimathandiza kuti maziko akhazikike pa Yesu Khristu.

_____ kukhala _____

5. Perekani vesi limodzi lowonetsa kuchepa kwa kholola la uzimu

6. Perekani vesi limodzi lowonetsa zomwe mungachite kuti musinthe vuto la kholola wochepa wa uzimu.

7. Perekani m'ndandanda wa zinthu zomwe zimakanikitsa kholola zomwe takambirana mu chaputala ichi.

POPITIRIZA KUPHUNZIRA

CHIPANGANO CHAKALE

Levitiko 19:19 Deutoronomo 22:9-28

Yobu 4:8 Salimo 105

Miyambo 6:12,14,19; 105; 16:28; 20:4; 24:30

Mlaliki 11:4 Nyimbo ya Solomoni 2:15

Yesaya 16:10; 17:10-11; 28:24-28; 32:9-20

Yeremiya 2; 5:17-19; 8:13-14; 12:10-11

Hoseya 8:7; 10:12-13 Amosi 4:5

Mika 6 Hagai 1

CHIPANGANO CHATSOPANO

Mateyu 13:1-23 1 Akorinto 9:6 Luka 8:4-15; 10:2; 22:31

Mariko 4:2-20 Agalatiya 6:7-8 Yakobo 5:4

CHAPUTALA 6

NDONDOMEKO ZA KHOLOLA WA UZIMU

MBALI YOYAMBA

ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputala ichi mukuyenera kuti muzakwanitse kuchita ichi:

- Kugwiritsa ntchito ndondomeko za m’Baibulo zomwe zimathandiza kuti kholola wauzimu achuluke.

MAVESI OTSOGOLERA

Amene amafetsa ndi misonzi amatuta ndi chimwemwe. Akubzala ndi misozi adatuta ndi kupfuula mokondwera. Iye amene ayendayenda nalira, ponyamula mbeu yakufesa; Adzabweranso ndithu ndi kupfuula mokondwera, alikunyamula mitolo yake (Masalmo 126:5-6).

MAU OYAMBA

Chaputala chapitachi chaonetsera zinthu zomwe zimantchinga kholola lauzimu. Chaputala chino ndi ena otsatirawo afotokoza mwa tsatanetsatane njira zomwe zingapangitse kuti kholola wauzimu akhale ochuluka.

Ndondomeko, mfundo, njira, ndi machitachita omwe amatsatidwa kuti ukafikire cholinga cheni cheni. Zawonetseredwa m’Mau a Mulungu ngati njira zakuthupi zomwe ndizosiyana ndi choonadi cha uzimu.

NDONDOMEKO ZA KHOLOLA

Izi ndindondomeko za kholola

Mudziko la kuthupi pamene Mulungu analenga dziko lapansi anapanga chomera chirichonse kuti chizitha kubereka pachokha.

Mulungu ndipo anati, dziko lapansi limene maudzu, therere lobala mbeu, ndi mtengo wazipatso akubala zipatso monga mwa mtundu wake, momwemo muli mbeu yake, pa dziko lapansi ndipo kunatero (Genesis 1:11).

Monga m’mene ziliri mbeu m’dziko la kuthupi kuti zimatha kubala, okhulupilira aliyense ali nkuthekera kobala muuzimu. Mwa munthu aliyense muli kuthekera kobala muuzimu.

Kungokhala ndi chidziwitso chochuluka pa zauzimu sikoyenera kuti mungathe kukhala mbali ya kholola la uzimu.

Ndipo ananena, Ufumu wa Mulungu uli wotere, monga ngati munthu akataya mbeu panthaka.... ndipo mbeu zikamera, ndi kukula, iye sadziwa umo zichitira. Pakucha zipatso pamenepo atumiza zenga, pakuti nthawi yakumweta yafika (Marko 4:26, 27, 29).

Nzosafunika kuti timvetse tsatanetsatane wa mmene mbeu zimakulira; umu ndi m'mene mbeu ya Mau a Mulungu imakhazizikira m'mitima mwa anthu. Sizikutengera kuti muchite kukhala chimvetsetso chakuya pa za Umulungu.

Chofunika nchakuti inuyo mutenge nawo mbali pa kholola la uzimu.

KUFESA NKOFUNIKA CHIFUKWA KUMAPANGITSA KUTI TIDZAKOLOLE

M'dziko la kuthupi, kuti udzakolole ukuyenera kufesa kaye mbeu. M'dziko lauzimunso ukuyera kufesa kuti udzakolole. Mulungu amapereka zipangizo zauzimu pa kafesedwe.

Ndipo Iye wapatsa mbeu kwa wofesa, ndi mkate ukhale chakudya, adzapatsa ndi kuchurukitsa mbeu yanu yofesa, nadzaonjezapo pa zipatso za chilungamo chanu. (Akorinto 9:10).

Mulungu amachurukitsa maluso ndi kuthekera kwanu kwa uzimu ndi cholinga choti mukathe kubala.

Mulungu amaze ndi kuchurukitsa njira zanu zopezera chuma kuti mukathe kufesa mu ntchito yake. Samachurukitsa chuma chanu ndi cholinga choti muzikundikire nokha. Cholinga nchakuti mukathe kufesa mu ufumu wake.

SIMUMAKOLOLA MUNYENGO YOMWE MWAFESAYO:

Pachiyambi Mulungu anakhazikitsa ndondomeko ya m'mene nyengo iziyendera ku dziko lapansi.

Pakukhalabe masiku a dziko lapansi, nthawi yakubzala ndi yakukunkha, chisanu ndi mafunde, malimwe, ndi msakasa, usana ndi usiku sizidzaleka. (Genesis 8:22)

Kufesa nkofunika chifukwa kumapangitsa kuti tikolole. Koma kukolola sikumachitika munyengo yomwe tafesayo. Ena amalandira masomphenya a kholola la uzimu ndipo amakhumudwa chifukwa samamvetsetsa mfundo imeneyi. Palitu nthawi yofesa koma mukuyenera kudikira kaye kudikira kuti mbeu ya mau imere m'mitima ya amuna ndi akazi. Pali nthawi yogwira nthito yosamalira mbeu mofatsa. Simungakolole mu nyengo yomwe mwafesayo.

Masalimo 1 akuyakhula za ndondomeka imeneyi mu m'moyo wa wokhulupilira:

Ndiye akunga mtengo wooka pa mtsinje ya madzi; wakupatsa chipatso chake pa nyengo yake... (Masalimo 1:3)

Ngati pali nyengo yoti zipatso zimabala ndiye kuti palinso nyengo zina pamene mbeu zimakhala osabala. Imeneyi ndi nyengo yolimanso nthaka, kufesa ndi kuti zikule. Koma nyengo imene kulibe zipatsoyi ndiyabwino popeza imatha kubweretsa zokolola.

Ndondomeko yozindikira nyengoyi ndiyofunika ku kholola. Mukuyenera kudikira mofatsa kwambiri pa nthawi yomwe mbeu zikukula, koma mukuyenera kuzindikira bwino nyengo yomwe muzakolole ndipo muzikhala antcheru kwambiri kuwopa kuti mbeu zingawonongeke.

Pakucha zipatso, pamenepo anatumiza zenga, pakuti nthawi yakumweta yafika. (Mariko 4:29).

Mwachidure, pali:

Pali mphindi yakubzyala ndi mphindi yakuzula zobzyalazo (Mlaliki 3:2).

UMAKOLOLA ZOMWE WAFESA

Mbeu zimabala malingana ndi mtundu wake pa dziko lapansi. Ngati mubzyala mbeu ya mandimu muzakolola mandimu. Izinso ziri chimodzimodzi ndi dziko lauzimu:

Musanyengedwe; Mulungu sanyozeka; pakuti chimene munthu achifesa, chimenenso adzachituta (Agalatiya 6:7).

Kufesa ku thupi kumabweretsa zokolola zovunda pamene kufesa m'chilungamo kumabweretsa zokolola zabwino.

MUKUYENERA KUFESA POSAYANG'ANIRA ZOKUZONGULIRANI

Onse amene amayang'ana nyengo zomwe zawazungulira sadzakhala nawo mbali imodzi ya masomphenya a kholola. Nyengo zomwe zawazungulira zimawangonjetsa monganso m'mene achitira mlimi amene alekelera munda wake chifukwa amayang'ana mphepo komanso mitambo:

Woyang'ana mphepo sadzafesa; ndi wopenya mitambo sadzakolola (Mlaliki 11:4).

Mfundo yofunika kwambiri pa kholola wa uzimu ndiyakuti muzifesa posayang'anira nyengo za moyo.

Odala muli inu, amene mubzala m’mbali mwa madzi monse, pakuti mbeu izamila matope ndipo madzi akabwera idzatumphuka; ndipo inu mudzaipeza pakapita masiku ochuluka ndipo muzakolola zochuluka kwambiri.... (Yesaya 32:20).

Mukuyenera kufetsa m’mbali mwa madzi zimene zikutanthauza nyengo zonse za moyo wathu. Ngakhale pamene nyengo zowawitsa zitsefukila m`moyo wanu, musaleke kufetsa. Pa ichi Mulungu walonjeza kholola lokhuchumuka.

KHOLOLA LANU LITENGELA MULINGO WA KUFETSA KWANU

Kumbukilani mau awa;

“Koma nditi ichi, iye wakufetsa mouma manja, mouma manjanso adzatuta. Ndipo iye wakufetsa moolowa manja, moolowa manjanso adzatuta.” (2 Akorinto 9:6).

Nzeru iyi imagwira ntchito mbali iliyonse ya moyo wa munthu. Ngati mupeleka nthawi yanu, luso lanu, ndi chuma chanu mouma manja ku nthito ya Mulungu, dziwani kuti kholola lanu lidzakhala lochepa zedi. Ngati mufetsa moolowa manja, mudzakolola mokhuchumuka. Pali milimgo yotsiyana mukholola la uzimu yomwe yakambidwa m`Buku Lopatulika pa Yohane 15. Zokolola za munthu zingathe kukhala:

- Zipatso : Yohane 15:2
- Zipatso zambili : Yohane 15:2
- Zipatso Zochulukitsa : Yohane 15:4
- Zipatso zochuruka ndi zokhalitsa : Yohane 15:16

Mulungu akufunitsitsa kuti inu mubale zipatso zochuruka komanso zokhalitsa.

Petro akuonetsera zimene mukuyenera kuchita m`moyo wanu kuti mubale zipatso zochuruka ndi zokhalitsa:

Ndipo wa ichi chomwe, pakutengaponso changu chonse, muonjezerepo ukoma pa chikhulupiriro chanu, ndi pa ukoma chizindikiritso, ndi pachizindikiritso chodziletsa, ndi pachodziletsa chipiriro, ndi pachipiliro chipembedzo, ndi pa chipembedzo chikondi cha pa abale, ndi pa chikondi cha pa abale chikondi. Pakuti izi zikakhala ndi inu, ndipo zikachuruka, zidzachita kuti musakhale aulesi kapena opanda zipatso za chizindikiritso cha Ambuye Yesu Khristu (2 Petro 1:5-8).

Petro akutichenjeza kuti ngati sitipanga zinthu izi kukhala mwa ife, sitingathe kukhala ndi masomphenya a uzimu.

Pakuti iye wakusowa izi ali wakhungu, wa chimbuuzi, woiwala matsukidwe ake potaya zoipa zake za kale (2 Petro 1:9).

MUNGATE KUFETSA POMWE INU ENI SIMUKOLOLA KOMANSO KUKOLOLA PAMENE INU ENI SIMUNAFESE.

AIsraeli atangolowa mu m'dziko lolonjezedwa, Mulungu adauza ana a Israeli kuti azadya kuchokela ku mpesa umene iwo sadalime. Adakatha kukolola pomwe iwo sadafetse.

Izinso zimachitika m'dziko la uzimu. Mutha kukolola zimene ena adafetsa.

Pakuti m`menemo chonenacho chili choona, wofetsa ndi wina, womweta ndi winanso. Ine ndinatuma inu kukamweta chimene simunagwirirapo ntchito: ena anagwira ntchito ndipo inu mwalowa ntchito yao (Yohane 4:37-38).

Kwa nthawi yaitali okhulupilira ambiri afetsa m'miyoyo yawo ku kholola la kuthupi. Pamene Ambuye atsala pang'ono kubweranso, zokolola zawo ndizochuruka m'maiko a padziko. Mumalowa mu ntchito zawo ngati mukukulola pomwe simunafese.

Inu mukuyenera kukhala mbali imodzi yakufesa osati ongokolola basi.

Ndipo naye Paulo akuyakhula zaizi:

Ndinaoka ine, anathirira Apolo; koma Mulungu anakulitsa. Chotero Sali kanthu kapena wookayo ndi wothirirayo ali amodzi; koma yense adalandira mphoto yake ya iye yekha, monga mwa kuchititsa kwake kwa iye yekha. Pakuti ife ndife antchito anzake a Mulungu (I Akolinto 3:6-9).

MUDZAKOLOLA ZOKOLOLA NGATI NDINU WOKHULUPIRIKA

Koma tisaleme pakuchita zabwino; pakuti pa nyengo yake tizatuta, tikapanda kufoka (Agalatiya 6:9).

Potero, lezani mtima, abale, kufikira kudza kwace kwa Ambuye. Taonani, wolima munda alindira cipatso cofunikatu ca dziko, ndi kuleza mtima naco kufikira cikalandira mvula ya myundo ndi masika (Yakobo 5:7).

Ngati muli okhulupirika Mulungu walonjeza kuti mudzakolola kholola. Musaleme pantchito yomwe wakupatsani kuti mugwire.

KUTI IKABALENSO MBEU IKUYENERA KUTI IFE

Mbeu imaoneka yakufa. Yopanda masamba obiriwira, yopanda mphukira kapena nthambi zosangalatsa. Koma kuti mbeu imere ikuyenera kuti ibzalidwe kapena ikwiriridwe.

Pali kufanana kwakukuru pakati pa za dziko ndi zauzimu. Moyo wauzimu umadalira imfa yomwe inachita mwa nsembe.

Wopusa iwe, cimene ucifesa wekha sicikhalitsidwanso camoyo, ngati sicifa (1 Akorinto 15:36).

Kunali kufunika kuti Yesu afere pa mtanda kuti moyo upezeke. Utumuki wake unawoneka monga osapindulitsa chifukwa unakathera mu imfa.

Koma imeneyo inali nthawi yake yofesa. Ndiye kudzera kukufesa kwake mu imfa kwatuluka kholola lochuluka kuchokera pa ngale ya tirigu yomwe inagwera pa nthaka. Kuchokera pa imfa Yake anthu ambiri apeza moyo.

Moyo wauzimu umafunika kuuperekera nsembe ya imfa. Umafuna kufa ku tchimo. Umafuna kufa ku zilakolako ndi zofuna za dziko.

Jim Elliott, anaphedwa chifukwa cha Khristu pamene ankayesera kuti akalalikire ku Auca ku Ecuador, analemba mu buku lake: “palibe munthu opusa amene angapereke chomwe sangathe kuchisunga kuti apindule chomwe sangakwanitse kuchitaya”

Pamoyo waku thupi, chotsutsana nacho chachikulu ndi imfa chifukwa imfa imabweretsa moyo wosatha kwa okhulupirira. Imfa yowawa ndi imene umafa popanda cheni cheni choferacho. Mutsimikizike kuti chomwe mukhalira ndi moyo, ndi choyenera kuchifera.

Nthawi zina sipamapezeka umboni wooneka wa kholola. Zitha kumawoneka ngati mukutaya moyo wanu chifukwa cha masomphenya amene akufa.

Koma mukuyenera kukumbukira kuti:

Indetu, indetu ndinena ndi inu. Ngati mbeu ya tirigu siigwa m’nthaka, nifa, ikhala payokha iyo; koma ngati ifa, ibala chipatso chambiri (Yohane 12:24).

Yesu sanangofa pachabe. Mkatikatimo muli moyo ochokera kwa Mulungu. Koma kuti moyo uperekedwe pakuyenera kuti imfa ichtike.

Hosea akuyankhula za zotsatira pakufesa moyo wanu m’njira imeneyi:

Ndipo ndidzam’bzalira iye m’nthaka ndipo ndidzachitira chifundo wosachitidwa chifundo; ndipo ndidzati kwa omwe si anthu anga, muli anthu anga; ndipo iwo adzati, Ndinu Mulungu wathu. (Hosea 2:23).

Ndime imeneyi ikukamba mwachidule chifukwa chogwiritsira ntchito ndondomeko za kholola lauzimu. Muzigwira ntchito kuti Mulungu azinena kwa anthu omwe siake “Awa ndi anthu anga; ndipo iwo azati, Ndinu Mulungu wathu.

MAYENSO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani mavesi omwe munaloweza.

2. Fotokozani tanthauzo la 'ndondomeko'.

3. Lembani ndondomeko zisanu ndi zinayi za kholola wauzimu zomwe zafotokozeredwa bwino mu chaputala chino.

POPITIRIZABE KUPHUNZIRA

FANIZO LA WOFESA

Pali mafanizo ambiri m'Baibulo omwe amakamba za kufesa ndi kuululanso zambiri za kholola lauzimu. Fanizo la Wofesa (Mateyu 13, Mariko 4, Luka 8) lafotokozedwa bwino m'phunziro lino. Mafanizo ena a munda wamphesa alembedwa m'musimu kuti mukathe kuwaphunzirabe.

DENGU LA ZIPATSO ZAKUCHA: Amosi 8:1-2

Ndi chitsanzo chotani cha padziko chomwe Mulungu anamuwonetsa Amosi?

Kodi tanthauzo lachitsanzo chimenechi chinali chani?

Kodi njala imene Mulungu anatumiza kwa a Israele chifukwa chosamvera mau ake inali yotani? (ndime 11-12)

MUNDA WA MPESA WA MULUNGU: Yesaya 5:1-7

Fanizo iri likunena za fuko la Israele. Mulungu abzala Israele mudziko lauzimu kuti akathe kubereka ndi kudalitsa mafuko adziko la pansu. Koma Israele sanakhale opindulitsa. Kodi zotsatira za kholola lauzimu zinali zotani kwa Israele? (ndime 4)

Kodi munda wa mphesawu unaweruzidwa motani (ndime 5-6)?

Kodi ndime 7 ikusiyana bwanji?

Mulungu anayembekezera _____ koma anapeza: _____

Anayembekezera: _____ koma anapeza:
_____ (zosalungama).

Ndizifukwa zotani zinapangitsa Israele kuti akhale munyengo imeneyi kuuzimu (ndime 13, 20)?

MUNDA WA MPESA WA MULUNGU: Mateyo 21:28-41; Mariko 12:1-9; Luka 20:9-16

Nalo fanizo la m'Chipangano Chatsopano limeneli likukamba za munda wa mphesa wa Mulungu. Iyi ndi mbiri ya momwe Mulungu anatumizira aneneri ake ku Israele koma iwo anamkana. Kenako anatumiza mwana wake yekhayo, Yesu Khristu, ndipo Nayeso anakanidwa.

Kodi yankho la wolimayo (Israele) linali lotani kwa atumiki omwe Mulungu anawatumiza?

Nanga mwana anayakha bwanji?

Ndi chilango chotani chomwe Mulungu anawatumizira?

(kwina komwe anakatumizanso kunali kwa amitundu)

MTENGO WA MKUYU: Luka 13:6-9

Pamene mwini munda anabwera kuti azakolole zipatso za mtengo wa mphesa, anapezamo chiani?

_____.

Amkafuna kuti atani? _____.

Kodi yemwe amakayang'anira mundawo anayankha motani? _____.

Mtengo wa mkuyu ukuimilira Israele. Ndiye muganiza kuti fanizoli likutanthauza chiani?

_____.

_____.

ANTCHITO M'MUNDA WA MPESA: Mateyu 20:1-16

Kodi antchito omwe anabwera molawira malipiwo awo anali wotani?

_____.

Kodi antchito omwe anabwera mochedwa analandira malipiro otani?

_____.

Kod ndi vuto lanji lomwe linabwera pakati pa antchitowo?

_____.

Kodi ndi ndondomeko iti yomwe Yesu akuwonetsera ndi fanizo limeneli? (ndime16)

_____.

FANIZO LA ANA AWIRI: Mateyu 21:28-31

Pamene bambo anauza ana ake kuti akagwire ntchito ku munda wampesa:

Kodi mwana woyamba anayankha motani? _____.

Kodi mwana oyambayo kwenikweni anachita motani? _____.

Kodi mwana wachiwiri anayankha motani? _____.

Kodi mwana wachiwiriyo kwenikweni anachita motani? _____.

Kodi ndi mfundo yotani yomwe Yesu amaphunzitsa kudzera mu fanizo ili?

_____.

ZOKOLOLA: Mateyu 9:37-38; Luka 10:2; Yohane 4:34-38, 12:24

Nthawi zambiri Yesu anagwiritsa ntchito zitsanzo za kholola la kudziko pofuna kufotokoza za choonadi chakuuzimu.

Kodi chosowa chachikulu m'munda ofuna kukololedwa ndi chiani?

Kodi ndi chinthu chotani tingachite ku vutoli (Mateyo 9:38)?

Kodi ndi ndondomeko yanji ya kholola yomwe Yesu anaphunzitsa pa Yohane 12:24?

Ndi choonadi chanji cheni cheni chomwe mukuphunzira pakati pa ofesa ndi okolola pa Yohane 4:36-38?

NAMSONGOLE: Mateyu 13:24-30

Ndi mbeu yotani yomwe inafesedwa m'mundamu? _____

Chinachitika nchilani pomwe antchito anagona? _____

Kodi yankho linali lotani pa vuto la nansongole yemwe anafesedwa? (ndime 30)

Nchifukwa chani mwini munda anabweretsa yankho limeneli? (ndime 29)

Kodi ndi udindo wathu kusiyanyitsa nansongole ndi tirigu? _____

MBEU YA MPIRU: Mateyu 13:31-32; Mariko 4:31-32; Luka 13:18-19

Mbeu ya mpiri ndi _____ pa mbeu zonse.

Imakhala mbeu yotani pamene ikukula? _____

Ndi choonadi chanji chazimu chomwe Yesu amaphunzitsa ndi nkhani ya mbeu ya mpiruyi?

Pa Mateyu 17:20 Yesu anagwiritsa ntchito mbeu ya mpiru ngati chitsanzo cha chikhulupiro. Kodi ndizotsatira zANJI pokhala ndi chikhulupiro chochepa?

CHAPUTALA 7

NDONDOMEKO ZA KHOLOLA WA UZIMU

MBALI YACHIWIRI

Pomaliza pa chaputala chino mukuyenera kutha kuchita izi:

- Kufotokoza kufanana kwa pakati pa zauzimu ndi momwe mbeu zimakulira mwa chilengedwe chake.
- Kutha kugwiritsa ntchito kufanana kumeneko ngati ndondomeko pa kholola la uzimu.

VESI YOTSOGOLERA

Pakuti monga dziko liphukitsa mphundu zace, ndi monga munda umeretsa zobzalamo, momwemo Ambuye Yehova adzaphukitsa cilungamo ndi matamando pamaso pa amitundu onse (Yesaya 61:11).

MAU OTSOGOLERA

Chaputala ichi chikupitiriza kuphunzitsa kwa ndondomeko za kholola lauzimu. Ikukhudza kwambiri mfundo ya kukolola. Mbeu imamera chifukwa cha nyengo ya kunjja.

Mu dziko la ku thupi pali nyengo zomwe ndizofunika kuti kukula kwa mbeu kuchitike. Nyengo zimenezi ndizofanananso ndi nyengo zauzimu zomwe ndi zofunika kuti mbeu ya Mau a Mulungu kuti ibweretse kholola wa uzimu.

ZOYENERA KUTI KUKULA KUCHITIKE M'MOYO

Popanda moyo kukula sikungakhalepo. Mu mbeu mukuyenera kukhala moyo, kupanda apo singakule. Yesu anali bvumbulutso lowoneka ndi maso la Mau a Mulungu, mbeu, ndipo mwa Iye munali moyo.

Mwa Iye munali moyo; ndi moyowu unali kuunika mumdima; ndi kuunika kwa anthu. (Yohane 1:4)

Pakuti monga Atate ali ndi moyo mwa Iye yekha, momwemonso anapatsa kwa Mwana kukhala ndi moyo mwa Iye yekha. (Yohane 5:26)

Yesu anabwera kuzadzala mbeu ya moyo mwa inu kuti mukathe kubekera:

Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wochuluka...

Moyo wake uli mwa inu. Mukadzala mbeu ya mau ake, mumadziwa kuti....

Pakuti munga mvula imagwa pansi ndi matalala, kucokera kumwamba yosabwerera komweko, koma ikhamiza nthaka ndi kuibalitsa, ndi kuiphukitsa, ndi kuipatsitsa mbeu kwa wobzyala, ndi cakudya kwa wakudya; momwemo adzakhala mau anga amene aturuka m'kamwa mwanga, sadzabwerera kwa Ine cabe, koma adzacita cimene ndifuna, ndipo adzakula m'mene ndinawatumizira (Yesaya 55:10-11).

NTHAKA YA CHONDE

Mwaphunzira mu phunziro lino, kuti nthaka yopanda chonde imachepetsa zokolola. Nthaka ya chonde imathandiza kuti kholola likhale labwino:

Ndipo iwo ofesedwa pa nthaka yabwino ndiwo oterewa akumva mau, nawalandira, nabala zipatso zakupindula makumi atatu, ndi makumi asanu ndi limodzi, ndi makumi khumi (Mariko: 20).

Ngati mukufuna kukolola mu dziko la uzimu mukufunika kuti mulime pa nthaka yabwino. Mukuyenera kulambula nthaka, ndi kudzala mbeu ya Mau mosamalitsa. Zonse ndi zofunika kuti kholola lichitike. (Hosea 10:12; Yeremiya 4:3)

Malingana ndi fanizo la wofesa (Mariko 4:3-20), ngati palibe zokolola ndiye kuti vuto ndi nthaka. Iyi ndi mfundo yofunika kwambiri pa kholola. Nthaka yopanda chonde sikuyenera kunyanyalidwa. Wina akuyenera kubzala, kukulitsa komanso kuzindikira nthawi yokolola. Koma apa sipoyenera kukhazikikapo pa mphamvu zauzimu. Yesu sananene kuti padzasowa ofesa koma anati padzasowa okolola. Ntchito yeniyeni ya kholola lauzimu ikuyenera kuti ikuikidwirapo mtima ngati nthaka yake iri ndi chonde komanso ngati pali zokolola.

Kuzindikira nyengo ndikofunika pa kholola. Okolola samafunika pamene mbeu yangofesedwa kumene kapena pamene siinakhwime. Koma nthawi yomwe zokolola zimakhwima chifukwa cha nthaka yabwino. Nthawi imeneyo ndiyomwe anthu okolola amafunika. Ngati antchito onse atanganidwa ndi nthaka yauzimu yopanda chonde ndipo palibe okolola, ndipo zikatero mwayi okolola umakhala wataika mpakana kale kale chifukwa cha nthaka yopanda chonde m'munda wa uzimu.

MADZI:

Madzi ndiofunika kwambiri kuti mbeu imere ndipo kuti ibereke mu dziko la kuthupi. Mulungu analonjeza:

Pakuti ndidzathira madzi pa dziko limene liribe madzi, ndi mitsinje pa nthaka youma. (Yesaya 44:3)

Kuthira uku ndikudzodza kwa Mzimu Woyera komwe madzi ndi chizindikiro chake:

Ndidzathira Mzimu wanga pa mbeu yako (Yesaya 44:3b).

Iye wokhulupirira Ine, monga chilemba chinati, “Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda, kuturuka mkati mwake” (Yohane 7:38).

Madzi a Mzimu Woyera amapangitsa kuti mbeu ya Mau a Mulungu kuti imere mizu m’mitima ya amuna ndi akazi omwe ali akufa muuchimo.

Pakuti akaulikha mtengo Pali chiyembekenzo chakuti udzaphukiranso. Ndikuti nthambi yake yamthete sidzasowa.

Ngakhale muzu wake wakalamba m’nthaka. Ndi tsinde lake likufa pansu.

Koma pa mnukho wa madzi udzaphuka, nudzaswa nthambi ngati womera (Yobu 14:7-9).

KUUNIKA:

Kuunika kumapangitsa kuti mbeu zikule m’dziko la kuthupi. Ndikuwala kwa Mau a Mulungu komwe kumachititsa kuti kholola la uzimu likhalepo.

**Mwa Iye munali moyo, ndi moyo moyowo unali kuunika kwa anthu. (Yohane 1:4)
Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; Iye wonditsata Ine sadzayenda mudima,
koma adzakhala nako kuunika kw amoyo (Yohane 8:12).**

Kuunika kwa Mulungu kumabweretsa moyo wa uzimu.

MPWEYA:

Pali chinthu chofunika kwambiri chomwe chimatchedwa mpweya woyipa womwe umagwiritsidwa ntchito ndi mbeu m’dziko la kuthupi. Mpweya ndiofunika kwambiri pa kakulidwe ka mbeu. Mu Baibulo Mzimu Woyera amafaniziridwa ndi mpweya kapena mphepo.

Mphepo iomba pomwe ifuna, ndipo ukumva mau ake, koma sudziwa komene imuka, chotero ali yense wobadwa mwa Mzimu (Yohane 3:8).

Mzimu Woyera umapumira moyo ku mbeu ya Mau yomwe imapangitsa kuti pakhale kukula muuzimu.

DANGA:

Mu fanizo la wofesa, mpikisano pa danga kapena mpata unapangitsa kuti mbeu zina zife:

Ndipo iye amene afesedwa ku minga, uyu ndiye wakumva mau; ndipo kulabadira kwa dziko lapansi, ndi chinyengo cha chuma chitsamwitsa mau, ndipo akhala wopanda chipatso (Mateyu 13:22).

Mpikisano pa zinthu za kuthupi kungapangitsenso kuti mbeu ya mau itsamwitsidwe ndipo zingapangitsenso kuti kholola wauzimu akhale ochepa.

MMENE MIZU ILIRI:

Mizu ndiyofunika kwambiri chifukwa imagwira, komanso imapereka zakudya ku mbeu. Salimo loyamba limanena m'mene mizu ingapangidwire m'moyo wauzimu wanu.

Wodala munthuyo wosayenda mu uphungu wa oipa, kapena wosaimirira m'njira ya ocimwa, Kapena wosakhala pansu pa bwalo la onyoza. Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace; Ndipo m'cilamulo cace amalingilira usana ndi usiku. Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; Wakupatsa cipatso cace pa nyengo yace, Tsamba lace lomwe losafota; Ndipo zonse azicita apindula nazo (Masalmo 1:1-3).

KUPUMULA:

Mbeu imapumula munthawi imene imatchulidwa kuti yachete. Nyengo yacheteyi ndimene mbeu zimapumula.

Nyengo yopumula imachitika nthawi yokula mwansanga isanachitike. Mbeu mu nthawi imeneyi imawoneka ngati yafa. Koma zimakhala zisanafe. Mbeu ya moyo imakhala ikadalipobe.

Mukabzala mbeu ya Mau a Mulungu mwa amuna ndi akazi nthawi zonse imakumana ndi nyengo yachete yomwe simungaone zikukula. Mukhoza kumaona ngati mwalephera cholinga chanu. Koma mbeu imakhala isanafe.

Monga mmenenso zimakhallira kudziko la kuthupi, nthawi yachete ya uzimu singapose nyengo yakukula kwake mwamsanga.

Taonani, wolima munda alindira chipatso chofunikatu cha dziko, ndikuleza mtima nacho kufikira chikalandira mvula ya myundo ndi masika (Yakobo 5:7).

KULUMIKIZIDWA KU MPESA:

Kudziko lakuthupi kuti mbeu ibereke zipatso nthambi imayenera kuti ilumikizidwe ku mtengo waukulu. Ngati nthambi ithyoka ku mpesa omwe umaupatsa moyo singaberekenso chipatso.

Yesu ndi mpesa ndipo ife ndi nthambi zake, ndekuti tibereke zipatso za uzimu, tikuyenera kukhalabe pa ubale ndi Iye:

Ine ndine mpesa weni weni, ndipo Atate wanga ndi wam'munda.

Nthambi iriyonse ya mwa Ine yosabala chipatso, aichotsa; ndi iri yonse yakubala chipatso aisadza, kuti ibereke chipatso chochuruka.

Mwakhala okonzeka tsopano inu chifukwa cha mau amene ndayakhula ndi inu.

Khalani mwa ine, ndi Ine mwa inu. Monga nthambi singathe kubala chipatso pa yokha, ngati siikhala mwampesa, motero mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine. (Yohane 15:1-4)

KUSADZA:

Kusadza nkofunikira kwambiri ku dziko la kuthupi ngati tikufuna kuti mbeu ipitirire kuchitabe bwino pakubereka zipatso. Pameme mlimi akusadza amakhala kuti akuchotsa nthambi zonse zosabereka ndicholinga choti apange mbeu kuti ibale zipatso zochuruka. Amachotsa zonse zomwe zinakatchinga kakulidwe ka mbeu.

Kusadza nkofunikaso m’dziko lauzimu. Kusadza kwa uzimu ndikukonzedwa ndi Mulungu. Kukonzedwa kumeneku Baibulo limakutchulaso kuti kukwapulidwa (chilango). Mulungu akamasadza, amachotsa china chilichonse m’oyo wanu chomwe chinakatchinga kukula kwa moyo wanu wauzimu. Ndongomeko imeneyi ndiyofunika ngati mufuna kuti mubale zipatso za uzimu.

Nthambi iri yonse ya mwa Ine yosabala chipatso, aichotsa; ndi iri yonse yakubala chipatso, aisadza kuti ikabale chipatso chochuruka. (Yohane 15:2)

Nthawi zina sitiona kufunikira kosadzidwa chifukwa timangomuda satana pamene Mulungu amakhala kuti akubweretsa nyengo m’oyo wanu ndicholinga choti akukozeni. Cholinga chenicheni cha chidzudzulo cha Mulungu chiri mu Hosea 6:1

Tiyeni tibwerere kunka kwa Yehova; pakuti wang’amba, nadzatipoletsera; wakantha, nadzatimanga (Hosea 6:1).

Chidzudzulo chosadzidwa zotsatira zake zakuti umabwereranso kwa Mulungu. Kubwerera kwa Iye kuzakupangitsani kuti mukhale aphindu ku uzimu.

NYENGO:

Nyengo ndiyofunika kwambiri ku dziko la kuthupi. Nthawi zina zomera zimasungidwa m’nyumba yotchedwa kuti “nyumba yotentha” pa mulingo woyenerera kuti zikule. Zimakhala zotetezeka kuzopsya za dziko la kuthupi. Ngati mungatenge mbeu mu “nyumba yotentha” nkuipititsa panja, imafa mwa msangasanga chifukwa imakhala mu nyengo yochita kukonzedwa. Singathe kupilira kunyengo yaku dziko la kuthupi.

Poyankhula mwauzimu, ife sitikufuna aKhristu a “nyumba yotentha” amene akumaoneka bwino munyengo yochita kukozayi koma akulephera kubala makamaka akakumana ndi za dziko la kuthupi. Mbeu ya Mau a Mulungu yabzalidwa m’ moyo wako ndipo imakhalabe moyo kwa onse amene ukuwatumikira ikuyenera kuti ikule posayang’ ana nyengo.

KUUMBA MKUTA

Chaputala chino chamalizitsa ndondomeko za kholola la uzimu. Kafufuku wa mfundo wapeza zinthu zotsatirazi zomwe ndizofanana pakati pa choonadi chamoyo wauzimu ndi moyo wa kuthupi:

- Mbeu iliyonse ili nkuthekera kodzichulukitsa
- Kufetsa nkofunika kuti tidzakolole.
- Sumakolola munyengo yomwe wafesayo.
- Mukuyenera kufesabe posayang’ ana nyengo zomwe zakuzungulirani.
- Umakolola molingana ndi zomwe unafesa.
- Ukhoza kufesa pomwe sungakolole komanso kukolola pomwe sunafese.
- Udzakolola zokolola ngati muli okhulupirika.
- Kuti mbeu ikabereke, ikuyenera kufa kaye.
- Mbeu imamera chifukwa cha nyengo zina zakuthupi.

Kumvetsetsa bwino ndi kuzigwiritsa ntchito ndondomeko zimezi zizapangitsa kuti kholola wa uzimu akhale ochuluka kwambiri. Chaputala chotsatira chionetsera m’mene tingakololere zokolola.

MAYENSO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yomwe mwaloweza.

2. Ndi ndondo iti ya kholola yomwe yaphunzitsidwa komalizira mu chaputala chino?

3. Lembani zinthu nkhumu zomwe ndi zofunika kuti mbeu ku moyo waku nthupi zikule zomweso tingazigwiritse ntchito ku kholola wauzimu:

_____.

(Mayankho ameyenso awa aperekedwa kumapeto chomaliza cheni cheni a buku lino)

POPITIRIZA KUPHUNZIRA

Mmachaputala awiri apitawo taona kuti pali kufanana pakati pa ndondomeko za kufesa ndi kukolola mdziko la uzimu ndi la kuthupi. Yesu anapereka phunziro lofanana kudzera mfanizo la ofesa. Fananitsani mafanizo atatu mu Mateyu 13:3-9; Mariko 4:3-20; ndi Luka 8:5-14.

1. Kodi panali kufanana kotani pakati pa zauzimu ndi mbeu yomwe inabzalidwa?

(Luka 8:1)

2. Nthaka yosiyanasiyana ikuimira m'mene anthu amalandiira mau a Mulungu.

Malizitsani tchatu yotsatirayi yomwe ikuwonetsa mitundu ya nthaka yosiyasiyana ndi zotsatira pa mbeu yomwe yafesedwa:

Mtundu wa Nthaka

Zotsatira kuchokera ku mbeu imene inafesedwa

3. Kodi chimachitika ndi chiani munthu akamva mau koma osati kuwamvetsetsa bwino? (Mateyu 13:19)
- _____

4. Kodi chinachititsa nchiani kuti mbeu zomwe zinagwera pa mwala zife? (Mateyu 13:20-21; Luka 8:6-13).
- _____
- _____

5. Ndi zinthu ziti zomwe zikufaniziridwa ndi minga zomwe zimatsamwitsa Mau a Mulungu?

(Mateyu 13:22; Mariko 4:18; Luka 8:14)

6. Chimachitika nchiani pamene mau atsamwitsidwa ndi minga? (Mateyu 13:22)
Amakhala_____

7. Kodi fanizoli likuwonetsa kusiyana kotani pamene mbeu yomwe inafesedwa pa nthaka yabwino yakololedwa? (Mateyu 13:23)

Nanga zotsatira zake nzotani?

8. Chinachitika nchiani ku mbeu zomwe zinagwera mbali mwa mseu?
(Mariko 4:4; Luka 8:5)

Kodi pali kufanana kotani pa zauzimu ndi izi (Mariko 4:15)

_____ zimabwera msanga ndi kutola Mau omwe afesedwa.

9. Kodi makhalidwe a anthu omwe mitima yawo iri ngati nthaka yabwino ndi otani? (Luka 8:15). Ali ndi mtima wo_____ ndi wo_____

10. Kodi ndi kuyankha kutatu kuti komwe anthu amene ali ngati nthaka yabwino amapereka? (Luka 8:15)

11. Mayankhidwe osiyanasiyana ku Mau a Mulungu sizikutanthauza kungovomera kokha Uthenga Wabwino. Zimagwiritsidwanso ntchito ku choonadi chenicheni cha mau omwe Mulungu wawabzala m'miyoyo yathu.

Masopenya a kholola abzalidwa mwa inu. Kodi abzalidwa pa nthaka yachonde yauzimu? Kodi zotsatira zake zingakhale zotani?

Kodi zagwera mphepete mwa njira? Ngati ndi choncho, ndiye kuti masomphenya akwatulidwa ndi satana chifukwa simunawapange iwo kukhala ofunika kwambiri.

Kodi zagwera pa nthaka ya miyala? Mukhoza kukhala kuti munalandira masomphenya a kholola ndi chimwemwe koma sizinazike mizu mmitima mwanu. Pamene nthawi ya zowawa ikafika mudzasiya masomphenyawo? Kodi masomphenya amenewa abzalidwa pakati pa minga? Kodi mmakhudzidwa kwambiri ndi chisamaliro, chuma, zosangalatsa, ndi zokhumba za moyo uno? Kodi zinthu za kathawizi m'mazitenga kukhala zofunika kwambiri kuposa masomphenya? Ngati ndichoncho, simudzabweretsa kholola. Kodi bvumbulutso la kholola lagwera pa nthaka yabwino? Kodi mwalandira ndikuwasunga maso mphenya? Ngati ndichoncho mudzabweretsa zipatso ndipo mudzakhala opindulitsa kuuzimu.

CHAPUTALA 8

KUTUTA MWA BVUMBULUTSO

ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputala ichi muzakhala mukutha:

- kufotokoza njira zomwe Mulungu amagwiritsa ntchito pochulukitsa.
- kuonetsera chifanizo cha uzimu chomwe chimapangitsa kututa mwa bvumbulutso.
- Kudutsa pa mdalitso kuti mukathe kumva mphamvu yauzimu.

VESI YOTSOGOLERA:

Koma muzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalem, ndi m'Yudeya lonse ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko (Machitidwe 1:8).

MAU OYAMBA.

Kudziwa ndondomeko za kholola lauzimu pakokha sikokwanira. Nkoyeneranso kuti mudziwe njira ndi zipangizo zokololera. Ndongomeko ndi njira yomwe mungagwiritsire ntchito zomwe mwaphunzira. Mukuyeneranso kugwira ntchito ya Mulungu m'mene Iye akufunira. Njira yake ya bvumbulutso lochoka kumwamba ndipo zotsatira zake ndi kubalana ku uzimu.

ndipo makutu ako adzamva mau kumbuyo kwa iwe akuti, Njira ndi iyi, yendani inu m'menemo: potembenukira inu kulamanja, ndi potembenukira kulamanzere. Ndipo mudzaipitsa cokuta ca mafano ako, osema asiliva, ndi comata ca mafano ako osungunula agolidi; udzawataya ngati kanthu konyansa, udzati kwa iwo, Cokani. Ndipo Mulungu adzapatsa mvula ya mbeu yako, ukaibzale m'nthaka; ndi mkate ndiwo phindu la nthaka, ndipo tirigu wace adzaca bwino ndi kucuruka; tsiku limenelo ng'ombe zako zidzadya m'madambo akuru (Yesaya 30:21-23).

Kumeneku ndiye kukolola ndi bvumbulutso lochokera kwa Mulungu osati ndi njira za munthu.

ADINDO A CHINSINSI

Okhulupirira ndi adindo a “zinsinsi za Mulungu”. Mdindo ndi munthu yemwe amayang'anira zinthu mwalo mwa wina. Chinsinsi ndi chinthu chosadziwika ndi anthu ena. Mulungu watituma kuti:

ndi kuwalitsira onse adziwe makonzedwe a cinsinsico, cimene cinabisika ku yambira kale kale mwa Mulungu wolenga zonse; kuti mu Eklesia azindikiritse

tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu, monga mwa citsimikizo mtima ca nthawi za nthawi, cimene anacita mwa Kristu Yesu Ambuye wathu: (Aefeso 3:9-11)

Mulungu waulula ku mpingo chinsinsi cha chipulumutso kupyolera mwa Yesu Khristu. Kupyolera ku mpingo Iye waulula chinsinsi chimenechi kudziko lonse:

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko (Aefeso 1:9-10).

Mpingo ndi chida chomwe chinsinsi cha Mulungu chimaululukirako kwa anthu ochimwa. Cholinga chathu ndicho “kututa mwa bvumbulutso.”

MBEU IDZAMUPULUMUTSA IYE

Kholola la kudziko la kuthupi limakhazikika pa mfundo yochulukitsa. Mbeu yafesedwa ndipo imabereka zokolola. Mkatikati mwa chipatso chokololedwa mmakhalamo mbeu yoti idzadzalidwense.

Ndipo dziko lapansi linamera mwa mtundu maudzu, therere lobala mbeu monga mwa mtundu wake... (Genesis 1:12)

Mbeu zimenezi zinthu kuchulukitsidwa ndikubweretsa kholola wina. Mchitidwe umenewu ngosatha. Pa zochitachita zathupi m'mapezeka choonadi chopambana chazimu. Ndichimodzi mwa chifukwa chimwene Yesu anagwiritsa ntchito kholola pofuna kuwonetsera masomphenya ofikira dziko lonse ndi Uthenga Wabwino.

Monga momwe chiliri chipatso kapena njere yomwe yakololedwa imakhala nkuthekera koberekaso mudziko la kuthupi, izi zili chimodzimodzi ku dziko lauzimu.

Yesu anafaniziridwa ngati mbeu:

Malekezero onse a dziko lapansi adzakumbukira nadzatembenukira kwa Yehova: Ndipo mafuko onse a amitundu adzagwadira pamaso panu. Mbumba ya anthu idzamtumikira; kudzanenedwa za Ambuye ku mibado yakudza. (Masalimo 22:27, 30).

Pamene Yesu anafa pamtanda chifukwa cha machimo a anthu onse, mbeu ya moyo wake inabzalidwa. Ndipo yabweretsa kholola lochuluka kwambiri chifukwa anthu ambiri apulumutsidwa kuchoka ku machimo awo ndikuchoka ku imfa kupita kumoyo. Aliyense obadwanso mwatsopano alingatati mbeu ku dziko la kuthupi. Mkati mwa aliyense muli moyo ndiponso kuthekera kobereka.

DZIKO LINAFLIKILIDWA

Anali masomphenya akulu omwe Yesu anawatsimikizira omutsatira ake. Munda wa kholola unafalikira msanga kuposa iwo. Analibe njira zamakono monga za zolembalemba, ma wailesi, kanema ndi makompyuta zomwe zimawathandiza pa ntchito zawo. Analibe njira zoyendera mwachangu monga mabasi, galimoto, masitima kapenanso ndege. Koma Baibulo linalimba kuti mwakamphindi kochepe analitembenuza dziko lapansi mwa mphamvu ndi Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu.

Pamene sanawapeze anakokera Yasoni ndi abale ena pamaso pa akulu a mudzi, napfuula kuti, Omwe aja asanduliza dziko lokhalamo anthu afika kunonso (Machitidwe 17:6).

Masomphenya anakwaniritsidwa ndi anthu omwe anamvetsetsa bwino njira za Mulungu za kachulukitsidwe komanso kholola lauzimu.

Pa dziko lonse lapansi kuli kholola wauzimu amene wacha koma miyoyo ikuonongeka ngakhale kuli njira za makono. Izi ziri choncho chifukwa ambiri sanamvetsetse bwino njira ndi zipangizo zokololela zomwe zacha mu bvumbulutso la kholola.

NJIRA

Mpingo makono ano wayesetsa njira zambiri pa kufalitsa Uthenga Wabwino ndi kuwonjezeranso chiwerengero cha anthu a mu mpingo pogwiritsa ntchito mipikisano, mphoto, ndi zochitika zina za paderadera ndi cholinga cholinga chokopa gulu la anthu. Wagwiritsa ntchito machitachita ambiri omwe amapangidwa ndi munthu ndi cholinga kuti akwaniritse ntchito yauzimu. Ntchito ya uzimu imayenera kuchitika ndi njira za uzimunso. Mulungu sangasiye omutsatira ake kuti akakwaniritse masomphenya popanda kuwapatsa njira yoti izi zitheke.

Njira ikhoza kuoneka kudziko lauzimu yomwe ndi yofanana ndi chipatso cha kholola yomwe iri ndi kuthekera kodzaberekanso. Zimenezi zafotokozeredwa mwachidule mu 2 Timoteo 2:2:

Ndipo zimene wazimva Kwa ine mwamboni zambiri, zomwe uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphuzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)

Dziko silinangofikiridwa ndi ophunzira khumi ndi awiri okha a Yesu Khristu. Aliyense ohulupirira amabereka aKhristu. Dziko lero silifikiridwa atumiki omwe ndi akachenjede ndi mamishonale. Anthuwa ngosakwanira. Mwa anthu 100 pa mpingo, 99 amakhala anthu wamba. Awa ndi ogwira ntchito amene akuyenera kulimbikitsidwa ngati tikufuna kufikira miyoyo ya anthu yokwana 3 billion ndi uthenga wa Yesu.

Baibulo limanena za chizunzo chachikulu chomwe mpingo woyamba unakumana nacho ku Yerusalemu ndipo:

Ndipo tsikuli kunayamba kuzunza kwakukulu pa mpingo anabalalitsidwa onse m’maiko a Yudeya ndi Samariya, koma osati atumwi ai. Pamene ndipo iwo akubalalitsidwawo anapita nalalikira mauwo (Machitidwe 8:1,4).

Atumwi, amene anali atsogoleri a mpingo ndipo analinso atumiki okhazikika, anatsala ku Yerusalemu. Anali okhulupilira omwe anabalalika napita ponseponse kulalikira mau. Okhulupirira aliyense amabereka ophunzira ena ndi kuwaphunzitsa za mu Ufumu wa Mulungu. Amene anabalalikawo anali asodzi, opanga matenti, ndi ntchito zina ndi zina, koma cholinga chawo chinali kufalitsa Uthenga Wabwino.

Pamene Paulo akazuka mpingo woyamba kunalembedwa kuti sikuti ankangopita kulowa mmakachisi mokha. Amapitanso m’nyumba kukagwira okhulupirira (Machitidwe 8:3). Izi zinali chonchi chifukwa nyumba iriyonse inali bwalo la kholola lauzimu. Pamene okhulupirira aliyense akubala ndiye kuti nyumba ili yonse imasanduka kukhala malo olalikira uthenga., kutseka makomo akachisi sikungaletse kafalitsidwe ka Uthenga Wabwino.

Monga mmene zinaliri ndi mpingo woyamba kuti ankabala, ndiye kuti nyumba iriyonse inali ndi cholinga chapaderadera.

Mwachitsanzo, zochitika zotsatirazi zinachitika makomo a okhulupirira:

- Machitidwe 2:1, 46: Pentekosite anachitikira mu chipinda chapamwamba cha nyumba. Itachitika pentekositi okhulupirira anakuma tsiku ndi tsiku m’nyumba.
- Machitidwe 9:11, 17 - Ananias anapita ku nyumba ya Yudas ndipo anakamtumikira Paulo. Izi zinapangitsa kuti Uthenga Wabwino ukafikense kwa amitundu.
- Machitidwe 10-11: Pamene Petulo anali kupemphera m’nyumba analandira bvumbulutso lomwe linathandiza kuti Uthenga Wabwino ukafikense kwa amitundu.
- Machitidwe 12:12; 16:15, 21-24, 40: Mapephero a okhulupirira ankachitikira ku nyumba ya Maria, Roda, Jarius.
- Machitidwe 20:20: Paulo sankangophunzitsa m’ mabwalo okhaokha komanso ankaphunzitsa m’nyumba.
- Machitidwe 21:8-14: Bvumbulutso la uneneri linaperekedwa kwa Paulo mmene anali m’nyumba ya Filipo.
- Machitidwe 28:30-31: Paulo analalikira ndi kuphunzitsa m’nyumba yobwereka.
- Aroma 16:5; 1 Akorinto 16:15, 19; Akolose4:15; Filemoni 2: Zikuwonetsa kuti mapemphero ankachitikira m’nyumba ya Prisila ndi Akula, Stefana, Nemfa ndi Akripo.

Nyumba iliyonse inali malo a kubala kwa uzimu. Okhulupirira aliyense ankabereka.

M'nyumba yanu sikuyenera kukhala malo omenyera nkhondo ya chitetezo chazimu okha ngakhale kuti mukuyenera kutetezedwa ku chiwembu cha adani. Ikuyenera kukhala malo olimba omenyerako nkhondo ya uzimu pakupititsa Uthenga Wabwino patsogolo ndi kupindula dera la mdani kuti likhale la Mulungu.

KUPHUNZITSA MMODZI KUTI AKAFIKIRE MMODZI

Njirayi ndi yophweka kwambiri: okhulupirira aliyense amabala okhulupirira wina, kuphunzitsa anthu okhulupirika omwe angathe kukaphunzitsa enanso. Monga mmenenso zimachitika m'dziko la kuthupi pa kholola wachipatso, zochitazichita nzosatha. Zotsatira za ndondomeko imeneyi nzosavuta kuzimvetsa kwake makamaka tikaona m'mene mpingo oyamba unatembenezira dziko ndi Uthenga Wabwino.

Onani tchati pa tsamba lotsatira. Tchati imeneyi imagwiritsa ntchito nthawi ya pachaka yomwe ndiyabwibwino kufikira munthu ndi Uthenga Wabwino ndi kuphunzitsa iye kuti akathe kubala m'Khrisitu. Zoona zake nzakuti, ndondomekoyi itha kutenga nthawi yaitali kapena ayi molingana ndi anthu omwe akukhudziwa.

Koma kugwiritsa ntchito chaka chimodzi ngati nthawi yoikidwa, ngati okhulupirira angafikire munthu m'modzi ndi kuwaphuzitsa ndi kulonjeza kuti pachaka aziphunzitsa munthu m'modzi, dziko lonse lapansi bwezi Uthenga Wabwino utafalikira kale. Tchati ikusonyeza kuti pachaka choyamba m'Khrisitu akuphunzitsa munthu m'modzi. Kumapeto a chaka chimenecho, kukukhala anthu awiri okhulupirikano (okhulupirira komanso munthu yemwe waphunzitsidwa)

Pofika chaka chamawa, yense mwa iwo afikirensa munthu mmodzi mmodzi. Pozatha chaka chachiwiri, pazakhala anthu anai, ndipo awanso akafikira munthu mmodzi mmodzi mu chaka chotsatiracho. Muyang'ane bwino bwino pamwamba pa tchatipo, ndi kulingalira zotsatira zake za ndondomeko imeneyi ngati ingatsatidwe kwa zaka zambiri.

Ngati inu ndinu chiwalo cha mpingo, mutengo chiwerengero cha anthu onse amupingo wanu ndipo chulukitsani ndi 131,072. Yankholo ndi chiwerengo chomwe mpingo wanu ukuyenera kukolola mu zaka 17 zotsatirazo ngati chiwalo chilichonse chikubala.

OPHUNZITSA	OPHUNZIRA	CHIWELENGO CHONSE
CHAKA 17 65,536	65,536	= 131,072
CHAKA 16 32,768	32,768	= 65,536

CHAKA 15	16,384	16,384	=	32,768
CHAKA 14	8,192	8,192	=	16,384
CHAKA 13	4,096	4,096	=	8,192
CHAKA 12	2,048	2,048	=	4,096
CHAKA 11	1,024	1,024	=	2,048
CHAKA 10	512	512	=	1,024
CHAKA 9	256	256	=	512
CHAKA 8	128	128	=	256
CHAKA 7	64	64	=	128
CHAKA 6	32	32	=	64
CHAKA 5	16	16	=	32
CHAKA 4	8	8	=	16
CHAKA 3	4	4	=	8
CHAKA 2	2	2	=	4
CHAKA 1	1	1	=	2

Mulungu nthawi zonse amagwiritsa ntchito amuna ndi akazi kuti akwaniritse cholinga chake. Ndongomeko ya Mulungu pakholola imafuna amuna. Munthu amasakasaka njira yabwino, koma Mulungu akufuna amuna abwino. Dziko limatenga amuna omwe alindi luso ndipo limawaptsa makhalidwe. Mulungu amatenga amuna amakhalidwe, okhulupirika ndipo amawapanga kukhala ndikuthekera.

Cotero munthu atiyese ife, monga atumiki a Kristu, ndi adindo a zinsinsi za Mulungu. Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika. (1Akorinto 4:1-2)

Sizikutengera kuti ndinu ophunzira kapena muli ndi luso. Chofunika nchakuti bolani ngati muli okhulupirika.

Amuna ndi akazi okhulupirika amapereka Uthenga Wabwino kwa amuna ndi akazi okhulupirikanso omwe ali nkuthekera kokaphunzitsa ena... Limeneli ndiye bvumbulutso la Mulungu pakututa kholola.

CHIDA

Kudziko la ku thupi sikuli ndondomeko zokha za kholola ndi njira zogwiritsira ntchito ndondomekozi, koma kulonso zida zokololela. Zida zimenezi zinayambira zophweka monga chikwawa mpakana kufikira makina amakono.

Mulungu waperekaso chida cha kholola la uzimu. Yesu anati:

Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine kumwamba ndi pa dziko lapansi.

Mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse...

Ndikuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo

onani Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansu. (Mateyu 28:18-20)

Pali zinthu zinai zofunika zokhudzana ndi mau akuti “onse” m’ndimeyi. Okhulupilira atumidwa kuti:

- Kuphunzitsa anthu a mitundu yonse
- Zinthu zonse

Ntchito ziwiri izi ndi udindo wathu. Ndi chidule cha masomphenya a kholola.

Udindo wa Mulungu ndi:

- Kupereka mphamvu kwa zonse kuti tikwanitse ntchito yathu.
- Kukhala nafe nthawi zonse (mu njira yonse).

Yesu anawauza ophunzira ake:

Komatu muzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m’Yerusalemu, ndi m’Yudeya lonse, ndi m’Samariya, ndi kufikira malekezero ake adziko. (Machitidwe 1:8)

Mphamvu za Mzimu Woyera ndi chida chomwe Yesu anawapatsa ophunzira ake kuti akakwanitse ntchito ya masomphenya a kholola. Kuti zikapindule, njira ya kuchurukitsa ikuyerena kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera.

Ambiri amalandira madalitso a Mzimu Woyera, amamva kudzodza, amakondwera, ndiposo amayankhula malilime ena. Koma umboni weni weni wa Mzimu Woyera sikungodalitsika kokha

kapena kuyankhula malilime osadzwika. Umboni weni weni ndi wa mphamvu ya Mzimu Woyera. Sikuti ndi mphamvu za ndale, kapena mphamvu za kuthupi. Izi ndi mphamvu za uzimu.

Simukuyenera kukhutitsidwa pongolandira madalitso a Mzimu Woyera. Mukuyenera kupita mupyola madalitsowo kukafikira bvumbulutso la mphamvu za Mulungu.

MPHAMVU ZOTSOGOZEDWA

Mphamvu zosatsogozedwa ndi zoopsya. Chimodzimodzinsu kayendedwe ka mathithi omwe amatipatsa madzi ndi mphamvu akhoza kuwononga mudzi onse ngati salondoleredwa bwino.

Mphamvu zomwe Yesu anabveka omutsatira Iye zinali mphamvu zotsogozedwa kuti zikawapangitse iwo kutha kuchitira umboni ku dziko lonse lapansi. Chinali chida chomwe amayenera kugwiritsa ntchito kuti akakwaniritse maso mphenya.

Mulungu ndiye mwini mphamvu zimenezi:

Mulungu ananena kamodzi; kachiwiri ndinamva izi, kuti mhamvu ndi Yake ya Mulungu. (Masalimo 62:11)

Okhulupirira analamulidwa kuti alandire mphamvu imeneyi:

Khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba. (Luka 24:49)

Mau akuti “kubvekedwa” akutathauza kuvekedwa ndi mphamvu. Mulungu akufuna kukukutani kuuzimu ndi mphamvu zake kuti izi zikakupangitseni kuchitira umboni ku dziko.

CHOLINGA CHA MPHAMVU

Mphamvu za Mzimu Woyera ndizofunika chifukwa zimakupangani inu kukhala mboni ya mphamvu chifukwa ndi mau a mphamvu.

Mphamvu zake zidzatenga mau omwe muyankhule nkuwapanga kukhala opindulitsa:

...Chifukwa mau ake anali ndi ulamuliro...Ndipo anthu onse anadadwa, nalankhulana wina ndi mnzache, nanena mau amenewa ali otani? Chifukwa ndi ulamuliro ndi mphamvu angolamula mizimu yonyansa, ndipo ingotuluka. (Luka 4:32, 36)

Mphamvu zake zimatsimikiza mau:

Ndipo iwowo anaturuka, nalalikira ponse ponse, ndipo Ambuye anachita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikiro zakutsatapo. (Mariko 16:20)

Mulungu mau ake amatsikimizika ndi zizindikiro zomwe zimawatsatira. Simungadikire kuti chizindikiro chachozizwa chichitika musanayambe mwagawa Mau a Mulungu. Muyambe kaye kugawa mau ake ndipo Iye adzagwira nanu ntchito ndi kutsimikiza mau omwe muziyankhula.

Tangoganizani zotsatira zofalitsa Uthenga Wabwino ngati okhulupirira aliyense angachitire umboni ndikutinso mtumiki aliyense akuchita akuonetsa zizindikiro za mphamvu zotsimikizira pamene mau alalikidwa. Izi ndi zomwe mphamvu zimachita:

IMABWERETSA MACHIRITSO:

Mphamvu yake izakhala nanu kuti mukachize:

Ndipo mphamvu ya Ambuye inali ndi Iye kuwachiritsa. (Luka 5:17)

IMABWERETSA MAMASULIDWE:

Pamene mukulowa m'munda wa kholola wa dziko, mphamvu ya Mulungu idzabweretsa mamasulidwe kwa onse ozunzika.

Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ake khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi ya kuchiza nthenda iri yonse ndi zofooka zonse. (Mateyu 10:1)

IMAPEREKA CHITETEZO:

Mphamvu ya Mulungu imakutetezani pomwe mukumugwilira ntchito.

Taonani ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira... (Luka 10:19)

IMATSIMIKIZIRA UTHENGA WABWINO

“Kutsikimiza” kumatanthauza kuti kuonetsera china chake. Mphamvu za Mulungu zimawonetsera zoonza zeni zeni za Mau a Mulungu.

Ndipo khamu lalikuru la anthu linamtsata Iye, chifukwa anaona zizindikiro zimene anachita pa odwala. (Yohane 6:2)

Zozizwa zomwe Yesu anachita ndizomwe zinachititsa anthu kuti abwere kwa Iye.

Amuna ndi akazi sadzatsata Uthenga Wabwino chifukwa cha bungwe, mpingo, kapenanso mlaliki otchuka. Adzabwera chifukwa chakuwonetseredwa kwa mphamvu za Mulungu wa moyo.

IMATSOSGOLERA ANTHU KWA MULUNGU:

Paulo analemba kuti:

Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'chionetso cha Mzimu ndi cha mphamvu;

Kuti chikulupiriro chanu chisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:4, 5)

Paulo anali ndi maphunziro abwino kwambiri ndipo anakatha kumayakhula ndi nzeru za anthu. M'malo mwake anatumikira ndi mphamvu ya Mulungu ndi ndikuonetsera Mzimu Woyera.

Cholinga chake chinali nchiani? Kuti chikhulupiriro cha anthu chisakhazikike pa nzeru za anthu koma pa mphamvu ya Mulungu.

MPHAMVU ZONSE

Yesu anati:

Taonani ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira, ndi pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo. (Luka 10:19)

Mphamvu zonse zinapatsidwa kwa Yesu (Mateyu 28:18). Kudzera mwa Mzimu Woyera wapereka mphamvu zimezi kwa okhulupilira. Pamene mukulowa m'munda wa kholola njira yanu ndiyochulukitsa. Chida chanu ndi mphamvu.

KUTENGA MPHAMVU

Lonjezani lilironse la Mulungu liri ndi mbali ziwiri: Lonjezani komanso kutenga mphamvu.

Yesu analonjeza mphamvu zonse. Inu udindo wanu nkuvomera kutenga mphamvu zimenezi. Kuti zimenezi zichitike mukuyenera:

KUZINDIKIRA KUTI ZIMENEZI NDI ZALERO:

Mu Yohane 11 pamene Yesu anabwera kudzamuukitsa Lazaro kwa akufa, Malita anakumana naye ndipo anati:

Ambuye mukanakhala kuno mlongo wanga sakadafa. (Yohane 11:21)

Yesu ananena naye:

Mlongo wako adzauka. (Yohane 11:23)

Marita ananena ndi Iye:

Ndidziwa kuti adzauka m'kuuka tsiku lomariza. (Yohane 11:24)

Yesu anayakha ndi mau omwe alinso ndi mfundo ya mphamvu kwambiri:

Ine ndine kuuka ndi moyo: wokhulupirira Ine, angakhale amwalira adzakhala ndi moyo. (Yohane 11:25)

Marita amakhulupilira kuti mlongo wake bwezi atachiritsidwa kukhala kuti Yesu anabwera msanga. Koma amakhulupilira kuti mlongo wake adzaukitsidwa ku chiukitso chikubwera kutsogolo.

Koma pamene Yesu anagwiritsa ntchito mau akuti “Ine ndine” pomuyakha Marita anakabvumbulutsa chithu chofunika kwambiri. Kulibe kuti izi ndi zam'mbuyo kapena zam'tsogolo pa tsiku lomwe chozizwa chitachitike. Mu nthawi iriyonse pamakhala mphamvu yokumana ndi zosowa za anthu. Mu nthawi iliyonse Mulungu ndi (Ine Ndine); wokwanira kukumana ndi zosowa. “Maira, lero ndi tsiku la chozizwa. Ine Ndine (ndi zomwe zikuchitika pano) Kuuka ndi Moyo.”

Pali ena omwe amati masiku a zozizwa anapita kale. Awa amakhala kuti sakulandira mphamvu ya Mzimu Woyera. Mau a Mulungu amawachenjeza onse oterewo...

Akukhala nao maonekedwe a chipembedzo, koma mphamvu yake adaikana; kwa iwonso udzipatule.

Mamasuliridwe ena anamasulira kuti okhala nawo mawonekedwe chipembedzo koma “alendo ku mphamvu yake.” (2 Timoteo 3:5)

Alingati mtengo wamkuyu omwe Yesu anautembelera. Ali nawo maonekedwe a Umulungu kunja kwao koma alibe chipatso chilichonse. Monga ngati mtengo wa mkuyu ulibe madzi omwe amazungulira omwe amapangitsa kuti ubale chipatso, alibe mphamvu ya Mulungu yomwe imayenda mwaiwo ndipo kuuzimu samabereka.

KUMVETSETSA GWERO

Gwero la mphamvu ya Mulungu:

Ine Ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake: wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu.

Ngati mukhala mwa Ine, ndi mau anga akhala mwa inu, pemphani chimene chiri chonse muchifuna ndipo chidzachitika kwa inu. (Yohane 15:5, 7)

Inu ndi nthambi. Yesu ndi mpesa. Moyo umachokera ku mpesa. Nthambi imangobereka chipatso. Simupanga chipatso koma m'mangobereka icho.

Yesu ndi amene amagwira ntchito yonse. Pamene Yesu anafunsidwa, “kodi tingatani kuti tithe kugwira ntchito ya Mulungu?” Sanawaphunzitse za machiritso ochokera kumwamba kapena kuwaonetsera mmene azipangira zozizwa. Yesu anayankha:

**Ntchito ya Mulungu ndi iyi kuti mukhulupirire Iye amene Iyeyo anamtuma.
(Yohane 6:29)**

Iyeyo anali ntchito ya Mulungu. Anali gwero la mphamvu, chozizwa, ndi machiritso.

Mphamvu sili mwa munthu kapene china chirichonse chomwe munthu ali nacho. Kukwaniritsa kwa lonjezo la mphamvu liri mwa Mulungu Iye mwini ndi Mau ake.

Yesu ndi mpesa omwe umapereka nthandizo. Iye ndi anthu amene tili nthambi. Kuchokera ku mpesa kuyenda mphamvu imene imapangitsa kuti masomphenya kuti akwaniritsidwe.

KUMVOMEREZA ULAMULIRO

Pamene mwapatsidwa udindo kuti muchite china chake mukuyenera kukhalanso ndi ulamuliro ochitira zimenezi.

Yesu anawatsa ophunzira ake ntchito yokolola komanso anawapatsa ulamuliro kuti akakwanitse ntchito imeneyi, koma monga munthu aliyense akuyenera kuvomera ulamuliro umenewu. Yesu anati “mphamvu zonse” (ulamuliro) zinapatsidwa kwa Ine. Wapereka mphamvu [ulamuliro] kwa inu. Mukuyenera kuvomera ndi kugwiritsa bwino ntchito kuti uthenga ufalikire.

Okhulupirira akuyenera kuzindikiranso mphamvu imeneyi mu mpingo mwawo. Mufanizo lomwe Yesu anapereka. Anati:

Pita msanga, pita kumakwalala ndi kunjira za mudzi, nubwere nao muno aumphawi ndi opunduka ndi akhungu ndi otsimphina.

Turuka, nupite kumiseu ndi njira za kuminda, nuwaumirize anthu alowe, kuti nyumba yanga idzale. (Luka 14:21, 23)

Cholinga cha Mulungu pa mpingo ndi chakuti mpingowo ukhale chida choonetsera mphamvu yake.

Munthawi zambiri mpingo wakhala malo ongosangalatsa basi, kapena malo achisangalalo chabe.

Ngati tiribe mphamvu ya Mulungu imene imayenda m'mpingo mwathu, ndiye kuti osauka, akhungu, ndi onse omwe ataika mu uchimo atuluka kudzera pakhomo pathu koma asanasinthe. Apita m'mene anabwelera, osasinthabe.

Mpingo umapangidwa ndi anthu. Ngati ukufuna kuti umve mphamvu ya Mulungu, nkoyenera kuti mamembera nawo alandire mphamvu imeneyi paokha-paokha.

PETRO: KALE NDI TSOPANO

Mphamvu ya Mulungu ndi chida chomwe chidzakusintheni kuchokera ku wokolola wosapindula kukhala munthu wodziwa kukolola kudzera mu bvumbulotso la kholola. Talingalirani chitsanzo cha Mtumwi Petro.

Tikumuona Petro akugona mu nthawi ya utumiki wa Yesu Khristu (Mariko 14:32-34). Tikumuwona Petro wa mantha kumukana Yesu kuti samudziwa (Mateyu 26). Tikuona munthu yemwe anatembenekira ku maitanidwe a kholola komanso kuti akhale msodzi wa anthu. Analondola zilakolako zake (Yohane 21).

Koma mwadzidzidzi pakuphulika zolemba za Baibulo zokhudzana ndi Petro watsopano. Kwa nthawi yoyamba yomwe munthu uyu anayakhula molimba mtima za Uthenga Wabwino, 3,000 anapulumutsidwa. Mmene analarikiranso kachiwiri 5,000 anaonjezereka ku mpingo. Chinachitika chiani kuti munthu uyu wothawa, wochokapo, munthu wotemberera kukhala mtumiki wamphamvu wa mpingo oyamba?

Petro analandira mphamvu. Zinali mphamvu zinampangitsa kuti anene kwa olumala:

Ndipo Petro, pompenyetsetsa iye pamodzi ndi Yohane, anati, Tiyang'ane ife. Koma Petro anati, Siliva ndi golidi ndiribe; koma cimene ndiri naco, ici ndikupatsa, M'dzina la Yesu Kristu Mnazarayo, yenda, Ndipo anamgwira Iye ku dzanja lace lamanja, namnyamutsa; ndipo pomwepo mapazi ace ndi mfundo za kumapazi zinalimbikitsidwa. (Macitidwe 3:4,6-7)

Sungamuuze munthu oti akuvutika kuti “tiyang'ane” pokhapokha ngati ukudziwa kuti uli nkathu koti umuthandizire pa bvuto lakelo. Sungamugwire munthu olumala ndi dzanja kumuimiritsa, pokhapokha ngati ukudziwa kuti uli ndi mphamvu zoposa zako. Petro payekha analibe kanthu koma anali ndi mphamvu za Mulungu zomwe zimayenda mwa iye. Mphamvu za Mulungu zinawayendetsanso olumala, sizinangowathandiza kuti asiyane nazo nyengo zolumalazo.

Kukumana ndi mphamvu kunasintha asodzi ngati Petro kukhala asodzi anthu.

KUKUNZA MALIRE

Yesu ananena ndongosolo lokulitsira malire lomwe ndi zotsatira kuchokera ku mphamvu zochitira umboni Uthenga Wabwino.

Komatu muzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ake adziko. (Machitidwe 1:8)

Ndondomeko ya kholola inaotseredwa mu mau Ake:

- Njira yake ndi kuchulukitsa.
- Chida chake ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.
- Mphamvu zinatsogozedwa. Zinapatsidwa kuti ziwapange ophunzira kukhala mboni.
- Chandamale cha mphamvu chinali kufikira maiko onse a padziko, kukulitsa malire...Yerusaremu, kenako Yudeya, Samariya, ndi kufikira ku malekezero ake a dziko.

Kuyambira komwe anali, pogwiritsa ntchito njira yochulukitsa ndi chida cha mphamvu, Uthenga Wabwino unakafalikira ku malekezero a dziko.

KUTENGA LONJENZANO

Lonjezani kawirikawiri limanenedwa ndi okhulupilira:

...Taonani, Ine ndiri nanu masiku onse, kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansipano (Mateyu 28:20).

Kwa onse amene akufuna kuona masomphenya...kwa onse akufuna kupita ndi mphamvu zokachitira umboni ku maiko.... Kwaiwo walonjeza...Ndiri nanu munjira yonseyi...

MAYENSO ODZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yomwe munaloweza.

2. Kodi ndi malemba ati omwe akuwonetsa ndondomeko ya Mulungu yochulukitsa?

3. Kodi chida cha kholola nchiani?

4. Lembani ndondomeko zitatu zotengera lonjezano la mphamvu.

POPITIRIZA KUPHUNZIRA

Njira ya Mulungu yochulukitsa yaperekedwa mu 2 Timoteo 2:2 ndipo inayenera kugwiritsidwa ntchito koyamba ku Yerusalemu ndi kufalikirano ponse ponse pa dziko lapansi. Mukuyenera kuyamba kututa kholola kuyambira pomwe mulipo ndipo kenako Mulungu adzakulitsa masomphenya ndi utumiki wanu. Zotsatirazi zikuthandizani: “Kukolola mwa chikhulupirilo” m’Yerusalemu wanu.

1. Muphunzire buku la Yoswa. Muone ndondomeko zomwe Mulungu anampatsa Yoswa kuti Israeli akakwanitse kutenga dziko la Palestina. Kodi mungathe kugwiritsanso ntchito ndondomeko zimenezi kuti mukathe kutenga dera lanu kwa Mulungu?
2. Mukhale ndi zolinga zoti mufikire dera lanu ndi Uthenga Wabwino. Zolinga ndi ndandanda wa zolinga zanu. Muzachita chani? Kufikira mpakana liti? Musankhe cholinga chomwe chikuthandizeni kuti mufikire anthu ndi Uthenga Wabwino konse komwe sunafikeko. Ichi ndiye chinali cholinga cha Paulo mu Aroma 15:20-21. Ndongomeko zina mukhoza kuzilingalira.
 - Yendereni nyumba iriyonse m’dera lanu ndi kugawa Uthenga Wabwino kwa omwe okuyandikirani.
 - Mukhazikitse ndondomeko ya za chuma yoti muzipereka ku mpingo wa pamalo komanso ku malalikidwe akunja.
 - Muzitha kutumikira ku magulu omwe ali ochepa mu dera lanu omwe sanafikiridwe ndi Uthenga Wabwino.
 - Muyambitse utumiki wa paderadera malo opumiramo, ndende, kapena m’zipatala. Muyambitse utumiki kwa anthu omwe azolowera mankhwala ozunguza bongo, kwa a umphawi, zidakwa, kapena kwa amai omwe sali pa banja. Tumikirani kwa anthu opatulika monga amai, abambo, ana, mabanja kapena kwa asilikari akhondo.

3. Kuzanu utumiki wanu kuchoka ku “Yerusalemu wanu kufikira ku maiko a padziko lapansi. Yambani kulowa maiko kudzera mumapemphero.

- Pezani mapu a dziko lapansi ndikuyamba kupemphelera maiko a padziko lapansi. Tengani achikunja ngati cholowa chani ndipo mumuthokoze Mulungu pokupangani inu kuti mukakhale dalitso ku maiko.
- Ngati mumapeza nyuzi pepala ya tsiku ndi tsiku, muzipemphelera mitu ya nkhani yomwe ikukamba za mabvuto omwe ali m’maiko osiyanasiyana. Mupemphelere atsogoleri a maiko, mamishonale, atumiki ndi abale okhulupirira.

GAWO LACHINAYI CHIYEMBEKEZO

Mumakhala mbali ya maso mphenya

CHAPUTALA 9

KUPHWANYA GOLI

ZOLINGA:

Pomaliza chaputala chino mukuyenera kutha:

- kunena magawo atatu agoli la ukapolo.
- kufotokoza magawo atatu a goli la Mulungu.
- kulemba mwa ndondomeko m'ndandanda wa kusiyana pakati pa goli la ukapolo ndi goli la Mulungu.
- kufotokoza cholowa chazimu pomwe goli laukapolo laphwanyidwa.

VESI YOTSOGOLERA:

Idzani kwa Ine nonse akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndizakupumulitsani inu.

Senzani goli langa, ndipo phunzirani kwa Ine; chifukwa ndiri wofatsa ndi wodzichepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu.

Pakuti goli langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wo pepuka. (Mateyu 11:28-30)

MAU OTSOGOLERA

Phunziro iri lakamba za:

- Kuzindikiritsa masomphenya
- Kumvetsetsa lingaliro la cholinga cha masomphenya
- Zolinga za kukwaniritsa masomphenya

Chaputala chomaliza cha phunziro lino limakhudza chiyembekezo chomwe chimakhalapo mukakhala nawo gawo lokwaniritsa masomphenya.

Cholinga cha Mulungu ndikukupatsa mathero a chiyembekezo:

Pakuti ndidziwa malingaliro amene ndilingilira iwe, ati Yehova, malingaliro a mtendere, si achoipa, akukupatsa iwe adzukululu ndi chiyembekezero. (Yeremiya 29:11)

Mathero a chiyembekezo ndi kukwaniritsa masomphenya, kumalizitsa ntchito ya Mulungu.

Chakudya changa ndicho kuti ndichite chifuniro cha Iye amene anandituma Ine, ndikutsiriza ntchito yake. (Yohane 4:34)

Pamene walowa mu chinachake chatsopano, nkoyenera kuti musiyere zakale. Kubadwa kumafunika kusiya chitetezo chomwe chibelekero chimapereka.

Mulungu akutiuzana kuti titenge njira yatsopano ya chikulupiriro:

Musakumbukire zidapitazo, ngakhale kulingalira zinthu zakale. (Yesaya 43:18)

Mwina mwamangidwa ndi ziphunzitsa zomwe zimanena kuti mphamvu ya Mulungu siyofunikanso lero. Mwina mmaganiza kuti ntchito yofikitsa Uthenga Wabwino kumaiko ndi udindo wa atumiki kapena mamishonale okha. Mwina munamangilirika mchikhalidwe kapena chipembedzo chomwe chimakuletseni kuti musagwirane manja ndi thupi la Khristu mmunda wa kholola wa Ambuye.

Koma Mulungu wakupatsani masomphenya atsopano. Mukhala nawo gawo limodzi latsopano lolumikiza antchito auzimu obwera pamodzi ndi kugwirizana ndi cholinga.

NJIRA YAMAKONO YOLUMIKIZANA

Baibulo linalamba zochitika zosiyana kawiri zokhudzana kugwiritsa ntchito ukonde mu dziko lakuthupi zomwe zimaonetsera choonadi chofunika chauzimu.

Koyambilira zinachitika pamene Yesu ankayamba utumiki wake pa dziko lapansi pano ndipo zinalembedwa mu Luka 5.

Ophunzira anakhala akuwedza usiku onse ndipo sanakole kalikonse. Yessu ananena nawo:

Kakhirani kwakuya, nimuponye makoka anu kukasodza (Luka 5:4)

Ndipo Petro anayakha:

Ambuye tinagwira ntchito usiku wonse osakola kanthu, koma pa mau anu ndizaponya makoka. (Luka 5:5)

Pomwe naponya khoka iwo anagwira nsomba zambiri zomwe anazilephera ndipo anaitana anzawo a ngalawa zina kuti adzawathandizire. Kuwedza kunali kochulukira moti nsomba zinadzadza ngalawa zonse moti mpakana zinayamba kumira. Petro anadabwitsika nazo izi koma Yesu ananena naye:

Usaope, kuyambira tsopano udzakhala msodzi wa anthu. (Luka 5:10)

Zimene Petro anagwira ku dziko la kuthupi sizingafaniziridwe ndi zomwe angadzagwire m'dziko lauzimu pamene akhale msodzi wa anthu.

Zangati zomwezi zinachitikaso kumapeto a utumiki wa Khristu mu Yohane 21. Ophunzira anasodza usiku onse koma sanagwire kalikonse. Koma pa lamulo ya Khristu powauza kuti ponyani khoka ka chikena, ndipo anadzadza ndi nsomba. Koma ulendo uno zinali zosiyana ndi poyamba paja. Khoka silinang'ambike ayi.

Cifukwa cace Simoni Petro anakwera m'ngalawa nakokera khoka kumtunda lodzala ndi nsomba zazikuru, zana limodzi, ndi makumi asanu ndi zitatu; ndipo zingakhale zinacuruka kotere, kokha silinang'ambika. Yohane 21:11

Zochitika ziwiri zimenezi zinachitika kudziko lakuthupi, koma zinali zofanana kwa kwambiri ndi ndizoona za kuuzimu. Koyambilira khoka linang'ambika koma kachiwiri silinang'ambike. Kodi chinawasiyanitsa nchiyani?

Khoka loyamba ndi chitsanzo chakugwira ntchito munthu ya yekha. Petro anali msodzi m'zochita zake. Amadziwa bwino njira zakudziko zausodzi, komaso ndi chikhalidwe cha asodzi. Kupyolera mukung'ambika kwa khoka Yesu anamuonetsa kuti kuyesayesa kwa munthu sikungakwaniritse masomphenya ndi ntchito ya Mulungu.

Pamene Petro anazindikira pa ntchito yomwe Mulungu amkamuitanira iye analira:

Luka 5:8, Muchoke kwa ine, Ambuye, chifukwa ndine munthu wochimwa.

Petro anayenera kukhala msodzi wa anthu. Khoka lakale silinakakwanitsa kusunga kholola wochulukira wauzimu. Petro amayenera kusiya makhalidwe a umunthu. Amayenera kudutsa mzere wakulekanitsa pakati pa Ayuda ndi amitundu. Khoka lakale likuyenera kung'ambika ndipo silikuyenera kukhalanso mbali imodzi kuzochitika zatsopano.

Yesu sanabwere kudzaononga zakale, koma kuzazikwaniritsa kudzera mu zatsopano. Sanaononge chilamulo, koma anangowonjezerako tanthauzo latsopano. Sanathetse kupereka msembe zamwazi kumachimo, koma anazakwaniritsa izi kudzera pakukheta mwazi wake omwe ukuchotsa machimo.

Yesu anachenjeza za kuika vinyo watsopano mu chotengera chakale. Chotengera vinyo chakale sichingakwanitse kusunga vinyo watsopano monga ngati mmene zinalirinso ndi khoka silikanakwanitsa kusunga nsomba. Zovuta za kutuma kwakukulu sizingakwaniritsidwe ndi china chirichonse kupatula khoka latsopano mu dziko lauzimu.

Pakati pa kusodza koyamba ndi kwachiwiri, kulumikizana kwatsopano kunapangigwa. Zomwe zinachitika ndi kuwedza kwa kudziko lakuthupiku zinali zofana ndi zomwe zimachitika ku dziko lauzimu.

Zochitika zatsopano za uzimuzi zikhoza kusunga masomphenya amene Yesu anapereka. Koma kuti munthu alowemo, akuyenera kuchoka ku zakale ndi kubwera ku zatsopano. Goli lakale likuyenera kuphwanyidwa. Khoka lakale likuyenera kung'ambika kuti latsopano lithe kusunga bwino bwino.

GOLI

Goli linkagwiritsidwa ntchito kale polumikizitsa nyama pamodzi zikamakagwira ntchito m'munda wa kholola. Maiko ambiri amagwiritsabe ntchito pa zifukwa za ngati zomwezi.

Yesu anayankhulapo za goli pomwe anati:

Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzicepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti 1 gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wo pepuka. (Mateyu 11:28-30)

Masomphenya aperekedwa m'munda wa kholola. Lero mundawu ukuimilira anthu okwana ma bilioni atatu amene alandira Uthenga Wabwino... Ndipo akuti akutitsimikizira kuti liri “lophweka” ndi “lo pepuka”.

Izi ndi chimodzimodzi zomwe akunena. Koma zochita zakale, goli lakale, sizingasunge masomphenya atsopano. Simungakwaniritse mwanokha. Simungachite ndi kuyetsa kwa umunthu. Mukuyenera kukhala mbali imodzi ya machitidwe atsopano ndikumagiliridwa pamodzi ndi Iye.

GOLI LA UKAPOLO

Tonsefe tiri mugoli lofanana. Muli mugoli la ukapolo kapena goli la Mulungu.

Goli la ukapolo liri magawo atatu, mukhoza kukhala mugoli la ukapolo, lodzikonda kapena la munthu.

GOLI LA UCHIMO

Ine ndine Yehova Mulungu wanu, amene ndinakuturutsani m'dziko la Aigupto, kuti musakhale akapolo ao; ndipo ndinatyola mitengo ya magoli anu, ndi kukuyendetsani coweramuka. (Levitiko 26:13)

Goli la Aigupto likutanthauza goli la uchimo. Mukuyenera kuti goli la ukapolo lithyoledwe m'moyo mwanu ngati mukufuna kukhala pansu pa goli la Yesu.

GOLI LA KUDZIKONDA

Goli la ukapolo likhoza kukhala goli lodzikonda:

Pakuti cimene ndicita sindicidziwa; pakuti sindicita cimene ndifuna, koma cimene ndidana naco, ndicita ici. (Aroma 7:15)

Kudzikonda ndi kunyada ndi zitsanzo za goli la kudzikonda.

GOLI LA MUNTHU

Goli la munthu limaikidwa ndi anthu ena:

Inde, amanga akatundu olemera ndi osautsa ponyamula, nawasenza pa mapewa a anthu; koma iwo eni okha safuna kuwasuntha amenewo ndi cala cao (Mateyu 23:4).

Goli la munthu ndikuphatikiza goli la chikumbumtima chotsutsa, miyambo, chipembedzo, kapena makhalidwe ena omwe amaikidwa ndi anthu ena.

Goli la magawo atatuli – la uchimo, kudzikonda, ndi la munthu – limakamba za ntchito yochita kudzipatsa wekha, kulemedwa, ndi kusowa mtendere.

MAGAWO ATATU A GOLI LA MULUNGU

Goli la Mulungu limakamba za kugwira ntchito mochita kugwirizana m'malo moti wina angolamula mokakamiza. Limakankhula za kupepuka m'malo molemera. Ndi goli lopumirapo osati losowetsa mtendere.

Magawo atatu a goli la Mulungu, ndilopweka, lopepuka ndiponso lokhazika mtima:

Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzicepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali woepuka. (Mateyu 11:28-30)

NDONDOMEKO ZITATU ZOLUMIKIZIRA POGUMUKIRA

Yesu anapereka ndondomeko zitatu zolumikizitsira pogumukira pakati pa goli la uchimo ndi goli la Mulungu. Ndi njira yotulukira kuchoka mu zakale kupita ku zatsopano:

Idzani: mukuyenera kubwera kwa Iye mwa kufuna kwanu. Izi zimaononga goli la uchimo.

Senzani: Mukuyenera kusenza goli lake. Pakuchita choncho, goli lokusezetsani munthu limakonongedwa.

Phunzirani: Pophunzira kwa Iye m' maononga goli lodzikonda.

Goli la Mulungu sikuti linangoperekedwa ndi Iye. Nayenso amasenza nawo.

KUPHWANYA GOLI

Ndicholinga cha Mulungu kuti goli lililonse la uchimo, lozikonda, ndi loperekedwa ndi munthu pa moyo wanu liphwanyidwe. Ndikoyenera kutero ngati mukufuna kukwaniritsa masonphenya. Mu mbiri ya Chipangano Chakale, Israele anazunguliridwa ndi adani a asirikali a Suri. Mulungu ananena kwa Aisraeli ndi kulengeza:

Yehova wa makamu walumbira, nati, Ndithu monga ndaganiza, coteru cidzacididwa; ndipo monga ndapanga uphungu, coteru cidzakhala; kuti Ine ndidzatyola Asuri m' dziko langa, ndi pamwamba pa mapiri anga ndidzawapondereza; pomwepo gori lace lidzacoka pa iwo, ndi katundu wace adzacoka paphuzi pao. (Yesaya 14:24-25)

Mulungu ankafuna kuphwanyiratu goli lomwe linali pa khosi pa Israele. Koma cholingachi chinapitirira moposera Israele mpakana kukafika pa dziko lonse.

Umenewu ndi uphungu wopangira dziko lonse; ndipo ili ndi dzanja lotambasulidwa pa amitundu onse. (Yesaya 14:26)

Kodi cholinga cha Mulungu chinali chiani? Cholinga chake chinali choti goli la uchimo liphwanyidwe ku maiko onse.

Machaputala ochepa analemba kuti:

Ndipo mthenga wa Yehova anaturuka, naphaipha m'zitando za Asuri, zikwi zana ndi makumi asanu ndi atatu ndi zisanu, ndipo pamene anthu anauka mamawa, taonani, onse ndiwo mitembo. (Yesaya 37:36)

Mulungu akufuna goli lililonse m' moyo wanu kuti likhale lakufa ngati mtembo. Akufuna kuliononga ndi cholinga choti akubweretseni ku goli lake.

LIDZAPHWANYIDWA BWANJI?

Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, kuti katundu wace adzacoka pa phewa lako, ndi gori lace pakhosi pako; ndipo gori lidzathedwa cifukwa ca kudzoza mafuta (Yesaya 10:27).

- Silidzathedwa ndi chiphunzitso cholamitsa. Silidzathedwa ndi maganizo kapena maphunziro.

- Silizathedwa kudzera mu ulangizi kapena mu bungwe kapenanso mu chipembedzo.
- Lidzathedwa ndi kudzodza kwa Mzimu Woyera amene ali mphamvu ya Mulungu.

Koma cholinga cha Mulungu pophwanya kapena kuthana ndi goli ndi zoposa moyo wanu kukafikira ku maiko onse. Akufuna kuphwanya goli la laukapolo mwa inu ndicholinga choti mukathe kukwaniritsa masomphenya ophwanya goli la maiko onse.

Ndipo Yehova wa makamu adzamuutsira cikoti, monga m'kuphedwa kwa Midyani pa thanthwe la Orebu; ndipo cibonga cace cidzakhala pamwamba pa nyanja, ndipo adzaisamula monga anacitira Aigupto, Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, kuti katundu wace adzacoka pa phewa lako, ndi gori lace pakhosi pako; ndipo gori lidzathedwa cifukwa ca kudzoza mafuta. (Yesaya 10:26-27)

ZOTSATIRA ZAKE POPHWANYA GOLI

Mulungu anati:

Kodi kumeneku si kusala kudya kumene ndinakusankha: kumasula nsinga za zoipa, ndi kumasula zomanga gori, ndi kuleka otsenderezedwa amuke mfulu, ndi kuti mutyole magori onse? Yesaya 58:6

Kenako anatchula zotsatira pophwanya goli:

Pamenepo udzaitana, ndipo Yehova adzayankha; udzapfuula ndipo Iye adzati, Ndine pano. Ngati ucotsa pakati pa iwe gori, kukodolana moipa, ndi kulankhula moipa, ndipo ngati upereka kwa wanjala cimene moyo Iwako umakhumba, ndi kukhutitsa moyo wobvutidwa, pomwepo kuunika kwako. kudzauka mundima, ndipo usiku wako udzanga usana; ndipo Yehova adzakutsogolera posalekai, ndi kukhutitsa moyo wako m'cirala, ndi kulimbitsa mafupa ako; ndipo udzafanana ndi munda wothirira madzi, ndi kasupe wamadzi amene madzi ace saphwa konse. Ndipo iwo amene adzakhala a iwe adzamanga malo akale abwinja; udzautsa maziko a mibadwo yambiri; udzachedwa Wokonza pogumuka, Wakubwezera njira zakukhalamo (Yesaya 58:6-12).

Zotsatira pophwanya goli ukapolo ndi izi:

- Udazindikra Mau a Mulungu. Tidzaitana, ndipo adzayakha, “Ine ndiri pano.” (vesi 9)
- Mudzapambana pokwaniritsa masomphenya. Kuunika kwako kudzauka mu mdima zomwe zikunena za chipambano (vesi 10).
- Ndipo Yehova adzakutsogolera mosaleka. (vesi 11)
- Adzakhala okupatsa m'zosowa zako. (vesi 11)
- Udzakhala opindulitsa. (vesi 11-12)

- Udzafanana ndi munda wothilidwa ku madzi omwe umakhala ndi zipatso. Udzakhala obala ndipo onse omwe uzawabale mu Uzimu azakhala opindulitsa. Azadzuka ndikumangaso zomanga zakale pa maziko woyenera. Mulungu anamulonjeza Israeli ku dziko la kuthupi:

Ndi mitengo ya kuthengo idzapereka zobala zao, ndi nthaka idzapereka zipatso zace, ndipo adzakhazikika m'dziko mwao; ndipo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, nditadula zomangira goli lao, ndi kuwalanditsa m'manja mwa iwo akuwatumikiritsa (Ezekieli 34:27).

Zomwezinsu ziri choncho ku dziko la uzimu. Kuphwanya kwa goli kumabweretsa kupindula mwauzimu. Zochita zakale zinali zosakwana, zong'ambika ndi zopanda kanthu. Sizingasunge kholola lochuluka. Magoli akale a miyambo, chipembedzo, kuyesa wekha, ndi kusakhudzidwa zikuyenera kuonongedwa. Maziko atsopano, magoli atsopano, njira zatsopano ndizofunikira pakulowa pogumukira pakati pa munthu wochimwa ndi Mulungu wolungama. Masomphenya adzakwaniritsidwa ndi amuna kapena akazi amene anakumanapo ndi kudzodza komwe kumaphwanya goli.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera yomwe mwaloweza.

2. Kodi magoli atatu a ukapolo ndi ati?

3. Nenani mau atatu omwe amakamba za goli la Mulungu.

1. Kodi ndi ndondomeko ziti zitatu zomwe mungatsate kuti mukathe kulumikiza pakati pa goli lauchimo ndi goli la Mulungu?

2. Lembani zotsatira zisanu za kuphwanya goli zomwe zalembedwa mu Yesaya 58.

POPITIRIZA KUPHUNZIRA

Kodi ndi magoli ati a ukapolo omwe akukulepheretsani inu kuchita ntchito ya Mulungu?

- Tchimo
- Chipembedzo
- Mantha
- Kusowa luso la chilengedwe ndi kuthekera.
- Chikumbumtima chokutsutsani
- Kuzidalira nokha
- Ndizina: _____

Werengani ndime iyi: Yesaya 14:24-27

Tengani lonjezano ili: Yesaya 10:27

Pempherani pemphero iri:

Ambuye, ndikukuthokozani chifukwa cha masomphenya a munda wa kholola omwe mwabadwitsa mu uzimu wanga.

Ndikukupephani kuti muphwanye goli lililonse la ukapolo m'moya wanga. Mudzina la Yesu, phwanyani goli la _____, _____ ndi _____ (tchulani magoli omwe ali m'moyo wanu)

Ndimangilireni pamodzi ndinu Yesu. Lengani kuthekera kwatsopano mwa ine komwe kudzabweretsa kholola lochuluka.

Ndikukuthokozani chifukwa cha kudzodza komwe kwaphwanya goli lililonse la ukapolo.

Mudzina la Yesu,

Amen

CHAPUTALA 10

KUDALITSA MAFUKO

ZOLINGA:

Pomaliza chaputala chino mukuyenera kutha:

- kunena makhalidwe a uzimu a Abrahamu omwe anampangitsa iye kukadalitsa mafuko.
- kuzindikira kuti inu ndi cholowa cha mapangano a Abraham.
- kumvetsetsa udindo wanu ngati wolowa m'nyumba kuti mukadalitse maiko a dziko lapansi.

VESI YOTSOGOLERA:

Koma ngati muli a Kristu, muli mbeu ya Abrahamu, nyumba monga mwa Lonjezano. (Agalatiya 3:29)

MAU OTSOGOLERA

Abrahamu anasakhidwa ndi Mulungu kuti akhale tate wa mafuko ambiri. Kupyolera mwa iye mafuko onse anadalitsika.

m'mbeu zako mitundu yonse ya dziko lapansi idzadalitsidwa: cifukwa wamvera mau anga. (Genesis 22:18)

Chipangano Chatsopano chimaonetsa kuti okhulupilira onse amapeza cholowa kumapangano omwe Mulungu anampatsa Abraham. Kutu mukhale opeza cholowa zikutathauza kuti munalandira kuchokera kwa iye.

chotero zindikirani kuti iwo a cikhulupiriro ndiwo ana a Abrahamu. Ndipo malembo, pakuoneratu kuti Mulungu adzayesa olungama amitundu ndi cikhulupiriro, anayamba kale kulalikira Uthenga Wabwino kwa Abrahamu, kuti, Idzadalitsidwa mwa iwe mitundu yonse. Kotero kuti iwo a cikhulupiriro adalitsidwa pamodzi ndi Abrahamu wokhulupirikayo. (Agalatiya 3:7-9)

Inu mupeza cholowa chifukwa mwakhala mbeu ya Abrahamu kudzera mwa Yesu Khristu.

Koma ngati muli a Kristu, muli mbeu ya Abrahamu, olova m'nyumba monga mwa Lonjezano. (Agalatiya 3:29)

Ngati mbeu ya Abrahamu ndinunso cholowa cha pangano la chipulumutso. Koma ngati opeza cholowa mwatumidwa kuti mukadalitse mafuko a dziko lonse ndi Uthenga Wabwino.

Mwauzidwa kuti mutenge cholowa chanu:

Undifunse, ndipo ndidzakupatsa amitundu akhale colowa cako, Ndi malekezero a dziko lapansi akhale ako ako. (Masalmo 2:8)

Kupyolera mwa Abrahamu maiko a padziko amayenera kukadalitsidwa. Kupyolera mwa Yesu mafuko ndi cholowa chanunso.

ZOYENEREZA ZAUZIMU

Zotsatitrazi ndi zoyenereza zauzimu zomwe Abrahamu anali nazo zomwe zinampangitsa iye kukadalitsa mafuko a dziko lapansi ndi momwe zoyenerazazi zikugwirizanirana ndi kholola.

ANALONDOLA KWAMBIRI:

Abrahamu anakhulupirira masomphenya omwe Mulungu anampatsa. Anatsikimizika kuti kudzera mwa iye Mulungu adzadalitsa mafuko a dziko lapansi.

Nakhazikikanso mumtima kuti, chimene iye analonjeza, anali nayonso mphamvu yakucicita. (Aroma 4:21)

Kuti masomphenya a kholola akakhale zenizeni, mukuyenera kutsimikizika kwatunthu, Mulungu analonjeza kholola lochuluka. Wapereka ndondomeko ndi njira zake. Inu mwaitanidwa kukhala wantchito okadalitsa mafuko a padziko.

ANAFESA MUZINTHU ZAUZIMU:

Abrahamu anafesa moyo wake onse mu zomwe ziri zosaoneka mu dziko lakuthupi.

Mulungu anampatsa Abrahamu lonjezano la malo okongola, koma choNsecho iye sanapondemo m'dziko limeneri.

Ndipo sanampatsa colowa cace m'menemo, ngakhale popondapo phazi lace iai; ndipo anamlonjezera iye kuti adzampatsa ili, likhale lace, ndi la mbeu yace yomtsatira, angakhale analibe mwana pamenepo. (Macitidwe 7:5)

Dziko lomwe linalonjezedwalo Abrahamu sanaliwone. Linalonjezedwa kwa mwana wamwamuna yemwe analibe. Komabe Abrahamu sanamukaikire Mulungu. Anafesa moyo wake muzochitika za Mulungu ndicholinga choti lonjezano la Mulungu likakwaniritsidwe ku mibadwo yakutsogolo.

Masomphenya a kholola ndi amuyaya. Mukhoza kukhala moyo wanu onse kufesa muzomwe ndizosaoneka. Koma zotsatira zake ndi zamuyaya. Mibadwo yobwera idzadalitsika chifukwa choti inu munakwaniritsa masomphenya.

ANALI WOMVERA KUMAITANIDWE:

Pamene Abrahamu anaitanidwa ndi Mulungu kuti apite kumalo omwe patsogolo azalandire ngati cholowa, iye anamvera:

Ndi cikhulupiriro Abrahamu, poitanidwa, anamvera kuturuka kunka ku malo amene adzalandira ngati colowa; ndipo anaturuka wosadziwa kumene akamukako. (Ahebri 11:8)

Sizokwanira kungoitaniidwa ku masomphenya a kholola. Mukuyenera kuvomera pomvera ku maitanidwe amenewo.

Ndipo Abrahamu anati, Mwana wanga, Mulungu adzadzifunira yekha mwana wa nkhosa wa nsembe yopsereza; nayenda pamodzi onse awiri. (Genesesi 22:8)

ANALI OKONZEKA KUIMA PAYEKHA:

Mulungu anayankhula ndi Abrahamu:

Yang'anani kwa Abrahamu kholo lanu, ndi kwa Sara amene anakubalani inu; pakuti pamene iye anali mmodzi yekha ndinamuitana iye; ndipo ndinamdalitsa ndi kumcurukitsa. (Yesaya 51:2)

Abrahamu anaitanidwe yekha. Anayenera kuchoka dziko la kwawo ndi banja lake poyankha maitanidwewo.

Pamene mwaitanidwa ndi Mulungu kuchipulumutso zimenezo ndi za aliyense yekha yekha. Munthu aliyense akuyenera kuvomera maitanidwe amenewa. Kuitana kokolola munda ndikofanana. Monga Abrahamu, inu mwaitanidwa nokha. Mukuyenera kupanga chiganizo. Kuvomera masomphenya kukhoza kupangitsa kuti muchoke ndi kusiya banja lanu. Mwachidziwikire kudzakhuza kuchoka pakati pa osakhulupilira omwe alibe masomphenya.

ANALI NDI MASOMPHENYA AUZIMU:

Abrahamu anali ndi masomphenya auzimu:

pakuti analindirira mudzi wokhala nao maziko, mmisiri wace ndi womanga wace ndiye Mulungu. (Ahebri 11:10)

Masomphenya ake anakhazikika pa zinthu za uzimu. Masomphenya ake anali mudzi womwe mmisiri wake anali Mulungu. Zinampangatsa iye kukakhala ku dziko la chilendo, kumakhala m'mahema, kulekanitsidwa ndi dziko lakwawo ndi banja. Masomphenya anasintha moyo wake.

Masomphenya a kholola asintha moyo wanu. Simudzakhalaso chimodzimodzi. Musamakhutitsidwe ndi zinthu zosakhalitsa za moyo uno. Muzifuna zokhalitsa.

ANKAMUDZIWA MULUNGU NGATI BWENZI LAKE:

Abrahamu ankatchedwa kuti, “Bwenzi la Mulungu”.

ndipo anakwaniridwa malembo onenawa, Ndipo Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo kudawerengedwa kwa iye cilungamo; ndipo anachedwa bwenzi la Mulungu. (Yakobo 2:23)

Pamafunika pakhale ubwenzi weni weni ndi Mulungu kuti inuyo mukathe kukwaniritsa masomphenya. Mukuyenera kuphunzira njira zake ndikutha kumva mau Ake. Mukuyenera kukhala bwenzi la Mulungu.

ANALI ODZALA NDI CHIYEMBEKEZO:

Paulo anayankhula za Abrahamu:

Ndipo poyang'anira lonjezo la Mulungu sanagwedezeka cifukwa ca kusakhulupirira, koma analimbika m'cikhulupiriro, napatsa Mulungu ulemu. (Aroma 4:20)

Ngakhale analibe mwana wamamuna, Abrahamu analandira lonjezani lokhala tate wa mafuko. Kuthupi zinkaoneka zopanda chiyembekezo. Koma munyengo yopanda chiyembekezoyo Abrahamu anakhulupilira m'chiyembekezo.

Posayang'ana zochitika zomwe zakungulirani, kaya nyengo yanu ndiyopanda chiyembekezo motani, mudziwe kuti Mulungu anakuitanani inu ku masomphenya a kholola ndipo adzakwaniritsidwa.

Muzikumana ndi nyengo yopanda chiyembekezon; tsimikizikani kuti kuti “chimene analonjeza, ndiothekera kuchichita”.

ANALI NDICHKHULUPIRIRO CHOLIMBA:

ndipo poyang'anira lonjezo la Mulungu sanagwedezeka cifukwa ca kusakhulupirira, koma analimbika m'cikhulupiriro, napatsa Mulungu ulemu. (Aroma 4:20)

Abrahamu anali ndi chikhulupiliro mwakuti anatha kumtamanda Mulungu chifukwa chokwaniritsa masomphenya ngakhale zinali zisanachitike. Anali wotsikimizika kuti Mulungu atha kuchita chirichonse chomwe anamlonjeza (Aroma 4:20).

Ukulu wamasomphenya omwe Mulungu wakuitanirani ndiwodabwitsa kwambiri. Ma bilioni atatu a anthu sanalandirebe Uthenga Wabwino. Amenewa ndi achikunja. Amenewa ndi cholowa chanu. Kupyolera mwa inu akuyenera kukadalitsika.

Koma musamagwedezeka pa lonjezano la Mulungu. Musamayang'ane kukula kwa ntchito mulinayo, koma muziyang'ana kukula kwa Mulungu. Mulungu walonjeza kholola lauzimu locholuka. Mukhale ngati Abrahamu amene...

Amene anakhulupira nayembekeza zosayembekezeka, kuti iye akakhale kholo la mitundu yambiri ya anthu, monga mwa conenedwaci, Mbeu yakoidzakhala yotere. (Aroma 4:18)

ANALI OLUNGAMA:

Chifukwa Abrahamu anakhulupilira Mulungu:

Cifukwa cace ici cinawerengedwa kwa iye cilungamo. (Aroma 4:22)

Monga mmene mwaphunzilira muphunziro lino, maziko antchito yanu pokolola chikuyenera kukhala chiyero.

ANALI OZICHEPETA:

Paulo amati Abrahamu anapereka ulemu kwa Mulungu (Aroma 4:20)

Abrahamu anadziwa kuti kukwaniritsidwa kwa masomphenya kumatheka kudzera mwa Mulungu yekha basi. Iye yekha akuyenera kulandira ulemu.

Mulungu wakupatsani masomphenya akulu mmunda wa kholola wa mafuko a padziko lonse. Koma kukwaniritsidwa kukhoza kutheka kudzera mwa Iye. Simungalandire ulemelero pa masomphenya kapena pa zotsatira za kholola. Ulemerero ukuyenera kupita kwa Mulungu chifukwa chokwaniritsa masomphenya.

ANALI WA MTENDERERE:

Mu Genesis 13 antchito a Loti ndi Abrahamu anakonda kukangana kwambiri chifukwa cha umwini wa madzi. Abrahamu anasankha kuthetsa vutolo mwamtendere.

Unthenga omwe unaperekedwa ndi angelo pa kubadwa kwa Yesu unali wa mtendere. Uthenga Wabwino omwe mukupititsa ku mafuko ndi uthenga wa mtendere pakuti mkudzera mwa Mulungu yekha momwe mtendere weni weni umabwera.

ANALI WAMACHAWI POCHITA CHIFUNIRO CHA MULUNGU:

Pamene Mulungu anamuyankhula Abrahamu kuti chizindikiro cha pangano pakati pa Mulungu ndi iye unali mdulidwe. Baibulo linalamba kuti pa tsiku lomwelo Mulungu anayakhula, Abrahamu anadula amuna onse a pabanja pake (Genesesi 17).

Nthawi ina kutsogolo Mulungu anakwaniritsa lonjezo lake kwa Abrahamu ndipo iye ndi mkazi wake, Sarai, anakhala ndi mwana wamamuna. Atangobadwa Isake, Mulungu anampatsa Abrahamu mayesero ovuta. Anamuza kuti akapereke nsembe mwana wake (Genesis 22).

Mwa Isake munali la mtsogolo la lonjezano la Mulungu. Anali cholowa chimene mbumba ya Abrahamu idzabwelere. Isake amayenera kubweretsa fuko la Israele lomwe mafuko amayenera kudalitsika nalo. Koma Mulungu anamuza kukapereka nsembe mwana wake.

Baibulo linalamba mu Gensesis 22:3 kuti Abrahamu atandira uthenga umenewu kuchoka kwa Mulungu, “anadzuka molawira” mamawa pomvera malangizo. Ngakhale chifuniro cha Mulungu chinali chovuta, Abrahamu sanazengereze. Pamene Mulungu wayankhula anachita kanthu mwachangu. Chifukwa chakumcera kwake, Mulungu anapereka nsembe ina ndipo moyo wa Isake unapulumuka.

Kugwira ntchito m’ munda wa kholola sikuti nthawi zonse kudzakhala kophweka koma pamene Mulungu wayankhula mukuyenera kumachitapo kanthu. Pamene mwapita chitsogolo mukumvera, Mulungu nthawi zonze adzayenda m’ malo mwanu.

Ndizosangalatsa kuzindikira kuti Abrahamu sanatenge kulankhula kwa Mulungu monga ngati. Koma iye anatenga uku kukhala kulambira. Ndi mulingo waukulu olambira omwe umaposa Isake, chomwe timakonda, kufika kwa Mulungu.

Mulungu wakupatsani masomphenya ndipo asintha moyo wanu. Koma sikuti masomphenyawo angakhale ofunika kwambiri kuposa Mulungu. Udindo wanu woyamba ndikukhala pa ubwenzi ndi Iye.

Mulungu anamuyesa Abrahamu pofuna kuona pomwe mtima wa Abraham unatsamira – Isake kapena Mulungu. Nthawi zomwe azikhala Mulungu amene ali poyambilira mmoyo wanu. Masomphenya sangalowe mmalo mwaopereka masomphenyawo.

ANKAYENDAYENDA CHIFUKWA CHA MULUNGU:

Abrahamu amakhala moyo wophweka omwe unkampangitsa kuti azitha kuyenda chifukwa cha Mulungu. Ankakwanitsa kusuntha mwachangu Mulungu akalamula (Genesis 12).

SANKAYANG’ANA PA MBUYO:

Abrahamu samkafunaso moyo wakale omwe anausiya kale, koma ankayang’ana ku zinthu zatsopano zomwe Mulungu anakachita:

koma wopanda cikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna iye. (Ahebri 11:6)

ANAYENDA MUCHIDZIWITSO CHA BVUMBULUTSO:

Abrahamu anachita pa bvumbulutso lochokera kwa Mulungu osati pa zam'maganizo a umunthu:

Ndipo Yehova adati, Kodi ndidzabisira Abrahamu cimene ndicita? Genesis 18:17

SANAYANG'ANA KUTHEKERA KWAKE KWA KUTHUPI:

Lonjezo la Mulungu ku mafuko linatumphuka ngakhale limaoneka lakufa ndi maso a kuthupi, Abrahamu analibe kuthekera kokwaniritsa malingaliro a Mulungu.

mwa icinso kudacokera kwa mmodzi, ndiye ngati wakufa, aunyinji ngati nyenyezi za m'mwamba, ndi ngati mcenga, uli m'mbali mwa nyanja, osawerengeka. (Ahebri 11:12)

ANAFUNAFUNA MULUNGU

Genesis 1 amanena mmene Abrahamu anamangira guwa ndipo anaitanira pa dzina la Mulungu.

ANKAGANIZIRA UDINDO WA ENA

Werengani nkhani ya Abrahamu ndi Loti mu Genesis 14. Ngati mukufuna kukhala mKhristu wa dziko lonse mukuyenera kuona kuti muli ndi udindo wothandiza ovutika omwe akuzungulirani.

ANALI WOPATSA (WOKOMA MTIMA)

Abrahamu analipira chakhumi pa zonse zomwe anali nazo:

Ayamikike Mulungu Wamkurukuru amene wapereka adani ako m'dzanja lako. Ndipo anampatsa iye limodzi la magawo khumi la zonse. (Genesis 14:20)

ANALI OKONZEKA KUKHALA KUDZIKO LACHILENDO:

Ndi cikhulupiriro anakhala mlendo ku dziko la lonjezano, losati lace, nakhalira m'mahema pamodzi ndi Isake ndi Yakobo, olova nyumba pamodzi ndi iye a lonjezano lomwelo; (Ahebri 11:9)

Anali wokonzeka kulemekeza chikhalidwe cha ena. Mwachitsanzo, anawerama pamanso pa anthu m'dzikolo monga mwa mwambo wawo.

Ndipo Abrahamu anawerama pamaso pa anthu a m'dzikomo. (Genesis 23:12)

ANABEREKA AMUNA OFANANA NAWO KUZIPEREKA:

Izi zikuwoneka m'moyo mwa mtumiki, Eliyazi (Genesis 24)

ANAPEREKA ULEMERORO KWA MULUNGU:

Mfumu ya Sodomu ndipo inati kwa Abram, Ndipatse ine anthu, nutenge cuma iwe wekha. Ndipo Abram anati kwa mfumu ya Sodomu, Dzanja langa ndamtukulira Yehova, Mulungu Wamkurukuru, mwini kumwamba ndi dziko lapansi, kuti sindidzatenga ngakhale thonje ngakhale cingwe ca nsapato, ngakhale kanthu kali konse kako, kuti unganene, Ndamlemeza Abram; koma cokhaci anadya anyamata, ndi gawo lao la anthu amene ananka pamodzi ndi ine, Aneri, Esikolo, ndi Mamre, iwo atenge gawo lao. (Genesis 14:21-24)

Nthawi zonse kumbukirani, ulemerero nthawi zonse ukuyenera kupita kwa Mulungu.

KUKWANIRITSIDWA KWA MASOMPHENYA

Abrahamu, munthu wa masomphenya auzimu...Anali munthu amene kudzera mwa iye mafuko onse a dziko lapansi amayenera kudalitsika. Ndipo masomphenyawa anakwaniritsidwa.

Mwa icinso kudacokera kwa mmodzi, ndiye ngati wakufa, aunyinji ngati nyenyezi za m'mwamba, ndi ngati mcenga, uli m'mbali mwa nyanja, osawerengeka. (Ahebri 11:12)

Pamene masomphenya ankaperekedwa kwa Abrahamu, kale lake linali losapindulitsa ndiponso tsopano lake linanso losapindulitsa. Koma sanavomereze kufa kwa thupi lake ndi chiberekero cha mkazi wake Sarai.

Mwina kale lanu linali losabereka kuuzimu ndiponso tsopano lanu silikubala zipatso. Koma tsopano mwalandira masomphenya a kholola.

Monga Abrahamu, muziyang'ana ndi maso a chikhulupiriro kutsogolo pozindikira kuti "Iye amene analonjeza ndi othechera kuchita izi".

MAYENSO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera lomwe mwaloweza.

2. Perekani mafotokozedwe awiri omwe akusonyeza kuti okhulupilira ndi cholowa cha Abrahamu:
Ndi _____

3. Ndife cholowa ku pangano la:

4. Ndife cholowa ku udindo wa:

5. Lembani zoyenerereza za uzimu za Abrahamu zomwe ndinamupangitsa iye kuti akwaniritse masomphenya okadalitsa mafuko adziko lonse.

<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>

(Mayankho amayenso aperekedwa ku chaputa chomaliza cha bukuli)

POPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. M'musimu mwalembedwa mwachidule zinthu zauzimu zomwe zinamuyenerereza Abrahamu kukhala mdalitso ku mafuko a dziko lapansi. Ngati mufukuna kukwaniritse masomphenya okadalitsa mafuko, mukuyenera kukhala ndi zoyenerereza zauzimu m'moyo mwanu. Muonenso choyenerereza chauzimu chirichonse. Fotokozani mulingo omwe umafikira mmoyo wanu wauzimu.

Choyenerereza

Pomwe ndili pa choyenerereza chimenechi m'moyo wanga

Kukopeka mtima kwatunthu

Kufesa mu zinthu zauzimu

Kumvera

Kukonzeka kuima panokha

Masomphenya auzimu

Kumudziwa Mulungu ngati bwenzi

Chiyembekezo

Chikhulupiriro _____

Kulungama _____

Kudzichepetsa _____

Wamtendere _____

Okonzeka kuchita chifuniro cha Mulungu _____

Kuyendayenda chifukwa cha Mulungu _____

Osayang'ana pa mbuyo _____

Kuyenda m'mabvumbulutso a chidziwitso _____

Osayang'ana kuthekera kwa kunthupi _____

Kufunafuna Mulungu _____

Kuzindikira udindo wa ena _____

Wachifundo _____

Kubereka amuna ozipereka mofanana _____

Kupereka ulemerero kwa Mulungu _____

Kufuna kukhala mudziko la chilendo _____

2. Mutatha kuchita kafukufuku wa moyo wanu pa zokuyenerezani; mungatani pa zinthu zomwe zalembedwa m'musimu kuti mukonze magawo amene mukupelewera:

- Kuwerenga Baibulo tsiku ndi tsiku:

- Moyo wanga wapemphero tsiku ndi tsiku:

- Nyumba ndi banja langa:

- Mpingo wanga:

- Malingaliro anga anzamtsogolo:
- Kunkhudzidwa kwanga pa masomphenya a kholola:
- Zachuma zanga:

CHAPUTALA 11

KUKWANIRITSIDWA KWA MASOMPHENYA

ZOLINGA

Muyenera kudziwa zinthu izi pamapeto pa phunziro ili.

- Kupeza mtundu wa nthu amene Mulungu amayitana kukhala okolora.
- Kugwiritsa ntchito malaonjezano a Mulungu pa kholola lauzimu.
- Kukwaniritsa masomphenya mmoyo wanu.

VESI YOTSOGOLERA

Koma tisaleme pakucita zabwino pakuti pa nyengo yace tidzatuta tikapanda kufooka (Agalatiya 6:9).

MAU OTSOGOLERA

Pamene munayamba phunziro limeneli, munayamba ulendo umene ukutengeni kuchokera ku masomphenya kufika ku kukwaniritsidwa. M'machaputala apitawa, mwaona malingaliro kapena zolinga za Mulungu kudziko lapansi ndiponso mwaona zinthu zolepheretsa kholola lauzimu komanso ndondomeko, njira ndi zipangizo za kukolola kwaphindu. Ndipo muchaputala chimenechi, tiona zakukwaritsidwa kwa masomphenya pamene inu mukhale gawo limodzi la anthu okwaniritsa masomphenyawa.

KODI MULUNGU AMAGWIRITSA NTCHITO NDANI?

Kodi Mulungu amagwiritsa ntchito ndani pokwaniritsa masomphenya a kholola? Kodi ndi anthu anji amene Mulungu amawayita kuti akafalitse Uthenga Wabwino? Werengani Mariko 16. Ndime imeneyi ili ndi mayankho amafunso afunsidwawa, koma mu ndime mwawerengayi tikupeza ophunzira a Yesu akupita kumanda kuti akadzodze mafuta thupi la Yesu. Koma iwo atafika kumanda, anapeza...

Ndipo pamene analowa m'manda, anaona mnyamata alikukhala ku mba li va ku dzanja lamanja, wobvala mwinjiro woyera; ndipo iwo anadabwa. Ndipo iye

ananena nao, Musadabwe: mulikufuna Yesu Mnazarene amene anapacikidwa: anauka; sali pano; taonani, mbuto m'mene anaikamo Iye! (Marko 16:5-6)

Azimayi anathamanga kukauza ophunzira a Yesu zankhani yabwino, koma angakhale kuti Yesu anamuonekera Maliya Magadala, ophunzira a Yesu sanakhulupilire kuti wauka (Maliko 16:11) koma patapita kanthawi, Yesu anaonekera kwa ophunzira awiri, ndipo pamene iwo anauza ena, anthu sanakhulupilirebe (Marko 16:12- 13).

Yesu aonekera kwa ophunzira ake....

Ndipo citatha ico anaonekera kwa khumi ndi mmodzi iwo okha, alikuseama pacakudya; ndipo anawadzudza cifukwa ca kusabvomereza kwao ndi kuuma mtima, popeza sanabvomereza iwo amene adamuona, atauka Iye. (Marko 16:14)

Ndipo anati kwa iwo:

Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. (Marko 16:15)

Mwinatu Yesu analawitsa kuwauza mau awa, chifukwa awa anali anthu omwe aja amene anapita kukadzodza thupi la Yesu mafuta mmalo moti akondwelere kuti Iye wauka, anali anthu amene anamukana ndi kumuthawa pamene zinthu zimaoneka kuti zavuta komanso anali anthu amene anabisala chifukwa cha mantha.

Yesu anakhala ndi anthu amenewa kwa zaka zitatatu akuwakonzekeretsa ophunzira ake za imfa ndi kuuka kwake, koma zinthu zitavuta, iwo samakhulupilirabe maumboni akuti Yesu wauka. Koma mwa kamphindi kochepe, Yesu anadzudza chifukwa cha kusakhulupilira kwao kenako anayika mwa iwo masomphenya a kholola lauzimu la dziko lonse lapansi.

Ndi chifukwa chiyani Yesu akuyika tsogolo la kulalika Uthenga Wabwino mmanja mwa ophunzira ake?

Yesu anapanga izi chifukwa amawaona mwa mtundu wina, kusiyana ndi mmene analili mbuyomo. Iye samaonanso mmene anachitira mbuyomo, amawaona mmene adzachitire akadzalandira mphamvu ya Mzimu Woyera.

ANTHU AMENE MULUNGU AMAGWIRITSA NTCHITO

Tiona anthu amene Mulungu anawagwiritsa nchito pofuna kukwanilitsa zolonga zake.

YAKOBO:

Mulungu anasankha Yakobo, munthu amene anafunitsitsa kukhala ndi mdalitso wa mwana woyamba mpaka kufika mlingo wongoba mdalitso wa mwana woyamba kwa m'bale wake Esau amene anepereka mdalitso wake chifukwa cha njala, angakhale izi zinali chomwechi, Mulungu anagwiritsabe ntchito Yakobo pofuna kubadwitsa fuko la Israyeli.

ABRAHAM:

Abrahamu amayenera kukhala tate wa mafuko onse adziko lapansi. Pamene iye analandira bvumbulutso kuchokera kwa Mulungu, iye sanakhulupilira (Genesis 17:1-3) patadutsa nthawi, Abrahamu ananama kuti Sara simkazi wake. Anachita izi chifukwa chakuopa kuti akhoza kuphedwa. Koma posatengela zimenezi, Abrahamu anatchedwabe “mnzake wa Mulungu” ndipo anakhalabe tate wa mafuko a dziko lonse lapansi.

MOSE:

Chifukwa cha kusamvera, Mose analemphera kukalowa mudziko la malonjezano, izi zinali chomwechi angakhale kuti anapulumutsa ana a Israyeli ndi kuwatsogolera mu chipulu kufikira ku dziko la malonjezano.

DAVIDE:

Iye analanda mkazi wa mwini ndikupha mwamuna wa mkaziyu pofuna kubisa tchimo, komabe anatchedwa munthu wokonedwa wa Mulungu ndipo Mulungu anampatsa ufumu wake.

GIDIYONI:

Pamene Mulungu amamuyitana Gidiyoni kuti akapulumutse ana a Israyeli, Iye amakolola tirigu mobisala chifukwa cha mantha adani. (Oweruza)

ANTHU WAMBA

Mulungu amagwiritsa ntchito anthu wamba kuti akakwaniritse chifuniro chake. Pamene Yesu anasandulitsa madzi kukhala vinyo, Iye anapempha anthu wamba kuti adzadze mbiya ndi madzi. Ndipo ichi chinali chozizwa choyamba chimene Yesu anachita mu utumiki wake. Pamene anachulutsa mkate ndi nsomba, zinaperekedwa kwa anthu wamba. Pamene Yesu amafuna kuchita chimodzi mwa zozizwa zazikulu mu utumiki wake, chimene chili chiukitso cha Lazaro, Iye anagwiritsa nthcito anthu wamba kuti akachotse mwala wolowera pa manda a Lazaro. Kodi Mulungu amene anaukitsa Lazaro analibe mphamvu zochotsera chimwali chapamanda a Lazaro?

Mulungu mphamvu anali nazo, koma Mulungu wakhala akugwiritsa ntchito anthu kuti akwaniritse malingaliro ake. Mulungu amaitana anthu wamba ndicholinga chowapanga anthu apadeleradera. Amawasintha anthu kukhala wongoyang'anira ndi kukhala otengapo mbali pa malingaliro ake.

- Nonse anthu wamba amene mumaganiza kuti Mulungu sangakugwiritseni ntchito.
- Nonse anthu wamba amene mumaganiza kuti simungakhale gawo limodzi la chozizwa.
- onse amene anamkana Yesu ndikukanika kukwaniritisa zofuna zake.

Mulungu sakutanga'anira mukuchitira pano kapena mmene munachitira mbuyo. Ndipo iye samakuonani mmene mukuzidzionera pakadali pano. Iye akukuonani mmene chimene mukhare pamene mwabvomeleza kuchita kholora la mmunda wadziko lapansi. Iye akuona chimene mukhare mukalandira mphamvu ya Mzimu Woyera.

Mulungu sakudalira chilichonse chimene mulinacho, kaya ndi maphunziro, luso lanu kapena mlingo wauzimu wanu. Iye akudalira chimene akudziwa kuti inuyo mukhoza kukhala ngati mupereka moyo wanu ku zolinga zake zauzimu.

Uthenga sunafalikire mumpingo woyambilira chifukwa chakulalika mwa mphamvu, koma chifukwa cha anthu amene anazindikira kulephera kwao nayanga'nira pa Mulungu posatengera zolephera zaozo. Iwo anazindikira kuti pamene anali ofooka kuthupi, moyo wauzimu unali wamphamvu chifukwa Mulungu analonjeza.

Mumayesa tsopano Uno kuti tirikuwiringula kwa, inu. Tilankhula pamaso pa Mulungu mwa Kristu. Koma zonse, okondedwa, ziri za kumangirira

kwanu. (2 Akorinto 12:19)

KHOLOLA LOCHURUKA

Kwa amene amvetsetsa masomphenya ndi nukwaniritsa ntchito ya Mulungu, pali malonjezano a kholola lochuruka:

Pakuti padzakhala mbeu ya mtendere; mpesa udzapatsa zipatso zace, ndi nthaka idzapatsa zobala zace, ndi miyamba Idzapatsa mame ao; ndipo ndidzalandiritsa otsala a anthu awa izi zonse, cikhale colowa cao. (Zekariya 8:12)

Adzasandulitsa chipululu nakhala nthaka ya chonde.

Asanduliza cipululu cikhale thawale, Ndi dziko louma likhale akasupe a madzi. Ndi apo akhalitsa anjala, Kuti amangeko mudzi wokhalamo anthu; Nafese m'minda, naoke mipesa, Ndiyo yakubala zipatso zolemeza. (Masalmo 107:35-37)

Mulungu adzapereka kholola angakhale pa malo opanda chonde

M'dzikomo mudzakhala zinthu zocuruka pamwamba pa mapiri; Zipatso zace zidzati waa, ngati za ku Lebano: Ndipo iwo a m'mudzi adzaphuka ngati msipu wapansi. (Masalmo 72:16)

Angakhale msinkhu sicholepheretsa ku malingaliro a Mulungu.

Adzabala zipatso angakhale atakalamba (Salimo 92:14)

Mukhoza kudutsa m'mikwingwirima kuti mubadwitse masomphenya, koma...

Akubzala ndi misozi adzatuta ndi kupfuula mokondwera. Iye amene ayendayenda nalira, ponyamula mbeu yakufesa; Adzabweranso ndithu ndi kupfuula mokondwera, alikunyamula mitolo yace. (Masalmo 126:5-6)

Simungamvetse za kuchuluka kwa kholola la kuchimaliziro kwa dziko:

Ulemerero wotsiriza wa nyumba iyi udzaposi woyambawo, ati Yehova wa makamu; ndipo m'malo muno ndidzapatsa mtendere, ati Yehova wa makamu. (Hagai 2:9)

Mulungu akulankhula za kholola limene lilibe malire.

Taonani akudza masiku, ati Yehova, akuti wolima adzapezana ndi wodula, ndi woponda mphesa adzapezana ndi wofesa, ndi mapiri adzakhetsa vinyo watsopano, ndi zitunda zonse zidzasungunuka. (Amosi 9:13)

Simungamalize kukolola mpaka kholola lina litafikanso. Nanga nchifukwa chiani anchito akufunika ambiri? Wolima m'munda akuthamanga kuposa okolola kotere kuti khololola lili ndi inu.

- Mukakamire malonjezano a kholola lochuluka

-mukakamire anthu osakhulupilira Mulungu ngati cholowa chanu

-minda ydziko lanu ili pafupi nanu. Ingotsekulani maso anu ndikupenya

KHOLORA LOMALIZA

Nthawi ikudza ya kholola lomaliza pamene Mulungu adzalamula angelo ake:

Ndipo mngelo wina anaturuka m'Kacisi, wopfuula ndi mau akuru kwa iye wakukhala pamtambo, Tumiza zenga lako ndi kumweta, pakuti yafika nthawi yakumweta; popeza dzinthu za dziko zacetsa. (Cibvumbulutso 14:15)

Ndipo anthu onse adziko lapansi adzasonkhana pamodzi. Kuchokera mayiko aku Africa, kumpoto ndikumwera kwa Amerika, ku Ulaya ndi zilumba zonse. Kholola lidzafika pa mpando wa ulamuliro wa Mulungu. Amayi ndi abambo amene anakwaniritsa masomphenya, komanso amene masomphenya linali gawo limodzi lofunika kwambiri m'moyo wao, anthu amene anamwalira akukhulupilirabe malonjezano a masomphenya; ndipo anabwera nao makoko akholola la dziko lapansi:

Zitatha izi ndinapenya, taonani, khamu lalikuru, loti palibe munthu anakhoza kuliwerega, ocokera mwa mtundu uli wonse, ndi mafuko ndi anthu ndi manenedwe, akuimilira ku mpando wacifumu ndi pamaso pa Mwanawankhosa, atabvala zobvala zoyera, ndi makhwatha a kanjedza m'manja mwao; ndipo apfuula

ndi mau akuru, nanena, Cipulumutso kwa Mulungu wathu wakukhala pa mpando wacifumu, ndi kwa Mwanawankhosa.

Ndipo angelo onse anaimirira pozinga mpando wacifumu, ndi akulu, ndi zamoyozo zinai; ndipo anagwa nkhope yao pansu ku mpando wacifumu, nalambila Mulungu, ndi kunena, Amen: Thamo ndi ulemerero, ndi nzeru, ndi ciyamiko, ndi ulemu, ndi cilimbiko, ndi mphamvu zikhale kwa Mulungu wathu kufikira nthawi za nthawi. (Cibvumbulutso 7:9-12)

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera yapamtima.

2. Lembani ndime ziwiri za m’Baibulo zimene zimalonjeza kholola lochuluka.

3. Tchulani anthu anayi amene atchulidwa muchaputala ichi amene agwiritsidwa ntchito ndi Mulungu posatengera zolephera zao.

4. Kodi ndi vesi iti imene imakamba za kholora lomaliza limene adzapange ndi angero.

MAYANKHO AMAFUNSO-ODZIYESA NOKHA

CHAPUTALA 1:

1. Papanda masomphenya anthu amaonongeka (Miyambo 29:18)
2. Masomphenya auzimu ndikuona kuposa zinthu zakuthupi. Masomphenya awa amatanthauza kumvetsetsa cholinga cha Mulungu komanso kuzindikira mbali yanu yoti muchite. Ndipo amaonetsera chenicheni chimene Mulungua akufuna kuti muchite pa moyo wanu wachikhristu watsiku ndi tsiku.
3. 2,3,1,4,6,5.
4. 3,1,4,2.

CHAPUTALA 2:

1. Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta. (Yohane 4:35).
2. Tikakamba za zitsanzo zakuthupi zofanana ndi choonadi chauzimu, zimatanthauza kuti Mulungu amagwiritsa ntchito zinthu za kuthupi pofuna kuonetsera choonadi chauzimu.
3. Chitsanzo ndi chakholora.
4. Mundau ndi dziko lapansi (Mateyu 13:38)
5. Mwina mkutheka munapereka zifukwa izi. Chitsanzo cha kholora ndi chimene ophunzira akanatha kumvetsa pa zifukwa izi:
 - Chuma cha Israyeli chinali chodalira ulimi.
 - Zikondwelero za mbiri zimakhudzana ndi kholora.
 - Kholora limakhara likuchita nthawi zonse chaka chonse.
 - Panali mfundo zakuthupi zofesera ndi kututa zimene zimagwirizana ndi kholora lauzimu.
 - Ophunzira a Yesu anazindikira zakufunika kochita machawi atamva chitsanzo chakholora lakuthupi.
6. Yohane 4:35
 - Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai,
 - ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu,
 - Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda,
 - kuti mwayera kale kufikira kumweta.

CHAPUTALA 3:

1. Maso ake ayanga'anira amitundu. (Masalimo 66:7)
2. Anthu okwana miyanda miyanda (3Billion)
3. Zilankuro zokwana 1000.
4. Kuti tikaone dziko lapansi ngati munda wakholora lauzimu umene ukufunika antchito.
5. Tchimo.
6. a.F b.F c.T
7. Nkhristu wa dziko lonse ndi amene tsiku ndi tsiku amakhara akulingalira zopititsa patsoyolo uthenga Wabwino kwa anthu amene sanafikilidwe ndi uthenga Wabwino.

CHAPUTALA 4:

1. Anatzindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)
2. a.F b.T c. T d.T
3. Mayanko anu amayenera kukhara ndi mfundo izi komanso ndi vesi imodzi monga awa:
Anatzindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10).

Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (2 Petro 3:9)

CHAPUTALA 5:

1. Musanyengedwe; Mulungu sanyozeka; pakuti cimene munthu acifesa, cimenenso adzaciduta. Pakuti wakufesera kwa thupi la iye yekha, cocokera m'thupi adzatuta cibvundi; koma wakufesera kwa Mzimu, cocokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha. (Agalatiya 6:7-8)
2. a.T b. F c. F d.F e.T f.T g.T
3. Makangano, mphulupulu, Kulimbana, Thupi.

4. Anthu opulumuka ndikukhara moyo opulumuka.
5. Yesaya 16:10 or Joel 1:10-12,16.
6. Yoweri 1:13-14; 2:12-13.
7. Onani mwachidule mitu ikuluikulu ya ndime zili munsimu

Kusamvera Mau a Mulungu.	Kuyanga'nira Nyengo Zathu.
Kuiwala Mulungu.	Kupanga Zinthu Opanda Kulunjika.
Kufesa Mosayenera.	Tizilombo Ndi Matenda.
Kusakhudzika.	Kukolora Mosayenera.
Kuyesa Mwatokha.	Nthaka Yosalimidwa.
Zobara Zotembeleredwa.	Maziko Osalungama.
	Antchito achepa.

CHAPUTALA 6

1. onse amene amafesa ndimisonzi amatuta ndichimwemwe
 Akubzala ndi misozi adzatuta ndi kupfuula mokondwera. Iye amene ayendayenda nalira, ponyamula mbeu yakufesa; Adzabweranso ndithu ndi kupfuula mokondwera, alikunyamula mitolo yace. (Masalmo 126:5-6)
2. Ndongomeko ndi mfundo, njira kapena machitachita amene amatsatidwa pofuna kufikira cholinga choika.
3. Ngati mwamphonya ina mwandondomeko, onaninso mutu waung'ono wa chaputala chonse.

-Mbeu iliyonse ndi nkuthekera kobeleka.

-Kufesa mkofunika kuti muzakolore.

-Umakolora zomwe wafesa.

-Mukuyenera kufesa posayang'anira nyengo.

-Umakolora mogwirizana ndi mulingo omwe unabzala.

-Utha kufesa pomwe sukolora komaso utha kukolola pomwe sunafese.

-Uzakolola kholora ngati ndiwe okhulupirika.

-Mbeu kuti ikathe kubala, ikuyenera kuti ife.

CHAPUTALA 7

1. Pakuti monga dziko liphukitsa mphundu zace, ndi monga munda umeretsa zobzalamo, momwemo Ambuye Yehova adzaphukitsa cilungamo ndi matamando pamaso pa amitundu onse. (Yesaya 61:11)
2. Mbeu imakula chifukwa cha nyengo zina zakudziko.
3. Ngati mwamphonyana ndi zinthu zomwe zimapangitsa kukula, onaninso mutu waung'ono wa chaputala chonse: moyo, donthi loyenera, kuwala, mpweya, danga, mmene mizu imayendera, kupumula, kulumikizidwa ku mpesa, kudulirira, nyengo.

CHAPUTALA 8

1. Macitidwe 1:8 Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko.
2. 2 Timoteo 2:2
3. Mphamvu.
4. Zindikirani kuti ndizalero, dziwa gwero, bvomerezani ulamuliro panokha ndi mpigo mu mwanu.

CHAPUTALA 9:

1. Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzicepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wo pepuka. (Mateyu 11:28-30)
2. Tchimo, kuzikonda, munthu
3. Lopepuka, wofewa, mpumulo.
4. Idzani kwa Iye, senzani goli lake, phunzirani kwa Iye.
5. Muzazindikira liwu la Mulungu; mudzakhara opambana pokwanilitsa masomphenya anu; Mulungu azakutsogolerani inu mosalekeza; azakhala thandinzo lanu; muzakhala opindula.

CHAPUTALA 10:

1. Agalatiya 3:29 Koma ngati muli a Kristu, muli mbeu ya Abrahamu, 7 nyumba

- monga mwa Lonjezano.
2. Agalatiya 3:10 ndi Agalatiya 3:29.
 3. Chipulumutso.
 4. Kudalitsa mafuko adziko lonse.
 5. Kukopeka kwaphuphu. Odzala ndi chiyembekezo Kufesa
muzithu za Uzimu. Olimba muchikhulupiriro

Omvera maitanidwe	Olungama
Kufuna kuima pawekha	Ozichepetsa
Munthu wasomphenya	Munthu wa mtendere
Kudziwa Mulungu ngati bwezni	Kuchita chifuniro cha Mulungu
Kuyendayenda chifukwa cha Mulungu	Osayang'ana m'mbuyo
Kuyenda mubvumbulutso lachidziwitso	Kufuna Mulungu
Kukhala ndi udindo paena	Wopatsa
Kubala amuna odzipereka	Kupereka ulemerero kwa Mulungu
Sanayang'anire kuthekera kwake kwa kuthupi	
Okonzeka kukhala mdziko lachilendo	

CHAPUTALA 11:

1. Agalatiya 6:9 Koma tisaleme pakucita zabwino pakuti pa nyengo yace tidzatuta tikapanda kufoka.
2. Mukhonza kugwiritsanso ntchito machaputala ndi ma vesi: Masalimo 72:16; Masalimo 92:4; Masalimo 107:33-37; Masalimo 126:5-6; Amosi 9:13; Hagayi 2:19; Zakaliya 8:12.
3. Yakobo, Abrahamu, Davide, Gidioni
4. Chibvumbulutso 14:15.

MATHERO

